


M'BADWO WA MPINGO

WA PERGAMO

 Chabwino. Tsopano, momwe ine ndikuganizira, izo zingakhale bwino kuzitulutsa panja. Chabwino.

² Ndife okondwa kwambiri kuti tiri muno kenanso usikuuno mu msonkhano wa Ambuye. Ndipo usiku wathawu ine ndithudi ndinamverera kuti Zakachikwi zinali zitabwera. Ndipo chotero tsopano ife tiri nawo ena, ine ndikukhulupirira mafunso ena apa, ndipo ine ndiwaika iwo mthumba mwanga kuti . . . Ine—ine ndikulingalira ili ndi pemphero . . . kuti apempheredwe. Ndipo ndife . . . Ndipo ine ndiyesetsa kuti ndiyankhe mopambana mmene ine—mmene ndingathere.

³ Kutu, ngati inu mungamuuze Doc ngati iye “angatembenuze icho,” icho . . . chikunyezimirira pansu pa ine, kuchitira kuti, ndisakhale ngati ndikuwonetsedwa. Inu mukudziwa, ine—sindine mmodzi wa alaliki owonetsedwa awa. Chotero zingakhale zabwino kukhala wopanda icho, ine ndikuganiza. Pomaliza . . .

⁴ Ine ndinachipempha icho, Doc. Ine ndikulapa, ine—ine ndikulapa, inu mukuona. Oh, oh, kodi iwe unatani . . . ? Iwe uyenera ukasinthire pamwamba apo ndi kukachisintho icho? [M'bale Branham akuyankhulana ndi m'bale wake, Doc—Mkonzi]. Oh, chabwino, ingochisiya icho chokha. Eya. Chabwino, ingochisiya icho chokha. Oh, ayi! Tsopano, usachigwetse pansu icho. Eya. Tsopano ine ndimakonda zimenezo mwabwinoko. Nthawizina . . . Ndipo ine sindimakonda kuwala kuti kuzingowalira pa nkhope pako, inu mukudziwa. Ndipo—ndipo iko kumawalira pansu apa pomwe ine ndimatha kuwona bwino. Ine ndikukuthokozani inu, bwana. Iye alipira zimenezo.

⁵ Inu mukudziwa, inu simungamalazitse pa mibadwo ya mpingo iyi. Ndipo lero pamene ine ndimawerenga pa uwu, ine ndinanena kwa mkazi wanga, ine ndinati, “Oh, mai! Ine—ine ndiri ndi zolembe zokwanira kulalikirira maualaliki fifite kuchokera mu umodzi uwu.” Mukuona? Ndipo iwo basi . . . palibe njira yochitira izo koma kungomenya mfundo zikulu zikuluzo, ndipo mwinamwake pamene tidzalembe bukhu ndiye ife tidzayesa kudzaikamo zochulukana mmenemo.

⁶ Ine sindinakuwoneni inu pano, m'bale. Muli bwanji, M'bale West? Ine ndinangomva nkhanu ina yabwino, kuti womaliza m'banja la M'bale Daulton wabwera, mnyamata winayo . . . mtsikana winayo. Ndiwo teni, sichoncho? Naini.

Inu mukukumbukira kuti zimenezo zinali pansi pa utumiki watsopano pamene Ambuye anamuwuzwa iye kumeneko kuti a...banja lake likanadzapulumsidwa. Ine ndakhala ndikuwapempherera iwo, nditaima pamenepo osadziwa zoti ndiyankhule, Mzimu Woyera unati, “Ine ndikukupatsa iwe banja lako.” Mukuona? Uh-huh. Ndipo ndi zimenezo, mmodzi aliyense wa iwo. Mukuona momwe Ambuye amachitira? Mwaona, mawu Ake ndi angwiwo, iwo nkomwe, samalephera nkomwe. Chabwino, ife sitikufuna kuti tilowe mbali ya machiritso Auzimu, ife tikuyesetsa kukhala motalika...gawo ili, mbali ya uneneri.

⁷ Tsopano, usikuuno ine ndiyesetsa kuti ndingoyankhula, ndipo ngati ine ndingathe, ndipo ife tidzafika ku mbali ya za mbiriyakale ya m’badwo waukulu wa mpingo uwu, wachiwiri...kapena m’badwo wa mpingo wachitatu umene ife tirimo usikuuno. Kodi mukusangalala nazo? Izo ndi zodabwitsa basi. Ine ndikungogoniza kuti ndizodabwitsa momwe Ambuye Yesu watidalitsira ife ndi kutipatsa ife zinthu izi, ndipo ife tikuyamikira izo ndi mtima wathu wonse, kutidziwitsa ife nthawi isanakwane zimene ziti zidzachitike mtsogolomo. Iye amadziwa mathero kuyambira pachiyambi, ndipo chotero ndife okondwa kwambiri chifukwa cha izi. Chotero ife tikudalira kuti Ambuye atidalitsa ife.

⁸ Ndipo kodi inu munazindikira, usiku wathawu, Mzimu Woyera unatipatsa ife (utatha msonkhano) mauthenga atatu ndi miyoyo itatu. Ndendende basi. Ndipo pamene Mzimu unali kuyankhula, ndiye zinadzabwerera pa kutanthauzira kotsiriza, kudzabwereza, kudzati, “Chimene Mzimu anena kwa mipingo...” Oh, “Iye amene ali ndi khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo.” Basi... Ndipo Mzimu ukuyankhula kudzera mu mphatso za mpingo. Oh, mulole mpingo ugwiritse zimenezo molemekeza tsopano, mwaona, mungosunga izo molemekeza. Musamale; Satana adzabwera kudzakutsatirani, kudzayesa kukuthamangitsirani inu kumapeto akuya pa izo. Mudzakhale otsimikiza kuti ndi Mzimu Woyera nthawi iliyonse. Ndipo ngati uli Mzimu Woyera, Iye adzayankhula mwachindunji kwa chinachake chomwe chikuchitika. Izo ndi za kumangiriza mpingo. Mukuona? Ndiyeno ngati inu muzilemekeza iwo, Mulungu ndiye adzakupatsani inu zochuluka. Mwaona, ingopitirizani kumawonjezera ndi kumawonjezera zochuluka. Ndipo monga...

⁹ Tsopano, winawake wakhala akuitana ndi kufunsa... anthu amayimba lero ndi kumafunsa kuti misonkhano ya machiritso idzakhala liti. Tsopano, misonkhano iyi ikangotha, Lamlungu likudzali madzulo, ine ndikuchokapo kwa masiku angapo, ndikakhale ngati ndikapumitsa pa mmero pang’ono pokha, ndipo Lamlungu likubwerali, Ambuye akalola, ife

tidzakhala ndi msonkhano wamachiritso, Lamlungu likubwerali mmawa. Ilo lidzakhala a . . . sindikudziwa basi kuti lidzakhala tsiku lanji limenelo, koma lidzakhala sabata kuchokera . . . Pa 18, Lamlungu mmawa- . . . Kodi ziri bwino zimenezo, M'bale Neville? Uhm? [M'bale Neville akuyankha, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Lamlungu mmawa, pa 18, kudzapempherera odwala.

¹⁰ Ndipo mu izi, m'busa wathu pano, ine sindinapeze mwayi wonena zambiri za iye, koma ine ndikufuna inu nonse, mudzayese kukumana ndi abusa athu. Iye ndithudi ndi—m'bale weniweni mwa Khristu. Ndife okondwa kukhala ndi m'bale ameneyo . . . anakulira mu Methodisti ndi chiyero. Ndipo ife tonse tikumudziwa Orman Neville, aliyense kuzungulira kuno amamudziwa. Palibe amene angaike chala pa moyo wake. Ine ndiku . . . Iye samakonda kuti ine ndizinena zimenezo, komabe ine ndibwino kuti ndimupitse iye kaduwa kakang'ono tsopano, kuposa nkhatu yonse iye atapita. Mukuona? Ndipo nthawi yake ndi inoyo.

¹¹ Usiku wina ine ndimatuluka mtchalitchi ndipo wina anati, "Oh, M'bale Branham, ine ndithudi ndinayamikira ulaliki umenewo."

Ndipo ine ndinati, "Zikomo inu."

¹² Ndipo chotero winawake ataimirira pakhomo, (zakhala ziri zaka zambiri zapitazo, cha kuno ku kachisi) mtumiki, anati, "Chabwino, Mulungu adalitsike, ine sindimafuna aliyense azindiuza ine zimenezo." Mukuona? Anati, "Ine ndimafuna ulemelero wonse uzipita kwa Mulungu."

Ine ndinati, "Chabwino, izo zimatero." Mukuona? Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ine ndimazikonda zimenezo, inemwini." Ine ndinati, "Ine ndimazikonda kwenikweni zimenezo." Ndipo ine ndinati, "Ine ndimayenera kukhala woona."

Ndipo iye anati, iye anati, "Chabwino, ine sindimakonda kuti anthu azinena zimenezo zokhudza ine, azidalitsa Mulungu!"

Ine ndinati, "Pali kusiyana kumodzi kokha pakati pa ine ndi inu: Ine ndimanena zowona zokhudza izo, ndipo inu simutero ayi."

¹³ Aliyense amakonda . . . Ngati inu mumutenga mwana wamng'ono, mukamubwekerera iye pang'ono, iye amakachita ntchito yabwinoko. Mukuona? Uko nkulondola. Mukuona? Ndipo Mulungu, nthawizonse, Iye amakonda kuwauza ana Ake pamene iye akuchita bwino. Inu mumakonda kuwauza iwo pamene iwo akulakwitsa, ndiye bwanji osawauza iwo pamene iwo akuchita bwino? Mukuona?

¹⁴ Chotero ndithudi ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha M'bale Neville pokhala m'busa wa gulu lino pano pa kachisi. Ndipo kumuwona bambo ameneyo, wochokera ku Methodisti,

wochedwa kuti . . . Bwanji, basi ngati kuti akufuna azidya mu khola lolakwika. Chotero . . . koma kudzapeza kudzera mu—mu Mzimu Woyera waukulu, ndipo tsopano akubwera mu mphatso zimenezo; ndi momwe mosajejema Mzimu Woyera ukumugwiritsira iye ntchito pamene sakugwiritsa ntchito malingaliro ake omwe. Kumawona kutanthauzira ndi nthetemya yofanana, ndi kukwera ndi kutsika mofanana, monga manauni ndi ma puronauni, ndi zina zotero, ndi kumayankha izo mobwezeranso.

¹⁵ Ndipo m'bale wamng'ono uyu, ine sindikuganiza kuti ali . . . Junior Jackson. Chabwino, ine ndikhala chete, Junie. Ine ndimamuthokoza Mulungu chifukwa cha Junie Jackson, m'baleyu ndithudi ali ndi mphatso yayikulu yochokera kwa Ambuye.

¹⁶ Ndipo basi nthawizonse amakhala wodzichepetsa. Tsopano, aliyense mu mpingo ali ndi chinachake choti azichita; koma musamayesere konse kuikokera iyo kumbali kwa chinachakenso, muziilola iyo izilumikizana ndi mpingo wonse. Ndi ya Mulungu, zinthu zonse. Mukuona? Mukuona? Si aliyense amene amafuna kuti aziyankhula ndi malirime, aliyense kutanthauzira.

¹⁷ Muziyesetsa kumachita chinachake chabwino ndi kumangokhalabe wabwino; osamakhala ndi njiru, osamakhala ndi mangawa, musamalole kuipidwa kulikonse. Ziribe kanthu kuti munthuyo ndi woipa chotani komanso amakunenerani zoipa bwanji, musamaganizire konse zoyipa mumtima mwanu motsutsana ndi iwo; chifukwa pomwepo mdierেকেzi adzalowa mkati mmenemo, adzagwira ntchito chinachake pamenepo. Muzingozisunga izo zonse zitakutiridwa ndi chikondi chaumulungu, kuvomereza, ndi kumakonda, ndi kumawachitira zabwino iwo amene amakuchitirani inu zoipa. “Ngati inu muzingochitira zabwino iwo okha amene amakuchitirani inu zabwino, bwanji,” Yesu anati, “kodi amisonkho nawonso samatero?” Mukuona? Ochimwa, aliyense akhoza kukhala wabwino kwa iwo omwe ndi abwino kwa iwo. Koma muzikhala abwino kwa iwo omwe sali abwino kwa inu, muziwachitira chinachake iwo omwe sangakuchitireni inu kanthu. Muzimulankhulira mawu abwino munthu amene angakunenereni inu choipa, ndipo mukamatero mudzachotsa kuipidwa konse mumtima mwanu; ndipo nthawizonse muzikhala mu chikondi ndi aliyense pamenepo, bola ngati mukungokhala mu chikondi.

¹⁸ Tsopano inu mukuti, “Chabwino, iwo anachita . . .” Sindife woweruza, Mulungu ndiye Woweruza. Ndipo inu simungafune kuti munthu wosaukayo adzatayidwe, sichoncho inu? Ndithudi ayi, ziribe kanthu kuti iwowo ndi ndani. Inu simungafune zimenezo, chotero muziyesetsa kukhala achifundo kwa iwo. “Ndipo chikondi chimabisa machimo awunyinji.” Uh-huh.

Inde, bwana. Chikondi, chabwino chimenecho, Chachikhristu, Chikondi chaumulungu.

¹⁹ Ngati munthu abwera ndi kudzakutchani inu “woyera-wodzigudubuza” ndi mitundu yonse ya maina, tsopano—tsopano osati kungochichita icho mwasesewero, mwaona, ngati inu simungathe kuchita monga choncho, ingochokanipo. Koma mu mtima mwanu, inu muyenera kufika pamalo oti muziti, “Chabwino, izo...tsopano, mwinamwake, m'bale, ngati inu mukanamvetsa, momwe ine ndikuchitira, inu mukanamverera monga ine ndikuchitira za izo.” Mukuona? Ndipo kungokhala okoma kwenikweni kwa iye, ndipo nkumangopitirira monga chomwecho. Ndipo ngakhale ife titakhala osamvetsetsana monga momwe kummawa kwatalikirana ndi kumadzulo, izo zizingapange kusiyana kulikonse.

²⁰ Monga ine ndinanena usiku wina, ine ndiri ndi mchimwene amene ali...ndi munthu wamkulu msinkhu, Melvin; iye ndi wamtali, wamutu-wakuda. Tsopano, ife sitimawoneka ofanana ngati kuti pali chibale chirichonse. Ndipo zathu—zilakolako zathu nzosiyana, ndipo zokhumba zathu nzosiyana; komabe amayi ake ndi amayi anga, abambo ake ndi abambo anga, iye ndi mchimwene wanga. Mukuona? Chifukwa ife tinabadwira m'banja limodzi.

²¹ Tsopano, ife tamasiyana. Melvin si Mkhristu, ndipo iye amakonda baseball, mjaha wa akavalo, ndi zinthu monga choncho. Ndipo ine—ine ndikuganiza kuti iye amakonda chitumbuwa cha chokoleti, chotero ine ndikutsimikiza ife timasiyana pamenepo. Chotero ine—ine sindimakonda mjaha wa akavalo kapena baseball, ine ndimakonda kuwedza ndi kusaka. Mukuona? Ndipo iye sangatembenuze dzanja lake chifukwa cha zimenezo, ndipo ine sindingatembenuze dzanja langa chifukwa cha zinazo. Chotero ndiye, onani, koma iye amakonda chitumbuwa cha chokoleti ndipo ine ndimakonda cha nthudza. Chotero ndiye...

²² Tsopano, ine sindikutsindika, mwawona. Koma ine ndinanena zimenezo nthawi ina mu msonkhano kwinaakwake, kuti ine ndimakonda chitumbuwa cha chokoleti, ndipo usiku wotsatira ine ndinali ndi pafupifupi machokoleti asanu... kapena chitumbuwa cha nthudza, ndipo ine ndinali ndi zitumbuwa foro kapena faivi za nthudza zomwe alongo anaphika ndipo anandibweretsera ine. Mai! Kodi ife tinali ndi phwando mchipinda changa! Koma, ine—ine sindikutanthauza izo mwanjira imeneyo. Mukuona?

²³ Chotero ine ndikutanthauza kuti ndikusonyezeni inu kusiyana kwake, inu mwawona. Koma ziribe kanthu chimene iye ali, ine ndimamukonda iye, iye ndi mchimwene wanga. Ndipo chotero iye si Mkhristu chifukwa iye amawona zinthu mu kuwala kwina, ine ndimawona zinthu mu Kuwala kwa Khristu; komabe

ine sindinganene kuti iye si mchimwene wanga, chifukwa ndife abale obadwira m’banja limodzi.

²⁴ Tsopano, usiku watha, ine ndinapanga chobwereza pomaliza. Ndipo kumbukirani tsopano, uthenga woyamba unabwera ku mpingo pambuyo pa womwe inu mukuwudziwa, kupatula wa kumusi kuja mu Kentucky, unali wakuti padzakhala zinthu zodabwitsa pa msonkhano uno zomwe zidzagwedeze ambiri. Mukukumbukira zimenezo? Izo ziri pa tepi, tsopano. Mukuona? Usiku wathawu chimodzi cha izo chinawululidwa. Chotero izo zinakhala ngati zinaima kwa mphindi yokha, koma ine ndikutsimikiza inu munachigwira icho; chifukwa Mzimu Woyera unabweretsa, zomwe zimayenera kudzachitika: “gehena Wamuyaya, mulibemo chinthu choterocho mu Baibulo.”

²⁵ Mulibemo gehena Yamuyaya. Ngati mungakhale ndi Yamuyaya... Ngati ungakawotchedwe ku gehena kwa Kwamuyaya, ndiye kuti iwe uyenera kukhala ndi Moyo Wamuyaya kuti ukakhale kumeneko, ngati uli moyo. Ndipo ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndiwo Mulungu! Mukuona? Chotero, ndiyeno Baibulo silimaphunzitsa za gehena *Yamuyaya*, limaphunzitsa “yanthawizonse” gehena. Izo zitha kukhala kwa zaka teni sauzande milioni, ine sindikudziwa, koma iyo idzayenera kudzatha.

²⁶ Chifukwa ine ndimayenera kuzibweretsa Izo mmenemo. Ine ndikuziika Izo kutali ndi mipingo ndi zinthu mpaka ine... ziri kwa ine kuti ndinene Izo. Ndiyeno pali zinthu zingapo muno zimene ziti zikhale kwa ine kuti ndizinene Izo, ndiyeno usiku uliwonse ife tikumazipeza izo.

²⁷ Koma tsopano, kuyambira usikuuno mpakana, muyambe kuvala kuganiza kwanu kwauzimu, inu mukuwona, mulole Mzimu Woyera uzilowetse Izo mkati. Ndiyeno ngati inu mungamvetsere ndipo nkusagwirizana nazo Izo, mudzangochokapo ndi kuti, “M’bale Branham wosauka, iye—iye ndithudi sakudziwa. Ine ndikamupempherera iye.” Ndipo muzichita zimenezo, ndiyeno ine ndidza... Ambuye adzandipanga ine kudziwa Choonadi pameneo, koma inu musingondimvera ine chisoni, ndipo osati—osati munditayire ine kutali. Chotero ndiye izo zikhoza kukhala zowona, aponso, koma, oh, ine ndikukhala ndi nthawi yabwino chomwecho kumaganiza izo mwanjira iyi. Chotero izo zikungopangitsa mapeto aliwonse kukumana. Ndipo ine, oh, ine—ine ndikhoza kulakwitsa; koma pakhoza kukhala kusamvetsa pameneo penapake kumene ine sindikudziwa kanthu ka izo, chotero mwinauwake inu mukudziwa, ndipo inu mupemphere kuti Ambuye awonetsere izo kwa ine.

²⁸ Ndipo tsopano, ndipo pamwamba pa zinthu zonsezo, zipitirirani kupempherana wina ndi mzake ndipo

musadzamulole konse mdierekezi kuti adzakuwonetseni kuyipidwa kulikonse paliponse. Mukuona? Musunge miyoyo yanu yoyera mu ora lino, pakuti ife tiri mu maora otsekera a mbiriyakale ya dziko lino. Mukuona? Ife tiri kumapeto, abwenzi, popanda mthunzi umodzi wa kukaikira.

²⁹ Pamene ife tikubwera motsatira mibadwo ya mpingo iyi, ife tipeza posachedwapa, ndipo mwinamwake zochuluka za izo usikuuno. Ife mochulukira kapena pang'ono tikubwerera mmbuyo ndipo tikuika maziko pamene ife tingatsekere izo, ndipo tsopano usikuuno ife tiwulula zinthu zina zenizeni zauzimu. Kumbukirani tsopano, ine ndanena zimenezo, inu muyenera kuvala kuganiza kwanu kwauzimu. Koma penyani Malemba, ziyenera kukhala *mu* Malemba, ndipo ziyenera *kudutsira* mMalemba. Mukuona? Tsopano kumbukirani... Chidziwitso chabe cha Mawu, akuti, “Chabwino, ine ndinapita ku sekondale sukulu. Ine ndinapita ku Baibulo sukulu. Ine ndinapita ku koleji.” Zimenezo sizitanthauza kalikonse. Afarisi onse ndi Asaduki ankachita chinthu chomwecho, ndipo anaphonya kumudziwa Yesu mwa mailosi milioni. Mukuona?

³⁰ Malemba, vumbulutso la Malemba, “izo zinabisika kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo zinawululidwa kwa makanda omwe angathe kuphunzira.” Chotero tiyeni inu ndi ine tikhale makanda ndipo tingotsitsa mitima yathu, ndi kunena, “Ambuye, Inu—Inu mutiuze ife, ndipo ife—ife tikumvetsera.” Ndipo mukatero mugwire tanthauzo lauzimu lake. Tsopano kumbukirani zimenezo, mawu omwe ati ayankhulidwe kuyambira usikuuno mpakana, mugwire tanthauzo lake lauzimu, chifukwa ife tikubwera mu m'badwo wa mpingo wodabwitsa kwambiri.

³¹ Tsopano, ine ndikuganiza izo zinali zonse. Tsopano kumbukirani mawa usiku, ife tidzikhala pa m'badwo wina wa mpingo usiku uliwonse. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti ife tikhoza kudzakhala ndi nthawi yochuluka mawa yoti tidzayendetse utali wa tsiku lonse pa izi, ndipo kenako mawa usiku aponso. Koma, onani, ambiri a iwo adzakhala akugwira ntchito ndipo ine ndidzayesetsa kudzatenga zapamwamba kumene za uthenga uwu, kudzagunda malo omwe akukambidwa apa, omwe mungatenge amodzi a iwo ndi kumangopitirirabe, kuziyendetsa izo mpaka osadziwa kuti zikulowera kuti. Inu mukuona? Koma...Ndiyeno mukawerenge izo kunyumba, ndipo ine ndidzakhala ndikukupemphererani inu, ndipo muzindipempherera ine, ndipo Mulungu atidalitse ife palimodzi monga ana Ake okhulupirira.

³² Tsopano ife tisanayambe, ine ndikudabwa ngati izo sizingakhale zokuvutani kuti ife tithe kuimirira.

Ndipo inu mukudziwa chifukwa chimene ine ndimakondera kuimirira ndi kupempherera? Yesu anati, “Pamene inu muimirira,

ndikupemphera, pempherani, ‘Atate Athu Akumwamba.’ Mukatero khululukiranani wina ndi mzake.” Inu mukuona? Ndiyeno Gideoni anasankha gulu lake lankhondo nthawi ina pakati pa omwe anali akugwa mapewa ndi omwe ankaweramira pansu ndi kumanyambita madzi, kapena omwe ankaimirira ndi kumamwa madzi. Inu mukuona? Chotero iwo omwe ankagwa, omwe anakhala—anaxhala akudzirambatitsa okha pamaso pa mafano, ndipo iye ankadziwa kuti iwo sanali oyenera kupita. Chotero, omwe ankaimirira ndi kumapenya ndi diso lawo nthawi zonse. Ndi momwe ife tikuchitira, kuimirira ndi kumapemphera. Tsopano, ine ndimakhulupirira mu kugwada ndi kupemphera, aponso; koma, kuimirira ndi kupemphera, ine ndikuganiza izo zimangotanthauza chinachake kwa ife, mwanjira ina.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, mtima uliwonse uwerame nawonso:

³³ Atate Akumwamba Achisomo, pamene ife tsopano mwaulemu tikuyandikira Mpando Wanu wachifumu wachirungamo. Ndipo ife sitikubwera kudzakufunsani Inu kuti mutipatse ife chirungamo, chifukwa ife tonse tikhoza kuwonongedwa, koma tikubwera, kudzachonderera “Chifundo, O Ambuye!” Tsanulirani pa ife, usikuuno, za Mzimu Wanu Woyera; osati chifukwa choti ndife oyenera, koma chifukwa choti ndife osayenera, ndipo tikuzindikira zimenezo ndipo tikudziwa zimenezo, ndipo sitikubwera mu dzina lathu lathu, chifukwa ilo ndi losakwanira. Ife tiribe chirungamo, kapena—kapena kanthu, chirungamo chatu chenicheni chingakhale nsanza zauve pamaso Panu. Chotero tikubwera modzichepetsa mu Dzina la Ambuye Yesu, kumubweretsa Iye patsofelo pathu, Magazi a pangano Lake, kuwanyamulira Iwo pa mitima yathu, ndi kunena kuti, “Mulungu, tichitireni ife chifundo ochimwa amene tikupempha chifundo mu ora la kupsyinjika.” Kutu, pamene tsikulina ulaliki wotsiriza ukadzalalikidwa, ife sitikudziwa kuti lidzakhala liti; nthawi yotsiriza kudzakhala mfuu uti udzapite mu mlengalenga; Baibulo lidzagona lotsekedwa paguwa; mikono idzawunjikidwa; ndipo mipope idzakhala ikulira; dzuwa lidzakhala likukalowa. O Mulungu! Ndiye mudzandibise ine, O Thanthwe la Mibadwo, mu ora limenelo.

³⁴ Ndipo ife tikuwona kuti palibe kothawira tsopano, palibe china koma kudzera mwa Inu. Ife tikuwona mafuko akusweka. Ife tikuwona kuti Baibulo likukwaniritsidwa. Ife tikuwona Israeli akuwuka. Ife tikuwona Uthenga kwa Mpingo. Ndipo ora langotsala pang’ono kutha, pa nthawi ya zinthu zazikulu kuti ziwululidwe, ndipo Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwire zikutsegulidwa.

³⁵ Mulungu, Mulungu, O Mulungu, tichitireni ife chifundo, ife tikupempha chifundo. Ndipo monga wantchito Wanu, ine ndikupempha chifundo kwa mmodzi aliyense mu Kukhalapo

Kwauzimu usikuuno. Mulungu, pasakhale munthu mmodzi pakati pathu amene ali ndi uchimo pa moyo wake, koma mulole atsukidwe pakali pano ndi Magazi a Ambuye Yesu, kuti ife tonse tikakhoze kukomana mmalo achisangalalo amenewo kutsidya la thambo.

³⁶ Ndipo pamene ine ndikuyandikira Lemba ili usikuuno, Atate, oh, ndine wosakwanira. Mulungu, palibe aliyense wa ife ali wokwanira. Ife tikuvomereza kuti sitikudziwa kalikonse, Atate, koma molemekeza ife tikudalira pa Mzimu Woyera kuti Iye akakhoze kuwulula kwa ife. Pamene ife tikufutukula kudzera chathu—chidziwitso chathu chomwe chimene Inu mwatipatsa ife, mbiriyakale, mulole Mzimu Woyera upereke kutanthauzira kwauzimu ku mitima yathu. Perekani izi, Atate, pakuti ife tikuyembekezera pa Inu mu Dzina la Yesu Mwana Wanu. Amen. Mukhoza kukhala pansu.

³⁷ Mu mutu wa 2 wa Bukhu la Chivumbulutso, ndi mpingo wachiwiri, m'badwo wa mpingo wachitatu. Kuyambira... [Mlongo akuyankhula mu lirime lina—Mkonzi]. Mundikhululukire ine.

³⁸ Atate athu Amene muli Kumwamba, Dzina Lanu liyeretsedwe. Ufumu Wanu udze, kufuna Kwanu kuchitike, padziko lapansi monga Kumwamba. Ife tikukupemphani Inu kuti mukhale nafe, Atate, ndipo mutidalitse ife, ndipo mutithandize ife kuti tikhale akatswiri omanga bwino mu ora ili lamasautso aakulu pakati pa anthu. Pamene chisokonezo ndi zonse zikuchitika, tithandizeni ife kukhala opambana, Ambuye, kuti tikhale antchito Anu kudzera mu Dzina la Khristu. Amen.

³⁹ Tsopano, ine ndinanena zimenezo poyambirira, kuti inu mukhoze kudziwa. Kodi inu munawona kutanthauzira sikunabwere ku Mawu? Mlongo wathu anadzozedwa ndi Mzimu Woyera, sindikukaika, koma iye amapereka uthengawo Mawu atabwera kale, inu mukuwona. Zangochoka pang'ono kuchoka ku dongosolo la chinthucho. Tsopano, izo zinali zabwino, mlongo wokondedwa, yense yemwe inu muli. Mzimu Woyera ukakhala pa iwe, oh, zimakhala zovuta kuti uzigwire izo munga choncho, ine ndikudziwa. Izo ziri monga... Kapena pamene iwe ukunena chinachake chimzake ndipo... Mukuona, koma izo zinali zabwino; koma mwinamwake inu munamverera izo ife tisanayambe nkomwe, inu mukuwona. Ndipo ndi chifukwa chake, onani, izo zimabwerera pamene Mzimu ukugwira ntchito. Mizimu ya olosera imawamvera aneneri, inu mukuwona. Ndi iweyo.

⁴⁰ Tsopano, mwinamwake Mzimu Woyera ukudzozaninso inu kachiwiri, basi... Ine ndikuyembekeza Iwo utero, ukangotha msonkhanowu. Ndipo inu muwone kutanthauzira kukabwera, mwaona, chifukwa iko kuyenera kukhala molunjika kumene mu dongosolo pamenepo, inu mukuwona;

koma ife tikungowayandikira Mawu, inu mukuwona, muno. Chotero, tsopano, izo zinali kwenikweni za Mulungu, izo zinali kwenikweni; ine ndikukhulupirira zimenezo ndipo ine ndikumverera izo ndi mtima wanga wonse, chifukwa ine ndinamverera kubwerera mmbuyo kwa izo, inu mukuwona. Koma Mzimu Woyera...sinali nthawi yake. Iye ali ndi uthenga kwa mlongoyo wa kwa mpingo, koma *pano* ndi pamene Iye akuchita Uthenga Wake tsopano. Inu mwaona, Iye sangadzisokoneze Yekha, Iye amayika zinthu zonse mu dongosolo. Inu ndikutsimikiza aliyense akumvetisa, inu mwaona, izo zoono basi.

⁴¹ Tsopano mu—mu mutu wa 2 wa Bukhu la Chivumbulutso. Ndipo ndiroleni. . . Ife tiyamba usikuuno ndi—ndi M’badwo wa Pergamo, mutu wa 12. Tsopano, usiku wathawu ife tinasiyira pa ndime ya 11:

*Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene
Mzimu akunena kwa mipingo; Iye amene alakika
sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.*

⁴² Tsopano, mu m’badwo wa mpingo woyamba, ife tinapeza kuti Chinikolai chinayambitsidwamo. Mulungu amadziulula Yekha monga...Yesu amadziulula Yekha ngati Mulungu Wamphamvuzonse: panalibe wina, panalibe magawo, panalibe zidutswa za Mulungu, Iye anali Mulungu yekha.

⁴³ Tsopano, mu m’badwo wa mpingo wa usiku watha, ife tinapeza kuti Iye anaima pakhomo ndipo Iye analemba zinthu izi kwa mpingo, ndipo anawauza iwo za umphawi wawo. Koma Iye anati iwo anali pa . . . Anikolai awa, ndi zina zotero, zomwe Iye ankadana nazo.

⁴⁴ Dzulo usiku iwo anali . . . anavala korona wa ofera. Iye anawauza iwo kuti asachite mantha, kufikira imfa, kuti Iye akanadzati—Iye akanadzakhala ndi iwo. Ndiyeno pomaliza pake Iye anati, “Iye amene alakika! Iye amene alakika sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.”

⁴⁵ Tsopano, ngati pali imfa imodzi, ndipo ife tikudziwa za iyo, ndiye payenera kukhala imfa ina kwinakwake; chifukwa imfa imodzi ife timafa iyo kuno mwathupi, imfa yachiwiri ife timafa iyo mu mzimu, solo. Ndizo, “Ndipo moyo umene uchimwa iwo ndithudi udzafa.” *Kufa* ndi basi, “mwamtheradi kutuluka kuchoka kwa chirichonse;” inu mwawona, ndinu—ndinu . . . *Imfa* imatanthauza, “kutengedwera kutali, ndiko—ndiko—ndiko kutengedwera kutali, kukabisidwa.” Ndiye pamene okonedwa athu afa, iwo samakhalaponso monga momwe tikudziwira. Ife timaitcha imeneyo imfa.

⁴⁶ Koma Mkhristu samafa. Palibepo Lemba lakuti Mkhristu amafa, chifukwa iye ali ndi Moyo Wamuyaya. Pamene wochimwa afa, iye amathetsedwa, ndipo solo yake potsiriza idzafa. Koma pamene Mkhristu afa, iye amakhala akungoyembekezera

limodzi ndi Yesu kuti adzabwerere kachiwiri. Oh, ine ndikuyembekeza ine ndikhala nayo nthawi yoti ndifike kwa zimenezo kumapeto a masomphenya awa usikuuno, kwa izo kumene ife tidzabwererako; ndipo inu mudzaziwona izo, momwe izo zidzabweretsere chinthu chomwecho cha imfa yachiwiri. Mutu womwewu umene ife tirimo usikuuno ukubweretsa chinthu chomwe chomwecho, ndi kagwiritsidwe ntchito kokongola komweko apa.

⁴⁷ Tsopano—tsopano, usikuuno, ife tiwerenga kalata iyi mofulumira, chifukwa ine ndiri ndi zina—nkhani zina mwambiriyakale ife tikufuna kufikako poyamba, ndipo ndiyetsa kuti ndisakusungeni inu motalika kwambiri. Tsopano, pa . . . misonkhano iyi ikatha, nthawi iliyonse imeneyo ine ndikumawerenga izi mofulumira, ngati inu mukufuna kuti mudzapeze tanthauzo la izo; M'bale Mercier apa ali nazo zonse, ine ndipereka zolembazo kwa iye; ndipo iye akhoza chifukwa iye akulemba bukhu, iye adzakupatsani chirichonse chimene mukuchidziwa . . . inu—inu mukufuna pa izo. Zimenezo zingakhale zabwino, M'bale Mercier.

⁴⁸ Ndime ya 12:

Kwa mngelo wa mpingo wa Pergamo lemba; Zinthu izi anena iye wakukhala nalo lupanga lakuthwa kosekonse;

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi komwe iwe umakhalako, ngakhale. . . Mpando wa satana. . . ndipo iwe ukugwiritsitsa dzina langa, ndipo sunakane chikhulupiriro changa, ngakhale mmasiku aja Antipasi anali wofera wanga wokhulupirika, amene anaphedwa pakati panu, kumene Satana akukhalako.

Koma ine ndiri nazo zinthu pang'ono zotsutsana ndi iwe, chifukwa uli nawo komweko akugwira chiphunzitso cha Balamu, yemwe anamuphunzitsa Balaki kuti akaponye chopunthwitsa pamaso pa ana a Israeli, kuti azidya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano, ndi kuchita chiwerewere.

Chomwechonso uli nawo iwo amene agwiritsitsa chiphunzitsocho. . . (izo zinali ntchito kumbuyo uko mu Efeso, tsopano zadzakhala “chiphunzitso”) . . . chiphunzitso cha Chinikolai, . . . (Inu mukukumbukira ine ndikukuuzani inu zimenezo usiku wina, momwe izo zinayandikira kwa izo? Ntchito mu Efeso, tsopano ndi “chiphunzitso”) . . . chi—chiphunzitso cha Chinikolai, zinthu zomwe ine ndimadana nazo. (Uhm!)

Lapani; kapena ukapanda kutero, ine ndidzabwera kwa iwe msanga, ndipo ndidzamenyana nawo iwo. . . (osati Mpingo weniweni) . . . iwo okhala ndi lupanga la mkamwa mwanga.

Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu akunena kwa mipingo; Kwa iye amene alakika ndidzampatsa kudya mana wobisika, ndipo ndidzampatsa iye (iye) mwala woyera, ndi mmwalawo dzina latsopano lolembedwa, limene palibe munthu aliyense akulidziwa koma iye amene alilandira ilo.

Tsopano Ambuye awonjezere madalitso Ake pa Izi, ndipo atithandize ife tsopano pamene ife tikuyesera.

⁴⁹ Tsopano pamaziko a mpingo uwu. Ndi m'badwo wa mpingo wachitatu, wotchedwa Pergamo. Ndipo a—tsiku lomwe mpingo uwu unayamba kukhalapo ndi kuyambira 312, A.D. 312 mpaka 606.

⁵⁰ M'badwowo unali: chiphunzitso chabodza, kunama kwa Satana, maziko a ulamuliro wa upapa, ndi kukwatirana kwa mpingo ndi boma.

⁵¹ Mphotho yake inali: manna obisika, mwala woyera.

⁵² Ndipo nyenyezi, mngelo wa mpingo uwu, mwa zonse zomwe Mzimu Woyera wandilola ine kuti ndichite, ine ndamusankha Martin Woyera. Ilo linali vu—vumbulutso lomwe linaperekedwa kwa ine pa zimenezo, chifukwa powerenga za oyera ena panthawi iyi. Ine ndinamusankha Martin Woyera chifukwa chakuti iye anali munthu waumulungu, mwa kulingalira kwanga iye anali mtumwi kuchulukitsa ka teni kumuposa Patrick Woyera.

⁵³ Tsopano, Patrick Woyera anali mmphwake wa Martin Woyera; Mlongo wa Martin Woyera anali amayi ake a Patrick Woyera. Ndipo Martin Woyera anali... zachidziwikire, amenewo anali amalume ake a Patrick Woyera.

⁵⁴ Tsopano, moyo wake unali kuyambira A.D. 315 mpaka 399. Tsopano nacha chifukwa chimene ine ndinamusankhira iye mmalo mwa oyera ena a tsiku limenero, chifukwa cha momwe iye amadzigwirira iyemwini. Ndipo pansa pa kudzoza kwa Mulungu, ine sindikukhulupirira kuti...

⁵⁵ Tsopano, mpingo wa Katolika sunamuvomereze iye, iwo sanamuzindikire iye, ndipo ndicho chifukwa china ine ndinamusankhira iye. Uh-huh, uh-huh. Ndipo onse awa amene ife tikuwawona, omwe ali ndi utumiki wauzimu, mpingo woyambirira uja unawakana. M—mpingo wa Chinikolai unazikana izo chifukwa cha zinthu izi: iwo anali auzimu. Ndipo monga ine ndajambulira apa, Mpingo unali ukufinyidwira panja ndipo chiphunzitso cha Chinikolai chinali mu—chinali mwa ambiri; ndipo Mpingo woona unali mwa ochepa, wakhala uli nthawizonse.

⁵⁶ Ndipo monga ine ndinanena kuchokera pachiyambi, anali Yesu yemwe anati, “Musawope, nkhosa zapang’ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu.”

Ndi chifukwa chake ndimawuika Ufumu ku Ufumu wauzimu. Ndipo ife tiri. . . tiri ndi Ufumu wauzimu, ndipo ndife okondwa kwambiri ndi zimenezo, komanso Mfumu mu Ufumu uwu. Kumbukirani, Iye ndi Mfumu ya oyera (*oyera awo*), Iye ndi Mfumu yawo yomwe imawatsogolera iwo.

⁵⁷ Moyo wa Martin Woyera unali. . . ndi umodzi wa miyoyo yodzaza ndi zozizwitsa kwambiri kuposa wa wina aliyense mmibadwo ya mpingo. Kuchokera njira yonse kuyambira kwa Paulo Woyera kutuluka, iye anali mmodzi wa anthu auzimu kwambiri. Iye anali. . .

⁵⁸ Chimodzi cha zozizwitsa chake choyambirira chinali. . . Iye anali msirikali, kuyamba ndi kuyamba, ine ndikukhulupirira. Ndiyeno tsiku lina iye anali kubwera pamene ndipo panali winawake. . . M—munthu atagona, atazizidwa komanso akunjenjemera, ndi anthu onse omwe anali ofunitsitsa. . . kapena, osati ofunitsitsa, koma anali okhoza kumuthandiza munthuyo, iwo ankangomudutsa iye monga wa—wansembe ndi Alevi ankachitira mu *Msamariya Wachifundo*. Koma pamene Martin Woyera anabwera, pozindikira udindo wake ngati Mkhristu wokhulupirira, iye anali ndi chikhoto chimodzi, chofunda pa mapewa pake, iye anachidula icho pakati ndi lupanga lake ndipo anapereka theka kwa wopemphetsayo, iye anatenga theka linalo. Ndipo usiku umenewo anayamba ntchito yake, chifukwa, Yesu Khristu anawonekera kwa iye, mmasomphenya, anadzifunditsa mkanjo womwewo umene iye anawudula pakati; zomwe zinakwaniritisa Lembu, “Mochuluka momwe inu mwachitira kwa awa, inu mwachitira izo kwa Ine.”

⁵⁹ Chotero mutenge zimenezo ngati phunziro. Chirichonse chomwe inu mungamuchitire wina, inu mwachitira icho kwa Khristu. Muzikumbukira basi. Tsopano inu. . . Tiyeni tinene izo pamodzi [M'bale Branham ndi osonkhana akuyankhula mogwirizana—Mkonzi.]: “Zomwe inu muchitira ena, inu mwachitira kwa Khristu.” Chotero ziribe kanthu zomwe iye akuganiza za inu, ndi zomwe inu mukuganiza za iye, mwawona, zimenezo zimabweretsa mdalitso.

⁶⁰ Chimenecho chinali chozizwitsa chake choyambira ndi kuyamba kwa utumiki wake. Pali zochulukwa kwambiri kwa izo, ine—ine sindingakhale nayo nthawi. Chifukwa ine ndikufuna inu mubwerere mawa usiku ndi usiku uliwonse, chotero ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalika kwambiri.

⁶¹ Chabwino, chozizwitsa chotsatira chimene ndinasankha kuti ndiyankhulepo usikuuno.

⁶² Iye mwamtheradi anali akuchigwetsa chikunja, ndipo iye anali wotsutsana mwamphamvu mpingo waku Roma. Iye mwamtheradi sanagwirizane ndi mpingo wonse woyamba wa mabishopu aku Roma, iye. . . iwo amayamba kukhala achidziko ndi zina zotero monga choncho, ndipo iye anawatsutsa iwo.

Iye ndithudi amatsutsana nawo iwo. Ndi chozizwitsa kuti iye anakhalapo mu nthawi za mtundu umenewo. Tsopano . . .

⁶³ Koma iye anali kuwononga malo achikunja tsiku lina, ndi kugwetsera pansu guwa lachikunja, ndipo kunali mtengo wopatulika umene unali pafupi ndi guwa lachikunja. Ndipo iye anali kuwudula mtengo uwu, ndipo ambiri anali ataimirira pamenepo amazikana izo. Iye anati, “Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu . . . Mundimangirire ine komwe mtengowo watsamira ndipo musiye mtengowo ugwere pa ine. Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu . . . Ngati sindine munthu wa Mulungu, mtengowo undipha ine. Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu, Mulungu wanga akhoza kuwukhotetsa mtengowo kwinakwake.” Chitsutso ndithu! Chotero iwo anayamba kuwudula mtengowo; ndipo pamene mtengowo unayamba kugwa, iwo unatembenuka ndipo unapha gulu la owonererawo. Mulungu anawupotozera iwo kubwerera cha ku phiri. Chozizwitsa! Oh, nthawi zonse mumakhala zozizwitsa mu msonkhano wake.

⁶⁴ Chozizwitsa china chimene ndimaganiza kuti ndiyankhule, chinali khanda lakufa limene anagonekapo thupi lake. Ndipo iye anauka ku moyo kenanso, iye atamupempherera kwa kanthawi mwana uyu.

⁶⁵ Wina umene unali wapadera kwa ine, unali wa mfumu. Ndipo amapita kukapha ena a anthu a Mulungu odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo zoonadi anali dzanja lamanja la—la bishopu wa mpingo woyamba waku Roma, pa nthawi imeneyo, ndipo iye kwenikweni anali papa iye asanatchulidwe papa. Dzina lake anali D-a-m-a-s-u-r, ndipo anali kupha Akhristu onse omwe amakwanitsa kuwapeza kuti awaphe. Ndipo—ndipo mkazake wa mfumu uyu, wachikunja, ndipo mdima uli pa mtima pake pomwe.

⁶⁶ Ndipo pamene woyera uyu Saint Martin anabwera kudzaimira pakati, mkazi wake anamuyika iye pafupi pomwepo kuti iye ayesere kupembedzera Akhristu awa kuti asaphedwe. Ndithudi, pamene iye potsiriza anadzafika kwa iye, sizinachite ubwino uliwonse, chifukwa iye anangokhala munthu wa dzanja lamanja kwa papa uyu; chotero iye amawapha Akhristu odzazidwa ndi Mzimu Woyera awo mulimonse.

⁶⁷ Koma Martin Woyera ankafuna kuyankhulana naye iye, ndipo alonda anamuyimitsa iye pa chipata. Chabwino, Martin Woyera anagwa pa nkhope yake ndipo anagona pamenepo ndi kupemphera mpaka Mulungu atamuwonetsera iye kuti alowe. Pamene iye anadzuka kuchoka pamenepo, iye anayenda kupita ku zitseko zolokedwa izo ndipo izo zinatseguka zokha, anayenda kumapitirira.

⁶⁸ Tsopano, iyi ndi mbiriyakale, uyu si winawake amene akulemba za iye, ndipo basi pang’ono chabe . . . Ngati chirichonse, iwo akhoza kukhala atsankho, ngati izo

zikanakhala kuti mpingo wina ukuyankhula; kapena, ine ndinganene, osachepera, makamaka tchalitchi cha apapa, iwo sibwenzi atatchula zinthu zimenezo. Koma, mwaona, mbiriyakale imabwereza choonadi. Mwaona?

⁶⁹ Ndipo bambo uyu anayenda chokwera pamenepo, Martin Woyera, ndipo kumudutsa mlonda aliyense, ndi china chirichonse, mpaka pamaso pa mfumu. Ndipo mfumuyo siinafune kulemekeza wantchito wa Mulungu. Inu mukudziwa, izo—izo sichoncho—si khalidwe limenelo. Chotero iye anangotembenuza mutu wake ndipo sanamulemekeze nkomwe iye. Inu mukudziwa chimene Mulungu anachita? Iye anayesetsa kuti ayankhule naye ndipo iye amangotembenuza mutu wake, ndipo Mulungu anali woti awapangitse achikunja awa kuti apereke ulemu kwa wantchito Wake. Chotero Iye anangoyatsa chinthucho ndi moto, ndipo iwo unamuwotcha iye mpaka ananyamuka pa mpando wakewo, unamudzutsa iye, unamupangitsa iye kuti aimirire.

⁷⁰ Tsopano imeneyo—tsopano imeneyo ndi mbiriyakale ya Baibulo, *Nicene Council*. Iye amayenera kumulemekeza wantchito wa Mulungu; Iye anamupangitsa iye kuti ayimirire. Iwo unatentha ngakhale mpando pomwe iye anakhala; moto unadutsa mthupi lake ndi kudzawotcha pansu pampando, ndipo iye anachita kulumpha kuchokera pamenepo. Mulungu ali nayo njira yochitira zinthu, inu mukudziwa. Uh-hum. “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.” Ndipo inu kumbukirani, Mulungu yemweyo akukhala pakati pathu usikuuno. Ndi Mulungu yemweyo. Chabwino.

⁷¹ Ndiyeno wina umene ine ndimawukonda, ndiyeno ine ndiyima. Ine ndiri nawo wina apa, koma ine nditenga... Tsopano uwu ndi umene ine ndimawukonda kwambiri, panthawi yomwe anali kuwadikirira tsiku lina anthu ake, akupemphera mchipinda chake chowerengera.

⁷² Ndipo iye—iye anali munthu wopambana, ndipo iye ankawunyamula Mpingo wodzazidwa-Mzimu Woyera uwu, ndipo ankatikhadzula ife tonse...Oh, iye anali... amawapangitsa onsewo kudzazidwa ndi Mzimu, osonkhana ake onse. Ndipo konsekonse mu dziko lonse, Akhristu ankachita zozizwitsa ndi zodabwitsa.

⁷³ Mwaona, Mulungu amalankhula ndi mthenga Wake, mthenga amalankhula kwa anthu wamba. Ndiyeno ndi zimene zinkachitika, inu mukuona, Iye—Iye amawaika anthu wamba ndi iye mofanana mwa Mulungu; inu mukuwona, Mzimu Woyera umayenderera kupyola mu gulu la iwo.

⁷⁴ Nthawi zambiri pamene iwo aphedwa, iwo amamuimitsa mtumikiyo pakati pawo (monga *choncho*) ndipo amawapha iwo onse nthawi yomweyo. Ndi zoipa zomwe iwo amawachitira anthuwo! Iwo amawawotcha iwo. Iwo ankawatenga amuna

ndi kuwakhomerera iwo ndi. . . pansi pa zipika, ndi kumasula agalu olusa, kapena. . . ndipo nkuwasiya iwo adye ku nsana kwa munthuyo, kumasolola matumbo munthuyo asanafe nkomwe. Kumawatenga akazi, kumawadula mabere awo akumanja, ndi kuwalola iwo ayime pamenepo mtima wawo ukugunda, ndipo nkumagunda mpaka kugwera pansi, nkufa, monga choncho. Kutenga ana awo kuchokera kwa amayi omwe akuyembekezera ndikuwadyetsa iwo ku nkumba ndi zinthu, kuwalola azimayi ayime ndi kumawonerera izo. Ndi mitundu yonse!

⁷⁵ Tsopano, inu simungaganize kuti anthu omwe amati ndi Akhristu angachite zimenezo. Koma mveterani, Baibulo linati, Yesu anati, “Izo zidzachitika kuti iwo adzakuphani inu, kumaganiza kuti iwo akumuchitira Mulungu ntchito.” Inu mukukumbukira, Yesu yemwe uja amene ananena zimenezo, kupyolera Mzimu womwewo, ananeneratu izo kachiwiri mu nthawi yotsiriza. Izo zikuyenera kudzabwera. Ngati zinazi zinagundana mwangwiro ndi Lemba, penyani ndipo muwone ngati izo sizikugwirizana ndendende kudzera mu Lemba ndi kudutsa mbiriyakale. Mulungu anati zidzachitika, mbiriyakale ndi iyi yonena kuti izo zinachitikadi; Mulungu anati izo zinachitika apa, ndipo apa ndi pamene izo zinadzachitika. Mwaona, ndendende basi. Ndiye kodi ife tidzachita chiyani pamene tidzafika ku M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya (onani, pamene ife tiri tsopano) ndi matsoka ndi zinthu zinalengezedwa zotsutsa iwo?

⁷⁶ Chotero, tsopano, ndiye izi, iye anali mmenemo akupemphera pamene osonkhana ake anali akudikirira. Ndipo kunali wopemphetsa anafika pakhomo ndipo anadzagogoda pakhomo pake, ndipo iye anatsogola chitseko (ndipo iye anali atatanganidwa), ndipo iye anamuwuzira kuti akufuna cho—chovala. Iye anali wamaliseche ndipo analibe kalikonse, kunali kukuzizira, ndipo iye anati. . . Iye anamutumiza kuseri kuti akawonane ndi dikoni wamkulu. Ndipo dikoni wamkulu anali wokwiya naye ndipo anamuthamangitsa iye. Ndipo pamene iye anatero, iye anathamangira kuseri, iye anadzabwereranso kachiwiri ndipo anadzamuza Martin Woyera kuti—kuti—dikoni wamuthamangitsa iye.

⁷⁷ Ndipo chotero ndiye, pafupi nthawi imeneyo, dikoni wamkulu uyu anadalowanso mkati ndipo anadzamuza iye mokalipa, kuti, “Osonkhana anu akukuyembekezera inu! Inu mukuwadikiritsa iwo!” Koma iye anali mu pemphero. Ndi kwabwino kuti iye akhalebe mu pemphero kufikira atamva kutsogozedwa ndi Mulungu kuti atuluke.

⁷⁸ Ndipo wopemphetsa uyu anabwerera pakhomo. Ndipo Martin Woyera anavula chovala chake chabwino ndipo anachipereka icho kwa wopemphetsayo, ndipo anamuza di—di—dikoni wamkuluyo kuti apite ndi kukatenga china ndikubwera nacho kwa iye. Chotero iye amayenera kuti

akatenge chovala, mulimonse, ndi kuchiveka icho pa Martin Woyera. Ndipo iye anavala chovala chotsikirapo pamaso pa anthu mmalo mwachovala chake chabwino.

⁷⁹ Mwaona izi zikungowonetsera kuti: muzipereka zabwino zomwe muli nazo, muzipereka moyo wanu, muzipereka nthawi yanu, muzipereka chirichonse kwa Khristu. Ndipo Mzimu womwe uja umene umakhala mwa Khristu, udzakhala mwa inu, ndipo—ndipo chikoka chanu mdera lanu komanso pa anthu omwe inu mukuchita nawo, chidzakhala chofanana kwambiri ndi Khristu mpaka chidzagwira ntchito yofanana ndi yomwe Khristu ankachita.

⁸⁰ Potsiriza zinafika pochitika kuti anthu ankagona mmithunzi ndipo amachiritsidwa. Uko—uko nkulondola, basi amakhala ndi mphamvu yochulukira kwambiri powazungulira iwo. Ndipo iwo ananena kuti “Pamene Martin Woyera amalalikira, atatuluka atavala mwinjiro wotsika uyu, kuti osonkhana onse anazindikira kunyezimira kwa Kuwala paliponse pomuzungulira iye.” Uh-huh. Mukuona? Mwaona, chifukwa iye anali atachita chinthu cholondola.

⁸¹ Nthawizonse muzichita zolondola, udindo wanu kwa Mulungu; muziganiza molondola, ndiwo udindo wanu kwa inueni; ndipo mudzatulukapo muli wabwinobwino. Ndiko kulondola, inu muyenera muzitero basi.

⁸² Tsopano, ife tikufuna kuti tiyambe tsopano kuyesera kuti tizitenge izi mu mndandanda wa kufokoza, usikuuno, chifukwa Izo zikuchita apa mwamphamvu kwambiri.

Tsopano, kwa mngelo wa mpingo wa Pergamo lemba; Zinthu izi zomwe anena iye amene ali nalo lakuthwa konsekonse- . . . lupanga . . . lupanga lakuthwa konsekonse;

⁸³ Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire Iye akudziwonetsa Yekha kenanso usikuuno mu Umulungu. Mpingo uliwonse unali umodzi wa ulemelero Wake: Umene unali ndi nyenyezi thwelofu . . . kapena “nyenyezi seveni mdzanja Lake, Iye amene ali nalo lupanga lakuthwa konsekonse,” mwawona, chinachake chimzake, “Iye amene ali ndi mapazi a mkuwa, maso omwe amayenderera ndi . . . malawi a moto.” Iye akudzidziwitsa Yekha kubwerera ku Umulungu Wake.

⁸⁴ Tsopano inu mukuti, “Umulungu uli kuti umu, ‘Iye wokhala ndi lupanga lakuthwa konsekonse lotuluka kuchokera mkamwa Mwake?’”

⁸⁵ Chabwino, *lupanga* ndiro “Mawu.” Ahebri 4, ife tinazitenga izo pachiyambi pamene ife tinkayendetsa Umulungu uja wa Iye. Lupanga, ife tinapeza mu Ahebri 4:12, zinali kuti, “Mawu a Mulungu anali akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse.” Nkulondola uko? Amenewo anali Mawu a Mulungu. Kodi ndi choncho . . . ? Pamenepo, tsopano penyani, inu mw- . . . mumvetse

kutanthauzira uku. Tsopano tsatirani Mawu amenewo, Yohane Woyera 1, “Pachiyambi” (kumbuyo uko) “panali Mawu amene analenga miyamba ndi dziko lapansi.” Nkulondola uko? “Ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Umulungu. Ndipo Umulungu unasandulika thupi ndipo unadzakhala pakati pathu.” Nkulondola uko? “Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

⁸⁶ Ndipo apa Iye waima apa, Mmodziyo wa pachiyambi, “Nena izi kwa mngelo wa mpingo wa—wa Perga- . . . Pergamo. Nena izi kwa iye, ‘Ine ndine Mawu a Mulungu.’” Oh, ife tikumuwona Iye cha mu Chivumbulutso, akubwera ndi chovala Chake choviikidwa mmagazi, korona ali pa mutu Wake, atakwera kavalo woyera, ndipo pa ntchafu Yake patalembedwa, “Mawu a Mulungu.” Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. Iye ndi Mawu, Mawu a Mulungu. Chotero ife tikuwona Umulungu uwu ndiye pachiyambi, kuti akuzidziwitsa Iyemwini, Iye ndi Mawu.

⁸⁷ Tsopano, ngati Iye ali Mawu amoyo, ndiye Izi zomwe zinalembedwa pa Baibulo ndizo gawo la Iye; ndiye ngati inu mungalandire Izi, mwa Iye (amene ali Mawu), Mawu awa amabwera mwa inu mwa chikhulupiriro, amawapangitsa Iwo kukhala amoyo, chifukwa . . . Oh! Mukumvetsa Zimenezo! Mawu amabwera mwa inu, ngati Mzimu Woyera uli mmenemo, Iwo amadzakhala amoyo nthawi yomweyo Iwo akangobwera mmenemo, ndipo lonjezo lirilonse ndi loona. Palibe . . . “Chotero, ngati mudzanene kwa phiri ili ‘Suntha,’ ndipo osakaikira mumtima mwanu.” Chifukwa (chiyani?) inu ndi Umulungu mukuyankhula. Inu mukukhulupirira zimenezo? Baibulo linanena chomwecho. Ndipo chirichonse chimene mudzanena chidzafika pochitika ngati simudzakaikira, ngati mungadzachotse zonse za—za chidziko kuzitulutsa mwa inu, nkulola Mzimu Woyera kuti ukupangeni inu kukhala mwana wamwamuna wathunthu kapena wamkazi wa Mulungu: popanda dziko, popanda kutsutsidwa, popanda kukaikira. Ndi chiyani chimenecho, ndiye? Si inunso ayi, ndi Mulungu mwa inu. Ndiye inu mutenge Mawu Ake, Iwo ndi lonjezo, ndi kuti, “Atate, ndi lonjezo Lanu.” “Satana, . . .” Chinachake chikuyenera kusuntha. Mukuona? Mukuona?

⁸⁸ Tsopano, inu simungathe kuchita zimenezo kufikira Mulungu atawulula kwa inu ndiye kuti vutolo lingakhale chiyani. Mukuona? Ndiye pamene inu mwadziwa kuti vutolo lidzakhala lotani, ndiye inu mukhoza kudzanena, monga Yesu. Iye *anali* Mawu. Nkulondola uko? Ndipo komabe Yesu, mwamunayo, kachisi, anati, “Ine sindichita kanthu kupatula ngati Atate atandisonyeza Ine poyamba.”

⁸⁹ Ndiye si Mawuwo ndiye mpaka atadzawonetseredwa kwa inu. Inu mukumvetsa zimenezo? Nzosadabwitsa kuti anthu amanena kuti “masiku a zozizwitsa anapita,” Mawu sanawonetseredwe kwa iwo. Nzosadabwitsa kuti

samakhulupirira mwa Mzimu Woyera, Mawu sanawonetseredwe kwa iwo. Nzosadabwitsa iwo samawona vumbulutso la ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, Mawu sanawonetseredwe kwa iwo panobe; ndipo komabe iwo alibe Lemba limodzi loti apiteko, palibepo malo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mwanjira ina iliyonse.

⁹⁰ Za Mzimu Woyera, Baibulo linanena kuti “Palibe munthu angamutche Yesu kukhala Khristu, kupatula mwa Mzimu Woyera wokha,” ndipo anthu ndiye amanena kuti iwo sakhulupirira kuti Mzimu Woyera ndi wolondola. Mukuona? Mwaona, izo sizinapangidwe kwa iwo. Yesu anati, “Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse omwe Atate ali nawo” (tensi ya mmbuyo) “aperekedwa kwa Ine adzabwera kwa Ine.” Oh, kodi zimenezo si zokongola! “Onse amene Atate andipatsa Ine, adzabwera kwa Ine. Palibe mmodzi wa iwo adzataika kupatula mwana wa chiwonongeke, ndipo Ine ndidzatero. . . (iye anabadwira cholinga chimenecho), ndipo Ine ndidzamuukitsa iye kachiwiri pa tsiku lotsiriza.”

⁹¹ Oh, mai! Uko nkomwe maina athu anaikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa: kuyambira ku maziko a dziko lapansi. Kodi zimenezo si zokongola! Kodi ife tingakayikire bwanjinso?

⁹² O Mulungu, chotsani kukaikira pakati pathu, mungovinira mitima yathu yosauka yaumunthu mpaka sipadzakhala kukayika konse pakati pathu. Ndiro pemphero langa. Mungoyalulapo kukaikira kulikonse, Ambuye. Mundirole ine ndidzikhala mokoma, modzichepetsa, ndi kumayenda ngati—ngati mwanawankhosa wa Mulungu padziko lapansi. Mundirole—mundirole ine ndiziyenda monga Iye ankayendera. Mundirole ine ndiziyankhula monga Iye amayankhulira. Mulole zolinga zanga zikhale monga zolinga Zake. Mundirole—mundirole ine. . . Mulole ena amupeze Yesu mwa ine. Mundirole ine ndidzitaye ndekha ndipo ndikapeze izo, Ambuye, mwa Inu. Ndi zimenezo, mundirole ine ndidzimasule ndekha ndi kukazipeza izo mwa Inu; nditangophimbidwa kwambiri mwa Khristu kufikira kuti osakhalanso kukaikira, basi zomwe Iye anena.

⁹³ Tsopano, musapite kunja kuno ndi kukati, “Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya! Mulungu alemekezeke! Inu mukuwona zomwe ine ndingakhoze kuchita? Ulemelero kwa Mulungu!” Inu simunachipezebe Icho apobe. Njira yake si imeneyo yomwe Iye ankachitira izo, ayi, kutulutsa chidali chake ndikuti, “Mukuwona zomwe ine ndingakhoze kuchita? Inde, bwana. Ndine wa- . . .” Ayi. Iye sanadzitengere matamando pachabe, Iye anapereka izo kwa Mulungu ndipo ankayenda modzichepetsa ndi mokoma, ndi mpweya woterowo pomuzungulira Iye mpaka anthu ankangokonda kukhala pomuzungulira Iye. Adani

Ake okha...Ndipo Iye ankawakonda iwo mokwanira mpaka ngakhale Iye ankawapempherera iwo mosalekeza, nthawi zonse. Ndipo chimenecho chinali chitsanzo chanu, chitsanzo changa, kuti tizichitira ena monga momwe Iye ankachitira kwa ife.

⁹⁴ Tsopano, ife tikufuna kuti tizindikire apa kachiwiri tsopano, mu ndime ya 2, iyo imene ingakhale ya 13:

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi—ndi kumene ukukhalako iwe, ngakhale...mpando wa Satana... ndipo iwe ugwiritsitsa dzina langa, ndipo iwe sunakane chikhulupiriro changa,...

⁹⁵ Mwaona, iwo akukhala kumene Satana wakhala, ndipo iwo akusungabe Dzina la Yesu. Mwaona, “Ndipo sanakane chikhulupiriro Changa.” Kodi Iye anamupatsa chikhulupiriro cha mtundu wanji? Chikhulupiriro cha Chipentekoste, pachiyambi. Iwo anali nacho chikhulupiriro cha Chinikolai kumeneko, bungwe la mpingo, ndi zina zotero, iwo anali kumangirira, tchalitchi chikubwera powonekera pansu pa bungwe; koma Iye anati, “Iwe unachokako kumeneko, iwe unkadana nazo, ndipo Ine ndikuteronso. Ndipo iwe sunakane Dzina Langa; sunatsatire miyambo yawo yaying’ono yakale ndi zinthu, iwe wakhalabe molunjika pa Dzina Langa. Ndipo iwe ukadali nachobe chikhulupiriro Changa monga icho chinali pachiyambi.” Oh, ine ndikuzikonda zimenezo!

...sunakane chikhulupiriro changa, ngakhalenso monga aja mu masiku amenewo (Ndikuganiza kuti mumawatchula kuti A-n-t-i-p-s) Antipas anali wofera wanga wokhulupirika, amene anaphedwa pakati panu, kumene akhalako Satana.

⁹⁶ Ine ndiimira pamenepo miniti yokha. “Mpando wa Satana.” Ife tikufuna tikhale ngati tikuchita pa zinthu izi, ine ndikufuna kuti inu muzigwire Izo. Muwonetsetse kuti inu mukutero, tsopano. “Satana, mpando.” Tsopano, Mulungu analengeza mu Genesis komwe kuli mpando wa Satana, ndipo kumeneko kunali ku Babeloni. Iwo nthawizonse wakhala uli mpando wa Satana, ndipo mu Chivumbulutso chinali chinthu chomwecho. Koma, ngati inu mungazindikire, Babeloni anadzisintha yekha kuchoka ku *chikunja* kudzakhala “upapa.”

⁹⁷ Ndipo tsopano mu zaka zoyambirira, kapena izi zisanachitike (zaka pang’ono), mpando wa Satana unamanga wawukulu...Ine ndikulingalira inu mukhoza kumutcha iye wanse...mfumu-wansembe wa Akaldia. Ufumu wolowezana waku Babeloni unasintha mpando wake nthawi yomwe Aperesia ankamulondola iye, ndipo iye anachoka ku Babeloni. Dzina lake anali A-t-t-a-l-u-s, Attalus, mfumu yaunsembe yaikulu ya ku Babeloni. Pamene Aperesia anadzalowa ndi kudzalanda Babeloni, kuwathamangitsa Akaldia; Attalus, mfumu yawo yaunsembe, anathawa ndipo anakakhala ku Pergamo. “*Mpando*

wa Satana ndi kumene inu mukukhalako.” Mukumvetsa zimenezo?

⁹⁸ Tsopano, ndi chifukwa chake ine ndikubwerera kuti ndikatenge mbiriyakale iyi kuchokera mu mbiriyakale ya mpingo, kukapeza kumene . . . ku zimene zinachitika pamene Iye anati, “Inu mukukhala kumene kuli mpando wa Satana.”

⁹⁹ Ine ndinaganiza, “Chabwino, kodi kumeneko kungakhale kuti, chinthu chinachake, ‘mpando wa Satana?’” Ndiye ine ndikupeza kuti mfumu yayikulu iyi, itatha kuthawa Aperisia ogonjetsa amene analanda (malingana ndi masomphenya a Daniele), iye anabwera ku mzinda uwu wa Pergamo, ku Roma, ndipo kumeneko anakapanga likulu lake. Satana anasamutsa likulu lake kuchokera ku Babeloni kupita ku Pergamo, komwe (mtsogolo) iye akanadzayambitsa Babeloni watsopano. Oh, mai! Tsopano inu mumvetsetsa maziko pamene ife tiri. Chabwino.

¹⁰⁰ Tsopano, ndipo kumeneko iye anamupha m’bale wodabwitsa uyu, anaphedwa kumeneko, Antipas.

¹⁰¹ Kenako anadzasintha kachitidwe kake. Poyamba iye anali wozunza Akhristu. Oh, momwe ankadanira nacho Chikhristu! Ndipo iye anali wansembe-mfumu iyemwini, wachikunja mwachibadwa ndi nkachitidwe. Kenako iye anasintha kachitidwe kake ndipo anadzaphatikana ndi Konstantine.

¹⁰² Konstantine nthawizonse ankaganiziridwa (ndipo akuterenso ndi papa lero) amene anayambitsa Alupanga a Columbus, tsopano, amene anapereka lumbiriro la magazi lija. Koma Konstantine (ine ndikunena izi molemekeza ndi mwaulemu), mwanjira yanga yowerengera izo mu mbiriyakale, sanatembenezidwe konse.

¹⁰³ Tsopano, iye analota loto usiku wina, kuti ngati iye . . . iye anawona mtanda, ndipo anati ndi iwo iye akanadzapambana nkondoyo; ndipo . . . chifukwa chakuti iye analonjeza zithandizo kwa Akhristu, kuti iye akanadzakhala Mkristu, ngati iwo akanadzamupempherera iye kuti apambane nkondoyo. Ndipo ine ndinaima pafupi ndi mlatho pamenepo, apo pomwe iye . . . kutsidya lina la mlatho wawo, akugona, analota loto ili; ndipo anadzuka, ndipo anajambula mtanda woyera pa zishyango zake ndi za ankhondo ake onse. Ndipo apo ndi pomwe kunakhazikitsidwa Alupanga a Columbus omwe ali pansu pa chipembedzo cha Roma Katolika. Koma iye sanachite konse chinthu chimodzi chachipembedzo; chinthu chokhacho chomwe iye anachita chomwe chinalembedwa konse mu mbiriyakale, monga ine ndinayamba ndachiwonapo, chinali, iye anayika mtanda pamwamba pa St. Sophia Church. (Huh!) Koma iye anali wandale, ndipo pamene iye anadzakhala mfumu ya Roma pa nthawi imeneyo, iye ndi wansembe wachikunja uyu, palimodzi, analimbikitsa ndipo anabweretsamo mpingo wofunda wotchedwa Chinikolai pa nthawi imeneyo. Chikhristu,

chomwe chinkatsamira ku unsembe, ndipo ankazifuna izo mu mpingo wawo, zomwe tinazitenga nkuphunzira kwathu kwamtsogolo kwa mpingo waku Efeso, ndi zina zotero, ndi—ndi wa Smurna; Anikolai amenewo.

¹⁰⁴ Tsopano Anikolai anali atakhala . . . osati “ntchito” monga momwe izo zinaliri kumbuyo kumayambiriro *kuno*, koma *apa* ndi “chiphunzitso.” *Apa* zinali “ntchito,” iwo anali akungoyesera kuti azilowetsemo izo; koma cha *kuno* mu m’badwo wa mpingo wachitatu zinadzakhala “chiphunzitso,” ansembe aakulu, anthu aakulu. Anali asanawatchule iwo mapapa panobe, tsopano; koma iwo ankatchedwa, monga, ma arkbishopu, anthu apamwamba, inu mukudziwa, odziwika. Ndipo chiphunzitso chawo chinali, chinali, chinali chamwambo.

¹⁰⁵ Iwo anali akuchokako ku Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu, wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Iwo anawalola apang’onowo achokepo ndipo anawatcha iwo “ampatuko,” chifukwa iwo samagwirizana nawo iwo kuti akhale ndi zipembedzo zazikulu izi. Koma Mpingo unkafuna kukhala mfulu pansi pa ulamuliro, pansi pa mphamvu ya Mzimu Woyera monga Khristu anawalonjezera iwo; Iye bwenzi akukhala ndi iwo, ndipo ameneyo anali Mfumu yawo. Oh! Mfumu yawo!

¹⁰⁶ Mpingo woona sunasunthepo kachitidwe kake, osati kuti azilamuliridwa ndi gulu lina la—la . . . Ine sindikudziwa zomwe inu mumawatcha iwo kunja uko, makardinolo, ndi mabishopu, ndi mapapa, osalepherawo. Iye timakhulupirira kuti alipo wosalephera Mmodzi, Iye ndi Mfumu yathu, Iye ndi Yesu Khristu nafe tsopano mmawonekedwe a Mzimu Woyera; Mulungu mwa ife, akukhala pakati pathu, akutitsogolera ife ndi kumatilondolera ife ku madzi a Moyo, akudzipangitsa Iyemwini kudziwika; kuwonetsera, monga Iye anachitira pakati pa oyera oyambirira ndi ofera, kuti Iye anali Ambuye Mulungu wa chirengedwe, akuchiritsa odwala, akuukitsa akufa, akuwonetsera masomphenya, kutulutsa ziwanda.

¹⁰⁷ Palibe nthawi imodzi yomwe ine ndingakunkhe kanthu kamodzi, mwa mabishopu onse a mpingo wa Chinikolai omwe anapanga ulamuliro wolowezana wa Roma, papa; palibe nthawi imodzi mu mbiriyakale imene ife tinakhalapo nazo zolembedwa za aliyense wa mabishopu amenewo amene anawukitsapo wakufa, kapena chirichonse chonga chimenecho, chifukwa Khristu (chiukitsiro) sanali mmitima mwawo. Iwo anali atayanjana ndipo anali atatsatira chipembedzo, anagulitsa maufulu awo akubadwa. Koma Mpingo wa Mulungu wamoyo unali nayo mphamvu ya Khristu, mpingo winawo unali nawo olemekezeka mmenemo; koma Mpingo woona unakhala nawo Mzimu. Kodi inu mukumvetsa? Chabwino.

¹⁰⁸ Tsopano izi . . . Chotero Konstantine, kuti aphantikize ufumu wake pamodzi, ndi izi zimene iye anachita. Iye anawatenga

Achinikolai amenewo, ndipo anapita kwa iwo (chimene chinali mawonekedwe a Chikhristu). Kodi inu mukumvetsetsa izo? Iwo anali Akhristu, otchedwa choncho; odzitcha Akhristu, opanda Mzimu Woyera. Oh, ndikukhumba zimenezo zikanalowerera mkati kuchitira kuti inu musadzazilole izo kuti zidzakuthaweni. Mukuona? Iwo anali Akhristu, Akhristu achipembedzo, opanda Mzimu Woyera. Iwo anali Mkhristu mwa dzina, iwo anali Mkhristu mwa kusonkhana kwawo palimodzi, iwo ankadya mgonero, ndipo iwo ankasunga madongosolo; koma, anakana utsogoleri wa Mzimu Woyera. Iwo analibe zizindikiro ndi zodabwitsa pakati pawo, iwo ankadzinenera kuti zinthu zimenezo zinali za mmbuyo; kuti iwo amayenera kukhazikitsa mpingo kuti uzilamulira. Tilowa mu zimenezo mu miniti, ulamuliro wa mtundu wanji. Mukuona?

¹⁰⁹ Tsopano, chotero ndiye Mpingo wa Mzimu Woyera unkayenera kuti Udzitalikitse Wokha kutali ndi zinthu zoterozo. Koma, mu Pergamo, izo zonse zinalemberedwa kwa *mngelo* wa mpingo wa Pergamo. Mukuona? Chifukwa Iwo unali udindo wake tsopano kuchita zimenezo.

¹¹⁰ Koma Konstantine analibe chidwi ndi Chikhristu, iye ankafuna kubweretsa makolo ake achikunja, mpingo wake wachikunja. Ndipo Laodikaya yemwe anzika mizu ndipo. . . kapena Chinikolai chomwe chinali chitazikika ndi kukhazikika ku Roma ndipo chinali chitadziwonetsera mopambana, ndipo anthu ambiri anali okhulupirira Achikhristu (otchedwa), ofunda. Ndipo Mpingo woona unali apang'ono; nthawizonse amatero ndipo nthawizonse akhala ali! Ine ndingodikirira miniti, mulole zimenezo zilowerere mwakuya. Mukuona?

¹¹¹ Kumbukirani, Mpingo woona nthawizonse wakhala kagulu kakang'ono kwambiri kamene kamakankhidwira kunja kwa mipingo ina. Mpingo woona sunazipangepo bungwe, chifukwa iwo si bungwe, ndi Thupi lachinsinsi la Yesu Khristu likukhala moyo pa dziko lapansi, Mzimu Woyera kumayenda mwa mamembala amenewa. Chotero simungamupange bungwe Khristu, inu simungachite zimenezo. Ine ndikufuna kuti inu mugwiritsitse kwa zimenezo kwa M'badwo wa Laodikaya uwo, tsopano. Ndipo mukumbukire zimenezo ndipo muzisunge izo, chifukwa Mawu aliwonse omwe ndimalankhula ali pa tepi iyi. Ndipo tsopano kumbukirani, musunge zimenezo mmalingaliro: Mpingo woona wa Mulungu sunachitepo bungwe.

¹¹² Mpingo wa Katolika ndi bungwe loyamba kudziwika padziko lapansi, sipanakhalepo konse bungwe mmbuyomo, ndipo iwo—iwo ndi “manthu wa mpingo” monga Akatolika amanenera kuti ndi umenewo. Iwo ndi “manthu wa mpingo.” Manthu wa mipingo ya bungwe. Baibulo limanena kuti iye anali, chotero inu simungatsutse zimenezo pamene iwo anena kuti ndiwo “manthu wa mpingo,” iwo ndi “manthu wa mpingo.” Iye

akupezeka mu Chivumbulutso 17, ife tifika kwa iye molunjika. Chabwino.

¹¹³ Tsopano, chotero Konstantine, ali nacho ichi mu malingaliro ake kuti akalimbikitse ufumu wake (monga Roma nthawizonse anakachitira, kuti agwire makiyi a dziko lapansi), iye anawabweretsa malingaliro ake achikunja ndipo anatenga malingaliro Achikristu, ndipo mwanjira ina anawaphatikiza iwo palimodzi, kuti awalumikizitse iwo palimodzi ndi kudzipangira yekha mfumu yomwe singakhale yachiwiri kwa wina aliyense. Mukuona? Chifukwa chakuti iye anali. . . Izo zikanamupangitsa iye kukhala wolamulira wamkulu padziko lapansi, Konstantine.

¹¹⁴ Ndipo tikanena zotembenuka: iye anali—iye anali wandale, koma osati woyera wa Mulungu, monga ena a iwo amayesera kumupanga iye. Iye sanali! Palibe chinthu chimodzi chimene iye anachitapo chomwe chinamveka ngati Chikhristu kwa ine. Chotero pa umodzi wa mipingo ya Chinikolai iye anayikapo mtanda; ndipo tikanena za china chirichonse chimene iye anachitapo chimene chinkawoneka Mwachikhristu, ine sindinachiwone icho konse; kupatula iye. . . usiku uja umene anawajambula iwo pa zishango zake monga *pamenepo*, chifukwa iye anali ndi loto, Akhristu anali kumupempherera iye kuti apambane nkhoodoyo.

¹¹⁵ Tsopano, ndiye zikanalimbikitsa ufumu wake. Ndiyeno kuti achite izi, iye anabweretsamo miyambo yachikunja, mpaka mu mpingo Wachikhristu wa Chinikolai. Ine ndiwutcha iwo mpingo wachipembedzo wofunda womwe umapangika. Iye anabweretsa miyambo yachikunja mu mpingo wa Chinikolai uwu, ndipo uko kunali kubadwa kwa Chikatolika.

¹¹⁶ Tsopano, m'bale, ine ndikubwereza mbiriyakale. Ine ndiri nawo abwenzi masauzande Achikatolika, ndipo iwo ndi abwenzi ochuluka basi monga Achiprotestanti. Koma Achiprotestanti sangakhoze kufuula, ingodikirani mpaka usikuuno ukatha, mwawona. Mukuona? Inu mudzawona kuti iwo anachita chinthu chomwe chomwecho. Mpotu sungakhoze kutcha ketulo “noninoni.” Mwaona, chifukwa ndicho—ndicho chinthu chomwe chomwecho, mzimu womwewo unadzafika pakati pawo. Ndiyeno mudzawona chifukwa chimene ine nthawizonse ndimatsutsana ndi chinthu chimenecho. Chifukwa ndizolakwika! Mzimu kumene mwa ine, ngati ine nditayesera kutero, ndipo chinachake mwa ine chikufuula, Ine sindingathe basi kukhala chete za izi, nthawizonse ndakhala. Iwo amatcha. . .

¹¹⁷ Amuna opambana, atsogoleri opambana achipembedzo anandiuzapo ine, “Iwe uwononga utumiki wako. M'bale Branham, iwe ukuchita zinthu” anati, “iyo—imeneyo si ntchito yako. Mulungu anakuitana iwe kuti uzipempherera odwala.”

118 Mulungu anandiitana ine kuti ndidzachite zoposa kupempherera odwala. Odwala ndi chinthu chimodzi chokha kuti ine ndizikhoza kukopera chidwi cha anthu, ndipo ndizo zonse; odwala, kupempherera odwala ndi chinthu chaching'ono. Mukuona? *Uthengawu* ndi chimene ife tikuchikamba. Zinthu zimenezo zimabwereranso; odwala, munthu, munthu wodwala akhoza kuchiritsidwa ndi kudzafanso. Koma munthu amene wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu amakhala nawo Moyo Wamuyaya. Chotero Mulungu samangopita kukachiritsa odwala monga chomwecho. Mphatso imeneyo imakhala mu mpingo kumene kwa thupi la kumeneko; pa mmodzi, kenako pa mmodzi winayo, ndipo kenako pa mmodzi winayo, kenako pa mmodzi winayo. Mukuona? Kutu, mphatso, zimangodutsa mu mpingo. Koma Izo ndi zoposa zimenezo, ndipo ine ndikuyembekeza kuti inu mukuzimvetisa Zimenezo. Chabwino.

119 Kubadwa kwa Chikatolika, ndi cholinga chakuti adzachite izi, kuti adzagwire ma—maso a Akhristu komanso maso a achikunja, kuti adzawalumikize iwo pamodzi ndi kudzapanga mpingo umodzi.

120 Oh, ine ndikukhumba ndikanakhala nazo izo pakali pano, chidutswa cha pepala winawake anadzaika apa usiku wina. Ine ndimati ndibweretse zimenezo, ndipo ine ndinaiwala izo; muli zinthu zambiri mchipindacho uko. Iwo akuchita chinthu chomwe chomwecho pakali pano, ndipo inu munaziyambitsa izo pamene inu munasankha munthu womaliza yemwe inu munamusankha. Iwo akugwira ntchito tsopano kuti apeze ngakhale Baibulo limene silingawapweteke Akatolika, kapena Myuda, kapena Achiprotestanti. Awapangira iwo Baibulo limene lidzagwirizane ndi chinthu chonsecho. Kodi inu simukuwona kuthyathyalika kwa Konstantine wina? Mbiriyakale ikungodzibwereza mobwereza. Tsopano, inu mukuwona, ndipo ine ndiri ndi... Inu munandimva ine ndikuwerenga izo usiku wina, sichoncho inu? Ndipo ine—ine ndiri nazo izo kunyumba, ndipo iwo akhala akugwira ntchito pa izo kwanthawi yayitali.

121 Tsopano iwo amati, “Mu '62 iwo adzatero...” Ndipo zindikirani kuti Papa Yohane XXII wabwera i-... wapempha mipingo yaing'ono ing'ono yonse kuti ibwerere ku anthu wa mpingo. Musadandaule, iye atero. Iwo adzatero! Iye akupita, iwo abwerera kale. Iwo sakusowa kubwerera mmbuyo, iwo ali kale kumeneko tsopano.

122 Monga ine ndimanenera, “Dziko lino linati, ‘Chabwino, ngati Bambo Kennedy asankhidwa, Akatolika adzalanda ulamuliro.’” Kulanda ulamuliro? Iwo anachita kale zimenezo kalekale, ndipo inu simunadziwe kanthu za izo. Nndani amalipira aphunzitsi awo? Kodi amapanga bwanji kuti zinthu izi zipite ku sukulu zawo, ndi kumakaphunzitsa Chikatolika msukuluzo? Ndipo inu okhomera msonkho nkumalipira izo. Oh,

pansi kumene pa mphuno yanu, mwawona, monga choncho. Oh, mai, momwe iye ankagwirira ntchito! Ndipo Baibulo linati iye akanadzatenga mwachinyengo, ndipo iye anatero; mwaona, uko nkulondola; mwaona, kumalipira misonkho popanda kalikonse. Chotero, oh, pali zambiri zomwe zingathe kunenedwa apa. Ine ndikungoyenera ndidukire pamalo amenewo, ndi kudzabwereranso kuti ndidzazitolenso.

¹²³ Pofuna kuti chinthu ichi chizigwira ntchito, Konstantine anakhazikitsa zisangalalo zambiri zachidziko kuti akakope chidwi cha awiri onse achikunja komanso Akhristu kukalowa mu mpingo. Kodi ndinu a malingaliro auzimu? Kodi inu mukuganiza? Kodi umenewo si Uthenga wa Ora? Mpingo uli ndi masewera a buncu, maphwando, amapatsana magalimoto, kuti angowasakaniza iwo pamodzi, kulumikizitsa mphamvu imeneyo kuti ibwerere pamodzi kufika pakuti adzathe kupeza malo ochitira zinthu, pomwe pano.

¹²⁴ Tsopano, imeneyo ndi mbiriyakale, winawake alibe—alibe nkhwangwa kuti agayire, iwo akungonena zimene zinachitika. Koma iye anachita zimenezo, anawulumikiza mpingo pamodzi pokhala ndi zisangalalo za chidziko, kuti akawubweretse pamodzi mpingo wa Chinikolai. Tsopano kumbukirani, iye sakanakhoza kuwukhudza Mpingo wobadwa-kachiwiri uwo. Ayi, bwana, palibe aliyense wa iwo. Koma mpingo wofunda wa Chinikolai unatsatira zimenezo.

¹²⁵ Ndipo kodi ife tiri ndi chiyani mmatchalitchi athu Achiprotestanti? Maphwando a msuzi, zisangalalo, masewera olimbitsa thupi, (Oh, mai!) kugulitsa nsaza, ndi china chirichonse, mwawona. Tsopano, inu mukudziwa kuti izo ndi zoono. Chabwino, tsopano, ngati awo—ngati awo ndi Mawu a Mulungu, abwenzi, ndi Choonadi. Ndipo mipingo yonse ya Chiprotestanti ili yolakwa! Mukuona?

¹²⁶ Tsopano, silinakhalepo dongosolo la Mulungu ku—kukhala ndi mamphwando a msuzi ndi zovina mzipinda zapansi, ndi zonse zomwe zikuchitikazo, kuwalipira abusa ndi zinthuzo. Ngati anthu akanangophunzitsidwa kuti azipereka zakhumi zawo, izo zikanakhala zonse zomwe zikanakhalako kwa izo. Ndiro dongosolo la Mulungu. Koma Mulungu ali nalo dongosolo, koma munthu amafuna kupanga dongosolo lakelake, kumapanga haibulidi dongosolo la Mulungu. Chabwino.

¹²⁷ Tsopano, pochita izi, iwo anaphatikizana ndipo anapanga woyambirira . . . anayambitsa mpingo woyambirira wa Katolika, mtsogolo. Ndiye pa Nicene Council yoyambirira . . . Pamene ine ndinawerenga zimenezo, ine ndinangogwa pa mawondo anga. Bungwe lalikulu la Nicene linali litachitika mu A.D. 325, onse a iwo anasonkhanitsidwa pamodzi, mabishopu ndi abambo a chikhulupiriro cha Chikhristu anasonkhanitsidwa pamodzi ku Nicaea. Ndi chifukwa chake amatchedwa Nicaea Council, mu

A.D. 325. Ndipo pafupifupi nthumwi fifitini handiredi zinabwera ku—ku—ku msonkhano, kapena khonsolo, pafupifupi nthumwi fifitini handiredi, ndipo anthu wamba anaposa mabishopu faivi kwa mmodzi (mwa nthumwizo); komabe, kudzera mu Chinikolai (mawonekedwe ozizira) ndi dongosolo la ndale za Konstantine, iwo anavota kuwuposa Mpingo woona ndipo anapambana chigonjetso, ndipo analowetsamo mabishopu ndi dongosolo loyera la amuna; kuwuchotsa—Mzimu Woyera kuchokera mu msonkhano, ndi kuziyika izo pa mabishopu, makadinoro, ndi mapapa, ndi ena otero.

¹²⁸ Kachitidwe komweko ka utambwali kamene chipani cha Democrat chinachita mu chinthu chotsiriza ichi! Tsopano, uko nkulondola. Tsopano, ife sitiri...ine ndikufuna... Ndipo a Republican angakhale nawonso otsika-pansi. Koma ine ndikuyankhula za chinthu chimodzi chimene iwo anachitsimikizira (Edgar Hoover) mu California, ndi malo ena ambiri: iwo anali ndi makina ovotera amenewo omwe adayikidwa komwe ungavotere Bambo Nixon, iwe umayenera kuvotera—Kennedy pa nthawi yomweyo. Iye analibe mwayi. Chabwino, tsopano zimenezo iwo atsimikizira kuti izo “nzolakwika,” ndiye bwanji iwo sakuchitapo kanthu za izo? Ife tikukhala mu ora, ndi zimenezo, ife tiri mu nthawi yotsiriza. Iwo akudziwa zimenezo, iwo anatsimikizira kuti iwo anali atambwali, ndipo tsopano iwo sachita kalikonse ka izo.

¹²⁹ Icho chinali chovala cha utambwali kumbuyo uko, ndipo apa pali kubadwa kwake kwachiwiri: kuti amulowetsemo munthu wina, kuti atenge chiphunzitso china; Chiphunzitso cha Chinikolai, chimene nthawiyina chinangokhala—*zintchito*, tsopano icho chadzakhala “chiphunzitso.” Mmasiku a Al Smith zinali ntchito, koma tsopano ndi “chiphunzitso.” Uh-huh, uh-huh. Tsopano izo ziri pano, ziri pa ife. “Oh, iye adzamupanga wodziwika kukhala purezidenti,” palibepo kukaikira za izo mmalingaliro mwanga; ndithudi, pa teremu yotsatira imeneyo, mpaka iye atakhoza kudziphatikizamo, atawaphatikiza achikunja awa ndi owoneka ngati Akhristu pamodzi.

¹³⁰ Iwo akugwira ntchito pa Mabaibulo, kuti ayesetse kuwabweretsa iwo pamodzi, mapapa, makadinoro. Bishopu wamkulu waku England, bishopu wamkulu wa ku Canterbury, ine ndinakumana naye iye, ndinagwirana naye chanza, ndinayankhulana naye, inemwini, pamene ine ndinali mu England; masokosi pafupifupi kumafika mchiuno mwake, ndipo (Oh!) wokhala ngati munthu wovala-moseketsa. Koma iye anapita kukamuhezera papa, nthawi yoyamba imene iwo anadzachezera kwa zaka mahandiredi ambiri. Ndi chiyani chimenecho? Ife tiri pa ora lomaliza!

¹³¹ Ndi chifukwa chake ine ndaima pano usikuuno mmalo mokhala kunja kuno pa nsanja kwinakwakenso kuyesetsa

kuti ndilalikire ndi kupempherera odwala. Ndipo ine sindingathe kukumana nawo onse pa nsanja (mauthenga awa mobwerezabwereza), ndipo ndi chifukwa chake ife tikuziika Izo pa tepi ndi kuzitumiza Izo ku dziko, iwo akakhoze kuchenjezedwa ndi kubwerera ku Chikhulupiriro.

¹³² Ngakhale kumapeto kwa m’badwo wa Chikhristu, Yuda, Bukhu la Chivumbulutso lisanalembedwe; Yuda Woyera, ayenera kuti anali m’bale (m’bale womulera) wa Yesu, anati, “Ine ndikufuna kuti inu mulimbanirane modzipereka Chikhulupiriro chomwe chinaperekedwa kamodzi kwa oyera.” Iwo anayamba kuchokako kwa icho ndiye, itachitika imfa ya Ambuye Yesu. Ndipo tsopano ndikutali bwanji usikuuno? Mwawona.

¹³³ Tsopano, Nicene Council yoyamba iyi, ndipo inali mu A.D. 330..325. Pafupifupi nthumwi fiftini handiredi ndi mabishopu anakhala nawo pa msonkhanowo, koma anawagonjetsa iwo, mu khonsolo yaukali, ya mkuntho yomwe inachitika. Ndipo iwo anawalamulira iwo, ndipo anavotera mmenemo kuti Chinikolai chizilamulira, ndipo zimenezo zimayenera kutenga..mpingo wonse, ndi kuwuyika iwo pansi pa kuyang’aniridwa ndi mapapa kapena—kapena mabishopu, kapena chinachake; kuchotsa mphamvu kuchokera ku Mpingo ndikukaipereka iyo kwa mabishopu, kuti mabishopu azilamulira Mpingo ndipo amodzi okhawa womwe anali ndi chirichonse chonena cha Iwo.

¹³⁴ Kodi inu munazindikira mu mpingo wa Katolika lero? “Inu simungawerenge Baibulo limenelo, si za inu kuti mutanthauzire. Ameneyo ndi bishopu.” Mukuwona kumene izo zinachokera? Tsopano inu mukhoza kuwona chimene Chinikolai chinali kwenikweni iwo asanayambe kukuwa ndi kukwawa. Ichu chinabadwira pomwepo. Izo nzowona. Ndipo icho chinali mawonekedwe a Chikhristu; chikadalibe!

¹³⁵ Ndipo ndiyeno Chiprotestanti chikufanana ndi zimenezo. Baibulo, mu Chivumbulutso 17, linati, “Mayi ndi ana aakazi.” Ife tifika kwa izo pakadutsa kanthawi, Ambuye akalola. Tsopano inu mukuzindikira kuti ndi chimodzimodzi lero, iwo analanda ulamuliro. Tsopano, Konstantine anagwiritsa ntchito kachitidwe ka Balaamu.

¹³⁶ Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muyesere kumvetsera mwatcheru momwe inu mungathere. Tsopano, Iye ananena apa, mu Baibulo apa, “Gwiritsitsani chikhulupiriro Changa.” Tsopano:

...ndiri nazo zinthu pang’ono zokutsutsa iwe, chifukwa uli nazo... iwe... chifukwa iwe uli nawo iwo kumeneko... (osati awa apa, koma kumeneko; iwo ali nawo iwo, “muli nawo iwo mu—mu mpingo wa Pergamo,” mwawona) ... akugwirizira chiphunzitsocho—chiphunzitso cha Balamu, yemwe

anaphunzitsa Balaki kuti akayike chopunthwitsa pamaso pa ana a Israeli, kukadya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano, ndi kukachita ziwerewere.

¹³⁷ Tsopano, Konstantini anagwiritsa ntchito kachitidwe komweko kamene Balamu anakagwiritsa ntchito. Iwo anali ndi msonkhano utatha msonkhano wa khonsolo uwu kuno kuti mabishopu anayikidwa kuti aziyang'anira mipingo, ndi zina zotero, kuti aziyilamulira iyo, ndi kutenga mphamvu zonse kuchokera kwa anthu wamba, "Ndipo iwo analibe kulingalira kwa iwo okha, komanso iwo analibe ufulu wotanthauzira Malemba." Ndipo kuti zonsezo zinali za kwa ansembe, ndi omwe azichita kutanthauzira kwa Malemba.

¹³⁸ Potsiriza, patapita kanthawi, iwo anapanga *mbuye* wansembe, ndipo iwo... wolowa mmalo, yemwe anali papa. Koma tsopano iwo afika pamalo pomwe ayika izo, "konse—kumvetsetsa ndi kwa wansembe, ndipo osonkhana sakuyenera kuti aziwerenga Baibulo, iwo sakuyenera kuti azichita kalikonse;" ndipo, moona, iwo... Baibulo linachotsedwa kwa iwo. Ndipo tsopano iwo—iwo adzitengera izo zonse pa iwo okha ndipo izo zinavoteredwa kwa ife chifukwa izo zinkawoneka zabwino.

¹³⁹ Izo zinkawoneka zabwino chifukwa iwo anali olemera, ndi zina zotero, ndipo iye anapereka... Pa msonkhano waukulu uwu, pamene iye anawaitanitsa pamodzi, Konstantine anawapatsa mabishopu nyumba zabwino; iye anapeza ndalama zina ndi—ndi malo aakulu onse awa... monga nyumba, iye anazipereka izi ku tchalitchi, kuti azitha kuzigwiritsa ntchito monga—monga nyumba za tchalitchi. Oh, izo zinali nyumba zabwino, onse atavekedwa, ndi zina zotero, chotero iye anazipereka izo ku tchalitchi.

¹⁴⁰ Pambali pa zimenezo, iye anawaveka mabishopu awa ndi miinjiro yayikulu kwambiri, ndi malaya amkati ndi zinthu pansi pake. Ndipo pambali pa zimenezo, iye anawaika iwo pamwamba pa... kapena anamanga malo okwera monga awa, ndi kukawaika iwo pamenepo ngati fano. Ndipo mmusi mwake iye anapanganso maguwa a nsangalabwi, pansi pake. Ndipo iye anachita kutembenuza konse uku, kuchokera ku lingaliro lachikunja, uko, ndi kubweretsa Chikhristu mmenemo pomutenga bishopu wawo. Mwawona, iwo anangotsitsira pansi fanolo ndi kudzamukhazikapo bishopu. Mwawona, kumupangira iye guwa, chinthu chomwe chomwecho, ndi kumupanga iye mulungu. Anadzamuikapo bishopu, ndipo iye anali ndi zonena-zonse, anadzamuveka iye zonse ndi kumupanga iye kuti aziwoneka ngati mulungu. Mmalomomuwina iye ngati milungu yawo yachikunja, iwo anamuveka iye mwinjira ngati womwe Yesu ankavala. Mukuona? Ndipo iwo anamupanga iye kumangowoneka ngati fano atakhala pamenepo.

¹⁴¹ Oh, inu mukhoza kulingalira momwe wachikunja ananenera, “Chabwino, ine ndikhoza kutsatira zimenezo, pali winawake yemwe akhoza kutiyankhulanso ife. Ife takhala tikuyankhula kwa fano, koma munthu uyu akhoza kuyankhulanso kwa ife.”

¹⁴² Momwe Akhristu ankaganizira, “Chabwino, zimenezo ndi zabwino basi. Tsopano ife tikhoza kuchita chirichonse chimene tikuchifuna chifukwa pamenepo pali mulungu wathu. Ife basi tikhoza...Ife tikhoza kuyankhula naye iye, iye akhoza kutiwuzanso ife zoti tichite. Ngati ife tichimwa, ife tizimuwaza iye za zimenezo, tizimupatsa iye kanthu kenakake, kakang’ono...tizichita kudzitunduza pang’ono kapena chinachake; ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, ife tizikhala bwino bwino, ndipo tizibwereranso ndi kumakakhala momasukanso kachiwiri. Osasowa kudandaula za chirichonse.”

¹⁴³ “Oh, zimenezo zinkawoneka zabwino.” Ndithudi! Izo zikuchitabe zomwezo kwa malingaliro athupi, koma inu simungamuuze zimenezo mwana wobadwa mwatsopano wa Mulungu. Iwo sanayambe achitapo zimenezo. Pakuti iye amadziwa Yemwe iye wamukhulupirira ndipo ndi wokakamizidwa kuti Iye ndi wokhoza kusunga zomwe zaperekedwa kwa Iye pa tsiku limenelo. Ndipo poyiwala zinthu zimene ziri mmbuyo, ife timakakamira kuloza ku maitanidwe apamwamba mwa Khristu. Ameni! Oh, momwe ine ndiriri wothokoza!

¹⁴⁴ Guwa la nsangalabwi pansi pake, atakhala pamwamba apa, atavala kwenikweni, mpingo wabwino. Oh, mai, iwo onse anali atakonzedwa. Chabwino. Ndipo guwa ili linali litakutidwa, guwa la nsangalabwi ili, lokongola. Inu muyenera kuwawona iwo apabe, chinthu chomwe chomwecho. Litakutiridwa ndi golide, ndi kukongoletsedwa ndi miyala yamtengo, ngale mu guwa ili. Zokongola! Zinali zoyenera kwambiri kwa Achinikolai ndi kwa achikunja. Mukuona zomwe iye anachita? Iye anatenga miyambo yachikunja, malingaliro achikunja; ndipo anatenga Chikhristu, mawonekedwe ozizira omwe samadziwa chabwino chirichonse, analibe Mzimu Woyera kuti uziwatsogolera iwo mosiyana; ndipo anawapangira iwo mulungu pansi pano, ndipo anawapangira iwo guwa lansembe, ndi mulungu woti azikhala pamenepo kuti azikhululukira machimo awo. Kodi ndinu auzimu? Kodi inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? Mukuona chomwe icho chiri? Kupereka chikhululukiro cha tchimo padziko lapansi.

¹⁴⁵ Ine sindikunena zimenezo kuchokera mmalingaliro mwanga, imeneyo ndi mbiriyakale. Ndikupatsani inu tsamba ndi nambala ya mbiriyakale yopatulika, chimodzimidzi momwe ine ndingakuuzireni inu za George Washington, ndi Abraham Lincoln, ndi Nkhondo ya Gettysburg, ndi zina zotero. Ndithudi, zinthu zonsezo ndi mbiriyakale yomwe ine ndikubwereza pano.

¹⁴⁶ Tsopano, ndiye izo zinali zowayenera kwambiri kwa... osati kwa Mpingo wobadwa mwatsopano uwu. Ayi, bwana! Chabwino, pamene iwo anamuyika munthu kumtunda uko tsopano, kuti akhale bishopu wamkulu, kuti azibwereza miyambo, kunena moona zimenezo zinawapangitsa a Full Gospel kuchoka kwa izo. Izo zikuchitikabe lero. Mibadwo imeneyo ikungopitirizidwa, kumangolowelerana, mwawona; mawonekedwe ena, tsiku lina. Oh, pamene iwo anayikamo wolemekezeka kumtunda uko ngati mulungu, ndipo amanena miyambo pang'ono.

¹⁴⁷ Ndipo zindikirani kuti achikunja ankapemphera kwa makolo awo omwe anafa. Ndipo mpingo wa Chiprotestanti womwe ungayimirire ndikuti, "Ine ndimakhulupirira Mpingo Woyera wa Roma Katolika komanso kuyankhulana ndi oyera." Inu Amethodisti mumabisa nkhope yanu, Apresbateria, ndi Achilutera. Chirichonse chomwe chimapembedzera ndi akufa ndi zamizimu! Ndithudi. Koma, tsopano, Achiprotestanti sangathe kuwaseka Akatolika, iye amachita chinthu chomwe chomwecho, amapanga kuvomereza kokwanira-konse uku kuti iye amakhulupirira chinthu chomwe chomwecho; kubatizidwanso kubwerera mu mpingo wa Katolika mwa ubatizo wake wa mmadzi, kukana ndi kunyoza anthu omwe amayesa kukhala moyo woyenera; akapita ku tchalitchi ndipo akawawona anthu akufuula pansu pa mphamvu ya Mulungu, amaimirira panja ndi kumaseka Iwo. Zonsezo.

¹⁴⁸ Mwaona, mizimu siimafa; anthu zimatheka, koma osati mizimu. Mukuona? Mzimu Woyera, Iwo sungakhoze kufa. Zinali pa Yesu, tsopano Ziri mu Mpingo Wake; nthawizonse zidzakhala mpaka Iye atadza *kwa* Mpingo Wake, chifukwa Iwo ndi gawo la Iye. Mukuona? Ngakhale ozunza, iwo—iwo ankawaselewula iwo kumbuyo uko mu tsiku limenelo, iwo akukhalabe moyo kuno lero. Mulungu amachotsapo munthu Wake koma osati Mzimu Wake pa dziko lapansi. Mdierekezi amachotsapo munthu wake koma osati mzimu kuwuchotsa pa dziko.

¹⁴⁹ Ansembe aja omwe anavomereza kuti Yesu aphedwe, omwe anati Iye ndi "wambwebwe," kapena "mdierekezi," anthu amenewo anali achipembedzo munga achipembedzo onse angakhalire. Uko nkulondola. Iwo ankalidziwa Lemba limenelo mwa zolembedwa, koma iwo sankadziwa kutanthauzira kowona kwa Ilo. Iwo anali ndi lingaliro lawo lawo, ndipo sakanamvetsera kwa china chirichonse. Ndiyeno iwo anamuwona Iye ndipo anadziwa...Iwo angalephere bwanji kuwona kuti Yesu sanayenere zonse zomwe mneneri aliyense ananena za Iye? Koma iwo anali akhungu. Ndipo Mulungu anati Iye anawachititsa khungu maso awo ndi cholinga, kuti ife tidzakhale nawo mwayi wa chipulumutso.

¹⁵⁰ Tsopano Baibulo linaneneratu kuti Iye adza...kuti ife tiri mu M'badwo uwu wa Chipentekoste, ndi "wamaliseche,

womvetsa chisoni, wakhungu, ndipo sakudziwa izo.” Ndi chimenecho chikhalidwe cha mpingo, Filadelfia. Oh, inu Abaptisti amwambo, Apresbateria, ndi Achipentekoste! Mwawona, ndi zimenezotu. Nthawizina ine sinditanthauza zimenezo kwa inu mwakhala apa; Ine ndiri pa tepi, inu mukuwona, ndipo ine ndikudziwa komwe iyo ikupita. Mukuona? Lapani! Mubwerere ku Baibulo! Mubwerere kwa Khristu!

¹⁵¹ Chabwino, koma izo ndi zomwe zinachitika, Uthenga Wathunthu unakankhidwira panja. Zizindikiro ndi zodabwitsa mu tchalitchi zinathetsedwamo, ndipo pamene gulu la Mzimu Woyera linachotsedwa pakati pa enawo, ndiye iwo anakana kuti linakhalapo tsiku la zoterozo. Ndipo zinali pamenepo. . . Ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho lero! Ndizo ndendende. Kodi inu simukuwona mzimu wa izo? Monga ine ndinakuwuzirani inu; pachiyambi, muvale maganizidwe anu auzimu, mumulole Mulungu atsegule mtima wanu. Musakhale oweruziratu, mukhale ndi kumvetsera; muziti, “Mzimu Woyera, ndiwululireni ine. Ine ndikuziwona izo, ndi izo pamenepo.”

¹⁵² Miyambo. Kuti? Abaptisti, Apresbateria, ngakhale Achipentekoste, amangokhala mwambo wachipembedzo. Chinthu chokhacho chimene iwo amachita ndi kumenya limba, *chinachake chimzake*, amalumphu lumpha kwakanthawi; ndipo mwamsanga limba likangosiya: *Bruuuu!* Amapita panja, kukabera, kukaba, kukanama, china chirichonse. Koma weniweni. . . Ndi mkwiyo wokwanira wolimbana ndi macheka, kuyankhula za aliyense ndi chirichonse. Mukuona? Ndi zimenezotu. Osati kokha a Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Akatolika, koma mpingo wa Chipentekoste mu M’badwo wa Laodikaya kuno.

¹⁵³ Oh, bwanji inu simukubwerera ku zomwe makolo anu anali nazo? Chifukwa chiyani ife sitikubwerera ku chipentekoste chenicheni chimene chimayeretsa ndi kudzaza ndi Mzimu Woyera, zomwe zimabweretsa Khristu kwa ife? Ndicho chimene ife tikuchisowa. Chabwino. Tsopano, zomwezo lero!

¹⁵⁴ Tsopano, mawu akuti *Pergamo* amatanthauza “wokwatira.” Mawu kumene akuti *Pergamo* amatanthauza “wokwatira.” Chikhristu, imeneyo ndi mbali ya Achinikolai, mbali yofunda, yokwatirana ndi boma, ndi miyambo yachikunja. Zikondwerero zachikunja! Ndipo uko kunali kubadwa kwa mpingo wa Katolika mu tsiku limenelo.

¹⁵⁵ Tsopano, aliyense akudziwa kuti mpingo wa Katolika unabadwitsidwa ku Nicene Council. Zisanachitike zimenezo, iwo unkatchedwa *Chinikolai* ndi Mulungu, zomwe zimatanthauza “nikao,” *nikao*, “kugonjetsa,” kugonjetsa, kapena kuwalanda anthu wamba. Ndipo pamene iwo anachita zimenezo, iwo sanafune Mzimu pakati pa anthu, ndipo

azibusa, zomwe zimatanthauza “olishya,” kuti aziwulola Mzimu Woyera . . .

¹⁵⁶ Inu mukuti, “Bwanji, kodi wansembe sangakhale m’busa?” Kodi akukudyetsani chakudya chotani? Kodi mukumalandira zotsatira zomwezo zomwe iwo anali nazo, pa Tsiku la Pentekoste? Ndithudi ayi! “Tikuoneni Maria,” ndani anaziwona zimenezo pa Pentekoste? Kudzitunduza, kukonkha konse uku, kutsanulira, kugwiritsa ntchito Mulungu wapatatu (“Atate, Mwana, Mzimu Woyera”), kodi inu mumazipeza kuti zimenezo pa Pentekoste? Yesu anati, “Mulole nyumba ya Israeli idziwe ndithudi, Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, amene inu munampachika, zonse Ambuye ndi Khristu.” Uko nkulondola. Kodi zinthu zimenezo timazitenga kuti? Ndi Chinikolai kuyamba ndi kuyamba, ndipo zinapanga Chikatolika.

¹⁵⁷ Tsopano inu mukuti, “Chabwino, ndine wotsimikiza kuti ine sindiri pakati pawo.” Tsopano musakhale otsimikiza kwambiri. Mukuona? Tsopano kumbukirani: Chikhristu, Chinikolai. Tsopano kodi inu mukuimvetsa nkhaniyo? Mvetserani mwacheru ife tisanapite patali. Ine ndikufuna kuti inu mumvetsetse izo ngati ife titi tikhale pano mpaka pakati pausiku. Chotero, uh-hum . . . chotero . . . chifukwa, m’bale, ndi moyo wanu! Inu mukhoza kunena kuti, “Chabwino, ndine wa . . .” Izo ziribe—izo sindizo. Ngati inu mulibe Mzimu Woyera, m’bale, ine sindikusamala kuti ndinu membala wa mipingo ingati, inu mwatayika. Ngati inu simunabadwense kachiwiri ndi Mzimu wa Mulungu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, inu mwatayika; chifukwa inu mulibe Moyo Wamuyaya, ndipo Moyo Wamuyaya ndi chinthu chokhacho chimene Mulungu ati adzachiwukitse, chifukwa Ndiwo moyo wokhawo umene watsalira.

¹⁵⁸ Ngati njere ya chimanga . . . monga ine ndanenera apa, Ora la Zaulimi. Ndi angati akumukumbukira M’bale Spurgeon wachikulire, mlaliki wa Methodisti uko ku Henryville? Munthu wodabwitsa wabwino. Ife tinali titakhala popangira ice cream ku Red Furnish, tsiku lina, tikudya ice cream; ndipo ife tinali kuyankhula za msonkhano umene ine ndinali nawo kumtunda kumeneko, ndipo Ora la Zaulimi linali likuchitika. Ndipo Red anali ndi—ndi sipika yaing’ono itayatsidwa, ndi wa . . . walesi yake itakhala panja apo. Ndipo kwinakwake anali akuyankhula . . . chifukwa uthengawo unali ukubwera kuchokera ku Louisville. Koma 4-H Club inali—inali ndi makina omwe amakhoza kutulutsa njere ya chimanga yomwe iwo amakhoza kuyikamo calcium, ndi mafuta, ndi chirichonse mu chimangacho, ndi kuchipangitsa icho kuwoneka chimodzimidzi basi ngati kuti icho chinapangidwa kuchokera ku . . .

¹⁵⁹ A 4-H inali nazo, sayansi inapangitsa kuti chimangacho chiziwoneka chenicheni kwambiri kuti inu mukhoza kutenga chodzaza mdzanja kuchokera mthumba cholimidwa mmunda,

chodzaza mdzanja kuchokera mthumba lomwe makina apanga, ndipo ichi cha apa (chomwe makinawo apanga) chikhoza kupanga mtundu womwewo wa konifulekisi, mkate wa chimanga. Ndipo inu mukhoza kuzitengera izo koyezera ndi kukazidula izo pakati, mbewuzo, ndipo inu simungakhoze kusiyanita ina kwa imzakeyo. Zimakhala ndi kuchuluka kofanana kwa mafuta, kuchuluka—kuchuluka kofanana kwa calcium, ndi—ndi chinyezi; zonse zomwe zinalowa mu njere imodzi, zinalinso mwa inayo.

¹⁶⁰ Iye anati, “Njira yokhayo yotsimikizika yodziwira yomwe inamera mmunda, ndipo yomwe inapangidwa ndi makina: kwirirani zodzaza mmanja zonsezo. Ndipo ziwiri zonsezo zivunda, ndipo imene inapangidwa ndi makina siingakhoze kutulukanso; koma imene Mulungu anabzala, inadzalanso moyo.” Chifukwa chiyani? Chifukwa iyo siinameretsedwe.

¹⁶¹ Ndipo inu mukhoza kumawoneka ngati Mkhristu, kumachita ngati Mkhristu, ndi kumachita ntchito yabwino iliyonse yomwe inu mungakhoze kuchita, ndi kumakhala mokhulupirika ku mpingo wanu; koma pokhapokha inu mutameretsedwa ndi Mzimu Woyera, Moyo wa Mulungu, Moyo Wamuyaya ukubwera mwa inu; osati mwa kuvomereza, koma mwa *mphatso* ya Mzimu Woyera. Kodi inu mumawulandira chotani Iwo? Adotolo anati, pa Tsiku la Pentekoste, amene analemba ndondomeko yake, “Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo inu mudzalandira *mphatso* ya Mzimu Woyera.” *Mphatso* ya Mzimu Woyera, umene uli Moyo Wamuyaya. Ndicho chinthu chokhacho chimene Mulungu adzachiukitse. Ndi chinthu chokhacho chomwe chiri ndi Moyo chimene Iye angakhoze kuchidzutsa. Mukuona? Ndicho chinthu chokhacho chimene chingapite. Ine ndikukhulupirira kuti zikumveka. Mulungu azipangitse kuti zimveke.

¹⁶² Tsopano, Achinikolai nthawi imeneyo anali ndi mbali yofunda, ndipo anakwatirana ndi mpingo wachikunja; anabweretsamo maguwa achikunja, amapanga maguwa Achikhristu; anabweretsamo mulungu wachikunja, ndipo amamupangitsa iye kumayankhula ndi kulankhula, mmawonekedwe a bishopu. Anakhala pamwamba pamenepo, anamuveka iye mwinjiro ndi ndi kumupanga iye aziwoneka ngati mulungu. Inu mukuona? Si zomwe ziri kunja, ndi zomwe ziri mkati. Mbewu ziwirizo zinkawoneka chimodzimidzi; sizinali zomwe zinali kunja, zinali zomwe zinali mkati. Onani, chamkaticho, Moyo. Chabwino, zinapangidwa mmenemo, ndipo amenewo anali malo obadwira a tchalitchi choyambirira cha Katolika, chinali manthu wa mipingo ya zipembedzo zonse.

¹⁶³ Tsopano inu mukuti, “Chabwino, ine. . . M'bale Branham, ndiye bola ngati ine sindiri wa Katolika.”

164 Tsopano, miniti imodzi yokha, tiyeni tiime apa mphindi chabe, ndisanaiwale. Ndipo tiyeni—ife titembenezire tsopano ku Chivumbulutso, mutu wa 17, miniti yokha. Ndagotembenezira molunjika pamenepo. Tsopano, ili ndi vumbulutso la chiyani? Yesu Khristu, kwa mipingo Yake. Pamene ine ndikuwerenga, mvetserani mwacheru:

Ndipo apo anadza mmodzi wa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale seveni, ndipo anayankhula ndi ine, kuti. . . Bwerani kuno; ndipo ine ndidzakuwonetsa. . . iwe chiweruzo cha hule lalikululu lomwe likukhala pamadzi ambiri:

165 Tsopano, kuchitira kuti ine ndikhale ndi mboni, ndi angati akudziwa kuti *mkazi* mu Baibulo, nthawi iliyonse yomwe waperekedwa monga chopsiyipsyiritsa, zimatanthauza “mpingo”? Chabwino. Ndi angati akudziwa kuti wamkulu “hule,” pomwe pano mu mutu womwewo, ndi “mzinda womwe wakhazikika pamapiri asanu ndi awiri”? Chabwino.

166 Ndipo tsopano ndi angati akudziwa kuti Baibulo linati “madzi”? Apa iye wakhala pa “madzi ambiri”; osati *madzi*, koma “madzi ambiri.” Ndipo *madzi ambiri* amatanthauza “anthu.” Bwanji, tengani mutu wa 15, inu mukhoza kuwona apa, onani, ndime ya 15, onani:

Ndipo iye anati kwa ine, Madzi ambiri amene iwe unawawonawo, kumene hule akukhalako, ndi anthu. . . makamu. . . mafuko, ndi zinenero. (Mukuona? Mukuona?)

167 Tsopano, mkazi uyu anali wachinyengo. Sichoncho iye? Tsopano uku ndi kuphunzitsa, chotero muyenera kusiya kumbuyo chikumbumtima chanu tsopano. Mukuona? Kodi mkazi woyipa ameneyo amatchedwa chiyani “hule”? Ndi mkazi yemwe sali wowona pa lumbiriro lake la chikwati. Tsopano mpingo, mpingo wa Katolika, umadzinenera kuti ndi Mkwatibwi ndi Mkazi wa Khristu. Ngakhale manani amameta tsitsi lawo, ndipo samakhala ndi zokonda, “zokonda zawo zonse kwa Khristu.” Nkulondola uko? Ndithudi. Kapena aliyense. . .

168 Ine ndimachokera ku maziko a Chikatolika, mwaona. Ine ndiri nalo lawo la *Facts Of Our Faith*, ndi mabukhu awo; ndi Achiprotestanti anu, ndi Abaptisti, ndi chirichonse chimene inu mumakhulupirira; mmenemo mowerengera mwanga. Chotero, ine ndimaziwerenga izo chomwecho ngati wina anena chirichonse. “Wawuu!” Ine ndikhoza kuikira kumbuyo zonena zanu. Mukuona? Chotero, ora lafika kuti Izi zipite kunja.

169 Tsopano, chinthu choyamba, Mulungu anayenera kusuntha kudutsa fukoli, kuwonetsa zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwitsa, kuti anthu akhoze kudziwa. Nkhosa za Mulungu zimadziwa Liwu Lake, izo zimadziwa, izo zimadziwa ndendende. Inu muyenera kupeza choyamba. . .

Inu mumatuluka kunja popanda kukhala odziwika, ndiye inu basi. . . Kodi inu mumachita chiyani? Inu mumawavulaza iwo kwambiri kuposa kale. Lolani izo. . . inu mumulole Mulungu azisamalira zimenezo. Mukuona?

¹⁷⁰ “Ine ndikusonyeza iwe chiweruzo cha hule lalikulu.” Tsopano, ngati iye anali chimenecho, ndiye kuti iye anali mkazi wodzinenera kuti ali chinachake chimene. . . Iye anali kuchita chigololo! Nkulondola uko? Chabwino, ndiye, ngati uwo unali mpingo, iye anali kuchita chigololo molakwira Mulungu. Nkulondola uko? Ndiye chigololo, chingakhale ziwerewere, ziwerewere *zauzimu*: iye akuphuzitsa chinachake kwa anthu chimene sichiri Mawu a Mulungu. Nkulondola uko? Iye akuphuzitsa chinachake chimene sichiri chowona. Ndicho Chinikolai. Mukuziwona izo zikubwera apa? Kumapita kumakaika mapapa, ndi ansembe, ndi kumatulutsako Mzimu Woyera, “Masiku a zozizwitsa anapita”; ndipo Baibulo linati, “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo ndi kwa nthawizonse.” Baibulo linati, “Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu”; iye akuti, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” kukonkha, kutsanulira pamenepo. Oh, mai! Mukuona?

¹⁷¹ Chabwino, penyani zomwe mkazi uyu anali kuchita:

*. . . amene mafumu adziko lapansi achita naye
ziwerewere, ndipo okhalapo apa. . . dziko lapansi
aledzeretsedwa ndi vinyo wa ziwerewere zake.*

¹⁷² “Kuledzera!” Kukupha iwe, kukakuika ku imfa, kukuwombera iwe, kapena china chirichonse, m’bale. Iwo aledzera mwamtheradi ndi zinthu zimenezo. Mukuona?

¹⁷³ “Vinyo.” Ndi zomwe iye akupereka, onani, vinyo wake wa ziwerewere zake. “Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake! Amayi anga anali Mkatolika, ndipo ine. . .” Chabwino.

¹⁷⁴ Tsopano inu mukuti, “Izo ndizowopsya.” Tsopano ingodikirani miniti, Achiprotectanti. Huh! (Ine ndikuyankhula kwa awa pa matepi, mwawona.)

*Chotero iye ananditengera ine kutali mu mzimu
kupita ku chipululu: ndipo ine ndinawona—ine
ndinawona mkazi atakhala pa chirombo chofiira, . . .*

¹⁷⁵ Tsopano, kodi mawu *ofiira* amanena za chiyani? Iwo amanena za “ufumu.” Kutanthauza. . . Ine ndikutanthauza, amanthauza, “ufumu, kumvera, ufumu,” onani, monga mafumu ndi zina zotero.

*. . . lodzala ndi maina amwano, lokhala ndi mitu
seveni ndi nyanga teni.*

¹⁷⁶ Tsopano, *mitu* seveni ndiyo “mapiri” seveni pomwe mzindawo ukukhalapo. Ndipo mkazi uyu ndi mzinda, ife tikudziwa.

Ndipo mkaziyo anavekedwa cha pepo . . .

¹⁷⁷ “Mkaziyo.” Chilombocho chinali *chofiira* kwambiri, koma mkaziyo anavekedwa *pepo*. Tsopano, kodi ine sindinakuchenjezeni inu tsiku lina, pali makatani atatu? Ine sindikudziwa kuti ndidzakhala ndi moyo motalika bwanji, koma kumbukirani izi. Monga ine ndinakuwuzani inu zaka zambiri zapitazo, “penyani Russia.” Pali makatani atatu, kumbukirani izi. Pali katani ya *chitsulo*. Pali katani ya *nsungwi* (Red China ndi zina zotero). Ndipo pali nsalu yotchinga ya pepo, inu mupenye katani *imeneyo*, *imeneyo* ndi wachinyengo. Kwambiri zedi . . .

. . . mkaziyo anavekedwa pepo . . . mitundu yofiira, . . . wodzikongoletsa ndi golide . . . miyala yamtengo wapatali ndi ngale, (Mukukumbukira ine ndikuyankhula kumbuyo kuno chomwe guwa loyamba linali la Chinikolai? Mukuona? *Mkazi* kukhala “mpingo.”) *ali ndi chikho chagolide mdzanja lake* (Inu mukukumbukira? Golide anakuta guwalo, chikho chimene iye anali kuwapatsa anthu.) *chodzadza ndi chonyansa cha zonyansa za ziwewere zake:*

¹⁷⁸ Ndicho chimene iye akuwapatsa anthu; iwo anali kuchimeza icho. Ndithudi. Amaledzera zimenezo! Amangoledzera basi! Gulu lonse ilo la chi Irish, ndi chi Faransa, ndi zina zotero, kudula khosi lako ngati unena chinthu chimodzi motsutsana ndi mpingo umenewo. Ndithudi, iwo angatero. Mukuona?

Ndipo pamphumi pake panalembedwa dzina, CHINSINSI, BABULO . . .

¹⁷⁹ Tsopano, kodi Babulo anasamukira kuti? Kuchokera ku Babeloni mpaka ku Pergamo, ndi kudzakhala . . . Satana akusuntha mpando wake. Oh, ine ndikukhumba ife tikanakhoza kudutsa mu Chivumbulutso chonsecho, kuchitira kuti inu mukhoze kuchiwona icho.

. . . BABULO WAMKULU, MAYI WA TIMAHULE . . . MAYI WA TIMAHULE NDI ZONYANSA ZA DZIKO LAPANSI.

¹⁸⁰ Kodi iye anali chiyani? Mayi wa mahule. Iwo sanali ana. Kodi iwo anali?

¹⁸¹ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . mpingo wawo. Inde, bwana. Anati, “Kodi mpingo sutchedwa, mu Baibulo, ‘Babulo?’” Mwawona, mu bukhu lawo lomwe. Chabwino.

¹⁸² Tsopano, ngati iye anali wachiwewere, hule, ndipo iye anali mayi wa achiwewere, iye amayenera kukhala ndi ana aakazi. Ndipo ngati iwo anali ana aakazi, iwo anali atsikana, iwo anali mipingo. Tsopano kodi mpingo wa Chiprotestanti unachokera kuti? Nkulondola uko? Kodi kusiyana kwake

nchiyani pakati pa—pa hule ndi wachiwerewere? Chinthu chomwe chomwecho.

¹⁸³ Martin Luther anatulukapo, kudzayatsa, kuti adzawupatse Mpingo wona mwayi; Wesile; mpaka ku Pentekoste; ndipo mmodzi aliyense wa iwo anabwerera kumene ku lingaliro la Chinikolai loti apange bungwe, ndi oyang'anira onse, ndi china chirichonse, ndipo anabwerera komwe uko ndi ubatizo womwewo umene iwo anabatizidwa nawo, mawonekedwe omwewo, miyambo yomweyo, ngakhale ambiri a iwo ali ndi makatekisimu ndi '*tikuoneni Mariya.*' Osati *Tikuoneni Maria*, koma . . . Kodi ichi ndi chiyani chimene chiri pafupifupi chinthu chomwe chomwecho? *Chikhulupiriro cha Atumwi* chija. Ndiwonetseni ine Chikhulupiriro cha Atumwi mu Baibulo, m'bale. Ngati—ngati iwo anali ndi kachikhulupiriro, kanali Machitidwe 2:38, ndi zomwe analamulira aliyense kuti azichita. Ndi pati pamene inu munamumvapo mtumwi akupanga kachikhulupiriro, kumati, "Ine ndimakhulupirira mu Mpingo Woyera wa Roma Katolika. Ine ndimakhulupirira mu mgonero wa oyera"?

¹⁸⁴ Pamene . . . Petro, yemwe anali ndi mafungulo, anati, "Palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi anthu, koma Khristu Yesu."

¹⁸⁵ Koma tayang'anani pa mipingo ya Chiprotestanti. Kodi iwo ankachita chiyani? Iwo samakhoza kukhutitsidwa. Mmodzi aliyense wa iwo amene anatuluka, anatuluka ndi Madalitso Achipentekoste. Ndizo ndendende kulondola. Ngakhale Martin Luther anayankhula mmalirime. Ndiko kulondola ndendende. Anadzichotsako yekha, anati, "Mulungu, mawu oyipa amene ine ndikunong'ona, ndipo sindikudziwa zomwe ine ndikunena." Mukuona? Ndithudi, iye amakhulupirira mwa Iwo. Ndithudi, iye amatero.

¹⁸⁶ Tsopano, kudutsa mu m'badwo iwo akhala ali nawo—ali nawo Mzimu, koma iwo nthawizonse amachokako ndi kukapanga mabungwe oyambitsa akachokapo ndipo apita. Ngati inu mukanalola mpingo wa Lutheran kuti uzipitirira, ndipo osawupanga iwo bungwe, iwo ukadakhala wa Pentekoste. Kodi Mpingo wa Pentekoste ndi chiyani? Ine ndikutanthauza pentekoste weniweni. Osati chipembedzo, tsopano, ziri chimodzimodzi monga "mphika ndi ketulo" kachiwiri. Mukuona? Koma iwo anachita chinthu chomwe chomwecho, ndipo izo zinawapanga iwo kubwerera ku Chinikolai chimodzimodzi monga momwe iwo anachitira pachiyambi. Ndi angati akuwona zimenezo? nenani "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni!"—Mkonzi.] Uko nkulondola. Tsopano, kungoti ndikhale ndi mawu anu kuti ndinu . . .

¹⁸⁷ Onani, mayi wa "achiwerewere." Ngati iwo ali achiwerewere, kodi iwo anakhala bwanji achiwerewere?

Pochita ziwerewere motsutsana ndi Mawu a Mulungu. Ngati Mawu a Mulungu anati, “Lapani ndipo mubatzidwe mu Dzina la Yesu Khristu,” ndipo munthu aliyense mmenemo nkubatzidwa mu Dzina la Yesu, ndiyeno nkutenga “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Kuteroko ndi chiwerewere! Nkulondola uko? Ndipo ngati kubatiza kwa Baibulo ndi kumiza (*baptizo*, kuchokera ku mawu a Chigriki), ndiye inu mumapeza bwanji kukonkha ndi kutsanulira? Kodi zimenezo zikulowera pati? Ngati inu mukulowetsa mmalo kugwirana chanza, kapena kutenga kokulumunya pa mlomo panu ndi kumeza iko, kapena chinachake chimzake monga choncho, kukhala Mzimu Woyera, ndipo Mzimu Woyera unabwera kuchokera Kumwamba ngati mphepo ya nkokomo wamphamvu ndipo inawadzaza anthu, ndipo nkudzawapangitsa iwo kuyankhula mmalirime, ndi kufuula, ndi kumachita ngati munthu woledzera, ndipo inu nkulowezapo kugwirana chanza, kapena kukayika kalata yanu ku tchalitchi, kapena chinachake chonga zimenezo, ndiye inu mudzachokapo bwanji pa njira yochita ziwerewere zauzimu?

¹⁸⁸ Tsopano, mungodzifunsa nokha zimenezo. Musasire malingaliro anu pansi, mutsegule mtima wanu ndipo mukhale woona mtima, abale. Ife tiri pamapeto a ulendo. Misonkhano iyi sinangoikidwa pano pachabe, iyo inakonzedweratu ndi Mulungu. Ine ndikukhulupirira zimenezo motsimikiza basi monga ine . . . inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake. Ine ndikunena izi mu Dzina la Yesu, kuti Mulungu anaziika izo pa mtima wanga kuti ndibwere kuno. Ine sindimalandira kobiri limodzi pochita izi. Ine—ine—ine—ine—ine ndikanakhoza kukhala ndiri kunjika kuno ndikupempherera odwala kwinakwake, kapena chinachake chonga zimenezo. Kapena ndikanakhoza kukhala nditapita kutali kokawedza, ndi kumakatenga ndalama zanga chimodzimodzi basi, ine ndimalandira malipiro kuchokera ku tchalitchi. Koma Mulungu anaziyika Izo pa mtima wanga; ine ndimalephera kuti ndichoke kwa Izo, zimangokhalira kulirira kwa ine pa Izo, ndipo ine ndikuchita zonse zomwe ine ndingathe. Ine ndiri pano mu Dzina la Ambuye, kudzachita chirichonse chimene ine ndikuchidziwa kuchita. Musalole kuti Izo zikudutseni inu.

¹⁸⁹ Tsopano, Achiprotectanti, kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza ndi mpingo wa Katolika ndi wa Chiprotectanti? Basi . . . Umodzi uli chimodzimodzi monga winawo. Ndiko kulondola ndendende.

¹⁹⁰ Tsopano, zikutanthauza wokwatiwa, *Pergamo* amanthauza “wokwatiwa.”

¹⁹¹ Tsopano tiyeni titenge . . . Iye anati, “Iwe uli nawo iwo pakati pako omwe ali ndi chiphunzitsa cha Balamu.” Tiyeni tingotenga izo.

¹⁹² Kodi tiri nayo nthawi? Ine ndifulumira mwachangu momwe ine ndingathere. Kapena kodi inu mukhoza kungodikirira ndikuwona ngati ife tingakhoze kubwerera mmawa? Ndi angati akuti kuli bwino tipitirire nazo, kanthawi pang'ono chabe? Tiyeni... Chabwino, tsopano ine—ine ndikudziwa mwatentha mkati muno. Ndipo ngati mwangokhala pamenepo ndipo kukutentha, inu mukuganiza chiyani pamtunda pano? Inu mukuona? Koma, oh, mai, ife tikuyesetsa kuti tichoke pamalo amenewo amene *ali* otentha. Mwawona, ndi—ndi chimene icho chiri, pakuti, ndife Amuyaya.

¹⁹³ Tsopano, tsopano kunena moonana pamene iwo anakhazikitsa mpingo wonga umenewo, chinachitika ndi chiyani? Tsopano mveterani mwacheru, ana anga. Chinachitika ndi chiyani? Bwanji, moonana, zimenezo zinachotsa kumene Mzimu Woyera mu mpingo. Nzosadabwitsa kuti palibe wa mabishopu awo amene anawukitsa wakufa kapena kuchita zozizwitsa. Ndipo iwo kuyankhula za ena a oyera awa kukhala mu mpingo mwawo! Iwo anachitsutsa chinthucho, koma iwo amati ndi awo!

¹⁹⁴ Tayang'anani pa Joan waku Arc, mtsikana wamng'ono uja. Ine ndikukupemphani inu anthu Achikatolika, kapena inu Achiprotestanti, aliyense wa inu. Joan waku Arc, mu tsiku lake, kunalibe kanthu mu France kumeneko, koma mpingo wa Katolika umene unawasokoneza oyera. Koma Mulungu anasunthira pa mtsikana ameneyo ndipo analandira Mzimu Woyera. Ndipo kodi iye anachita chiyani? Iye amakhoza kuneneratu zinthu, Ambuye amakhoza kumupatsa iye masomphenya ndi kuneneratu izo. Iye amapempherera odwala. Iye anapempherera mwana wakhanda wakufa, ndipo iye anabwereranso ku moyo. Ndicho chipentekoste. Mukuona? Ndipo kodi mpingo wa Katolika unachita chiyani kwa iye chifukwa chotsutsa mpingo wa Katolika? Iwo anamuitanitsira mlandu, ndipo anamuwotcha iye pa nkhu ni ngati “mfiti.”

¹⁹⁵ Ndipo tsopano inu mukuti, “Woyera Joan waku Arc.” Zaka thuu handiredi mtsogolo, pafupifupi, pamene mpingo unadzapeza zomwe iwo anali atachita, kuti iye anali Woyera, oh, ndithudi, iwo anachita kulapa chifukwa cha izo; iwo anakumba thupi la ansembe amenewo anavomerezera imfa yake, ndipo anawaponyera iwo mu mtsinje. Inu mukuganiza kuti zimenezo zingatsuke magazi mmanja mwake? Baibulo linati, “Ma—magazi a wofera aliyense anapezeka mwa iye.” Izi ndi zimene Mngelo wa Ambuye ananena kuti zimapezeka mu Babulo, “Wakupha aliyense, kapena wofera, ndi oyera onse a Khristu omwe anaphedwa konse, anapezeka umu kuchokera ku M'badwo wa Chinikolai kudutsa kumapitirira, wofera aliyense.” Taganizani za zimenezo. (Zikomo inu, M'bale Ben.) Tsopano, taganizani za zimenezo.

¹⁹⁶ Tsopano, tipitirire patsogolo pang'ono tsopano. Mpingo wa Chikhristu unakwatirana ndi a—ndi... Babulo. *Pergamo* amatanthauza “ukwati.”

¹⁹⁷ Tsopano, “Chiphunzitso cha Balamu. Inu muli nawo iwo pakati panu omwe ali ndi chiphunzitso cha Balamu.”

¹⁹⁸ Oh, ine ndimangozikonda zinthu izi. Oh, ngati inu mutangokhala motalikira pang'ono pa chimodzi, mwawona, koma inu basi... Ife tikufuna tikuloleni inu kuti muwone ndipo kenako musunthire kwa china chakenso, chifukwa ndi basi—pangodzaza zonona za golide. Ndine wofufuza; ine ndimakonda kupita ndi kukakumba zonona zimenezi ndi kuziwalitsa izo, ndi kuzipukuta izo monga chonchi, ndi kuyang'ana pa izo. Ndipo chirichonse cha izo chizinyezimiritsa Yesu Khristu! Aliyense wa iwo, mwawona. Aliyense wa iwo akunyezimiritsa Yesu Khristu. Iye ndi Alfa ndi Omega, iliyonse—Karati iliyonse ya golide mu zononazo. Uko ndi kulondola. Iye ali chidutswa chirichonse cha Iwo. Ndi chifukwa chake, Iye ndi Umulungu wopangidwa thupi pakati pathu.

¹⁹⁹ Tsopano, kuti tipeze... ine—ine sinditenga nthawi chifukwa cha izi, chifukwa ine ndiri... ine ndikuwona kuti ndi naini. Ndipo ine—ine ndiri ndi chinthu china chimene ine ndikufuna kuti ndilowemo usikuuno, ngati Mulungu alola. Ndipo ine ndikufuna inu kuti mungolemba izi ndipo inu mukawerenga izo mawa, ndipo inu mulembe Numeri 22 mpaka 25. Ine ndikufuna inu kuti muwerenge zimenezo tsopano, ndipo inu mukhoza kunditsatira ine. Ndipo tsopano—ndipo tsopano Numeri 22 mpaka 25.

²⁰⁰ Ife tikudziwa kuti Israeli—Israeli anali anthu osankhidwa a Mulungu. Nkulondola uko? Iwo anali... Iwo anali Achipentekoste. Iwo anali nawo Mzimu pakati pawo. Inu mukukumbukira uthenga wa usiku watha? Momwe kuti Mose pamene iye anawoloka Nyanja Yofiira, kapena Nyanja Yakufa, ndipo napeza kumbuyo kwake mu Nyanja Yofiira, ya magazi, kuimira magazi... onse owagwiritsa ntchito omwe ankamumenya iye ndi ana onse a Israeli. Mose anakweza dzanja lake ndipo anaimba mu Mzimu. Oh, mmodzi aliyense wa ife akhoza kukhala Mose pamene ife tiyang'ana mmbuyo mu Magazi ofiira a Ambuye Yesu ndi kuwona woledzera wakale aliyense, botolo lirilonse lakale, mkazi aliyense woipa, chinthu choipa chirichonse chakale chomwe ife tinachitapo mmoyo wathu, zonse zitafa mu Magazi a Ambuye Yesu. Zimatipangitsa ife kuyimba mu Mzimu! Ndudu, fodya, ndi zizolowezi zoipa, ndi china chirichonse, zitafa, mu Magazi a Ambuye Yesu; ndiye ife tikhocha kukweza manja athu ndi kuyimba mu Mzimu. Mukuona?

²⁰¹ Taonani zomwe Miriamu anachita, mneneri wamkazi. Tsopano, kumbukirani, iye anali mneneri wamkazi. Iye anatenga

nkhotcho ndipo anayamba kumenya nkhotchoyo ndi kumavina mu Mzimu, ndipo ana aakazi a Israeli anamtsatira iye mpaka ku gombe, akuimba nkhotcho izi, ndi kumavina mu Mzimu. Pentekoste yenyeni!

²⁰² Ndiyeno ngati inu mungazindikire pamene iwo anadzafika ku Moabu. Tsopano ife tikubwerera...Ife tiri pa Lemba, tsopano, “chiphunzitso cha Balamu.” Ndipo Moabu, Moabu anali mchimwene wake wa Israeli. Ndi angati akudziwa kumene anachokera Moabu? Chabwino. Moabu ndi omwe ine ndikhoza kuwatchesa a haiburidi, chifukwa chakuti Moabu anayambira kwa ana a Loti. Loti anali ndi mwana mwa mwana wake yemwe wamkazi, anali ndi ana awiri. Ndipo Moabu anali mmodzi wa iwo, ndipo iye anapanga fuko la Moabu, fuko. Ndipo, kwenikweni, Loti anali mmphwake wa Abrahamu, yemwe anadzadzera mu mzere womwewo. Ife tikudziwa zimenezo. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire kuti iwo sanali achikunja, monga momwe ena a masewero athu aposachedwapa angakupatsireni inu...Kumbukirani, iwo anali okhulupirira. Tsopano, pamene apa panadzabwera Israeli paulendo wawo wa ku dziko lolonjezedwa, akupanga njira yawo kumene ali mu mzere wa ntchito, ndipo apa panali Moabu panjira kumene. Iwo anatumiza amnthenga ku Moabu, ndipo anati, “Tiloleni ife tidutse mdziko lanu. Ife ndi m’bale wanu.”

²⁰³ Tsopano, Moabu ankaimira Chinikolai. Tsopano inu mukuwona mu miniti yokha. Israeli ankaimira Mpingo wooka. Ndipo Balaamu anali mmodzi wa mabishopu, mapapa. Penyani ndipo muwone tsopano; Chikhristu chachithupithupi. Tsopano ife tikuzindikira kuti iye anali ndi mphatso, palibe kukaikira zokhudza izo. Ambiri a iwo ndi oyankhula abwino, madotolo azolakatula, ndipo—ndipo amuna otchuka. Inu simungakane zimenezo. Koma, “Akukhala nawo mawonekedwe achipembedzo, koma kumakana Mphamvu yakeyo.”

²⁰⁴ Bwererani ku Pentekoste yapachiyambi ija! Musati muchokeko kumeneko. Ngati pamene inu mutero, inu mwataika. Mukhale ndi mdalitso umenewo. Ndi Zimenezotu, Wodalitsa wa mdalitso.

²⁰⁵ Tsopano, zindikirani pamene iwo anali kuyenda. Iwo anadzafika ku mpingo wofunda wa haiburidi uwu, ndipo iwo anati, “Ife tikudutsira ku chitsitsimutso. Ife tikupita ku dziko lolonjezedwa. Kodi inu mungatilole ife kuti tidutse? Ngati ng’ombe zathu ziti zinyambite udzu uliwonse, ngati izo ziti zimwe madzi aliwonse, ife tikulipirani inu chifukwa cha izo.”

²⁰⁶ Ndiye iye kodi anachita chiyani...? Mfumu Balaki, iye anasangalala kwambiri, ndipo iye sanafune msonkhano ngati umenewo mu tchalitchi chake kapena mdziko lake. Chotero kodi iye anachita chiyani? Iye anatumiza kwa papa, kapena kwa bishopu, Balamu, mneneri waganyu, yemwe anakonda

ndalama kuposa momwe iye amakondera Mulungu. Ndipo Mfumu Balaki inamuwuzwa iye kuti, “Ngati iwe ungafike kuno ndi kudzawatemberera anthu awa, ine ndidzakupanga iwe kukhala munthu wopambana.” Ndipo Mulungu anayankhula ndi Balaki. Ndipo ine ndikudabwa ngati zingachitike chomwecho-...Ine ndikutanthauza Balamu. Ndikudabwa kuti ndi a Balamu angati alipo mdziko lapansi usikuuno? Atumiki a Methodisti, atumiki a Baptisti, ansembe Achikatolika, (Chifundo!) amene amamudziwa Mulungu ameneyo...ngati inu mungawerenge mbiriyakale yomweyi komanso Bukhu lomwelo limene ine ndimawerenga. “Balaamu!”

²⁰⁷ Tsopano, zindikirani. Kenako iye anati, “Bwera kuno ndipo udzawatemberere anthuwo.”

Ndipo Balaamu anati, “Ine ndimufunse Mulungu.”

Mulungu anati, “Iwe usapiteko!”

²⁰⁸ Koma mmawa wotsatira, iye anati...iye anapita ndipo anakamuuzwa wansembe, kapena a—a mfumu.

Ndipo anabwererako, anati, “Oh, ine—ine ndikupanga iwe kukhala munthu wotchuka.”

Chotero Balamu anapitirira; Mulungu anati, “Kazipita ndiye, iwe kapitirize.”

²⁰⁹ Mwawona, ngati iwe sutsatira Choonadi... Inu mukuganiza, Achinikolai, chifukwa chakuti Mulungu akukuchitira iwe zomwe ukuchita monga choncho...Chiripo Choonadi chapachiyambi! Inu mukungotenga chifuniro chongololera cha Mulungu. Inu mukuti, “Mulungu amatipatsa ife Mzimu Woyera,” kapena “Iye amatidalitsa ife, ndipo ife timabatizidwa mu dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Iwe Balamu! Mwawona, chiphunzitso cha Balamu. Mulungu anamuwuzwa iye, iye atakhala wamwano kwambiri, Iye anangomulola kuti azipita, nakadzipachika iye yekha. Iwe uyenera kubwerera ku Choonadi, Choonadi cha maziko. Kubwerera ku Baibulo. “Oh, chabwino, Iye watidalitsa ife! Ndipo gi-...” Oh, ine ndikudziwa zimenezo. Iye anatero, anamuuzwa Balamu, anati, “Iwe kazipita. Ngati iwe ukufuna kuti uzipita, ngati ndizo...Iwe ukufuna kutenga njira imeneyo, ndipo iwe ukufuna njira ya bungwe; utenge imeneyo kazipitirira.”

²¹⁰ Ndiye Balamu anawuyambapo, ndipo analumphira pa mphongolo yake, kapena, osati mphongolo yake, bulu wake, kutsika kudutsa kumeneko iye anapita. Ndipo chinthu choyamba, inu mukudziwa, Mngelo wa Ambuye anayima pa njira. Ndipo, inu mukudziwa, mneneri ameneyo, papa ameneyo, bishopu, kadinoro, chirichonse chomwe iye anali, anali wakhungu kwambiri ku zinthu zauzimu, poganiza kuti iye amukweza pantchito, chifukwa iye amakhala mu Mtsinje wa Firate. Ine ndikulingalira kuti iye ankaganiza kuti icho chinali cholowa china, monga “Pa thanthwe ili ndidzangapapo Mpingo

Wanga,' Petro," kapena pa thanthwe lina lomwe linali mu Roma, kapena chinachake. Koma pamene iye anadzafika pamalopo, pamenepo anaimirira Mngelo wokhala ndi lupanga losololedwa, ndipo iye anachititsidwa khungu kwambiri mwakuti iye samakhoza kuwona izo. Ndipo mphongolo inamenyetsa phazi lake kukhoma. Ndipo kenako iye anamukwera iye, ndipo mnge—Mngelo anadzaimanso pa njira. Mulungu adzatseka khomo lirilonse! Ndipo mphongolo iyi inapotolokabe. Ndipo iye analumphapo nachoka, ndipo anatenga ndodo yake ndi kuyamba kumufulira iye ndi iyo. Bulu wamng'ono uyu, atagona pamenepo, akumenyedwa pamutu.

²¹¹ Ndipo ine, ndithudi chomwe chinamusintha iye, nchiyani chinamupangitsa iye kukhala nalo lingaliro, kapena kumuuza iye pamene amalakwitsa, Iye analola mphongolo imeneyo kuti iyankhule mmalirime. Osati mphongolo, iye anali bulu! Musanene kuti iye anali "mphongolo;" iye sakanazikwanitsa zimenezo, iye anali haiburidi. Inu mukuona? Iye anali mbewu yapachiyambi.

²¹² Moabu anali, "Zizindikiro zitapita, zinthu zonse zitapita." Israeli anali ndi zizindikiro zikumutsatira.

²¹³ Koma bulu wamng'ono uyu anapotoloka ndipo anati, "Kodi ine sindinakhale bulu wako? Kodi ine ndinayambapo. . ." Ndipo ameneyo—bishopu wakhungu ameneyo atakhala pamwamba apo, akuimenyabe mphongolo imeneyo; ndipo mphongoloyo inayamba kuyankhula kwa iye, mu malirime osadziwika kwa mphongolo.

Ndipo iye anati, "Inde, ndiwe—ndiwe bulu wanga."

"Ndipo kodi ine—kodi ine sindimakunyamula iwe, kapena kodi ine ndinayamba ndakulepherapo iwe?"

"Ayi, inu simunateropo. Koma ngati ine ndikanakhala ndi lupanga, ine ndikanakupha iwe, ine ndikanaimitsa msonkhano uno. Ine ndiri paulendo wanga ndikupita kumusi uko kukaletsa gulu ilo la oyera odzigudubuza kuti asadutse mdziko lino. Ine—ine ndikayika izo pa iwe." Mukuona?

²¹⁴ Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anapezeka akuyang'ana pozungulira, iye anaganiza, "Chabwino, izi ndizoseketsa. Ine ndikumva mphongolo ameneyo akuyankhula."

²¹⁵ Oh, Balaamu! Hmm! Mwawona, Mulungu nthawizonse wakhala akuyankhula mmalirime osadziwika kwa anthu. Iye anatero mmasiku a. . .Inu mukuti, "Izo zimachitika pa Apentekoste basi." Oh, ayi. Ayi, ayi. Pa phwando la Belsazara Iye anayankhula mmalirime, anazilemba Izo pa khoma. Iwo anali ndi munthu pamenepo amene anali ndi mphatso ya kutanthauzira, chotero iye anatanthauzira iwo kwa iwo, anawauza iwo chimene icho chinali. Chinthu chomwe chomwecho lero.

²¹⁶ Chotero, pokhala kuti apo panalibepo wotanthauzira kwa Iwo, Mulungu anangomulola Balamu uyu kuti atutumuke (kardinoro uyu) ndi kuzindikira chomwe Icho chinali. Ndipo kodi inu mukudziwa kuti munthu wakhungu uja anapitabe mulimonse? Ndithudi. Ndi momwe iwo amachitira izo lero, chinthu chomwecho; Amoabu, Achinikolai, akupitirirabe mtsogolo. Ndipo iwo anapitirirabe mpaka kumeneko, ndipo iye anapita . . . Tsopano penyani, ngati Mulungu akanati azisamalira zachikhazikitso, Iye akanakhala wokakamizika kuti amudalitse Moabu; chifukwa, zindikirani, Balaamu anamanga maguwa seveni. Ndizo ndendende.

²¹⁷ Nambala seveni: mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Mukuwona momwe zikufananira ndi zauzimu? Tsopano, gwirani pamenepo tsopano: zikufanana ndi zauzimu. Ine ndifika kwa izo mu miniti, pamalo ovuta. Mwaona, kufanana ndi zauzimu. Maguwa a nsembe seveni, ng'ombe seveni (nyama zoyera), ndi nkhosa zamphongo seveni; kuyankhula za kudza kwa Khristu, zaka mahandiredi ambiri Iye asanabwere.

²¹⁸ Koma, iwo amakhulupirira. Kodi iwo amakhulupirira chiyani? Iwo amakhulupirira mwa Yehova Mulungu. Ndi chiyani china chomwe iwo ankakhulupirira? Iwo ankakhulupirira kuti nsembe zoyera imayenera kuperekedwa. Uko nkulondola. Ndipo iwo ankadzinerera kuti iwo ankakhulupirira kuti Mesiya akubwera, chifukwa iwo anapereka nkho—nkhosa yamphongo, yomwe inali nkhosa yamphongo. Nkulondola uko?

²¹⁹ Tsopano, inu mudzangomangirizana ndi wa Baptisti nthawi ina; mudzafufuze ngati iwo samachita chinthu chomwe chomwecho. Ndiko kulondola ndendende.

²²⁰ Chabwino, tsopano pali kusiyana kwanji? Apa pali Israeli pansu pa phiri, akupereka zopereka zomwezo zomwe iwo amapereka kuno, akupemphera kwa Mulungu yemweyo. Kodi inu simukuwona Achinikolai? Haiburidi! Mukuwona zimenezo? Kodi inu simukuwona zauzimu zenizeni? Kodi panali kusiyana kwanji pakati pawo? Mmodzi wa iwo anali ndi zizindikiro zikutsatira! Wina anali ndi *mawonekedwe*, winayo anali ndi *zizindikiro zikutsatira*.

²²¹ Ndicho chinthu chomwecho chimene chinachitika kuno, Nicene Council; Chinikolai, Chikhristu wamba. Ndipo Mzimu Woyera unabwereranso ndipo unati, “Inu muli nacho chiphunzitso cha Balamu pakati panu.” Mukuona? “Ndipo inu. . . Ine ndimadana nazo ntchito za Anikolai, ziphunzitso izo zomwe iwo ali nazo, chifukwa icho ndi chiphunzitso cha Balamu yemwe anaphunzitsa ana a Israeli kuti aphundwe.” Kodi iye anachita motani zimenezo?

²²² Ndiye pamene iye anatuluka kuti akatemberere anthu amenewo, Mulungu anati, “Ine ndikamanga lirime lako; iwe sukanena zoposa zomwe Ine ndikakuuze iwe. Iwe sungakhoze

kutemberera zimene ine ndazidalitsa.” Chotero iye anayang’ana pansu pamenepe.

²²³ Ndipo tayang’anani pa wachinyengo uyu! Oh, ife tikhoza kungopitirira nazo izo, mwawona. Tayang’anani pa Mfumu Balaki yakale iyi, m—m—m—mkulu wa zonse za izo, anamuza apa mneneri wabodza uyu, anati, “Pita kumusi uko ndipo ukangoyang’ana kumbuyo kwa iwo.”

²²⁴ Umo ndi momwe ma—matchalitchi akuluakulu amakonda kunena kwa apang’ono a Mulungu. “Inu mukudziwa chiyani? Ine ndimamudziwa mmodzi wa iwo. Mnyamata! Inu mukudziwa zomwe iye anachita? Iye—iye anachita izi, ndipo iye anachita izo. Awo ndi Achipentekoste. Ndithudi.” Oh, koma ngati inu mukangodziwa choonadi cha *iwo*, koma mapepala ndi zinthu zimatontholetsa izo. Koma mulole wachi Pentekoste wamng’ono achite zabwino nthawi ina, ndipo mudzawone momwe dziko lonse limazitsekerereza izo. Ndithudi. Inde, bwana.

²²⁵ Koma, tsopano zindikirani, iye anati, “Ukangoyang’ana ku nsana, ku nsana, gawo loyipitsitsa la iwo.” Balamu anati, “Eya, ine ndikangoyang’ana mbali yaku nsana, gawo loyipa lija lomwe iwo amachita. Ndizo zimene ine nditi ndikachite, ine ndikangoyang’ana pa zawo—zoipa zawo, zopanda-pake zawo.” Chifukwa ngati iwe ukayang’ane zopanda-pake, iwo analibe. Uko nkulondola. Iwo anali atachita tchimo lirilonse la pa kalendala. Koma zomwe iye analephera kuti awone, iye analephera kuti awone Thanthwe lokanthidwa, Njoka ya Mkuwa ija, chisangalalo chija chakuti Mfumu ili pakati pawo, machiritso, zizindikiro, zodabwitsa, ndi Lawi la Moto lija litapachikika pamwamba pawo.

²²⁶ Mneneri wakhungu uja samakhoza kuwona Zimenezo. Ayi, bwana. Koma iye anali kuwonetsa gawo loyipa la iwo, “Chabwino, ine ndikudziwa amene anathawitsana ndi mkazi wa munthu wina. Ine—ine ndikudziwa izi, iye anaba ndalama zina.” Uko nkulondola. Uko nkulondola. Ine ndivomereza zimenezo; koma iwo ali nacho chinthu chomwecho cha kumeneko, koma iwo sananene kanthu za izo. Mukuona? Chotero iye akungowonetsa gawo loyipitsitsa.

²²⁷ Koma Iye anati, Mulungu anati, “Iwe ukangonena zimene Ine ndikunena.” Ndipo Balaamu analowa mu Mzimu, anagwera mu chizimbwizimbwi; ndipo mmalo motemberera Israeli, iye analidalitsa iye. Amen! Ndi ameneyo apo.

²²⁸ Tsopano, ngati Mulungu akanati abwezere... kapena maulemu kwa achikazikitso, masukulu apamwamba awa, ndi maseminare akuluakulu ndi koleji, ndi ma Ph.D. ndi ma D.L.D. ndi, oh, mitundu yonse ya ma D.D... Chabwino, bwanji ngati Iye akanakhala ndi ulemu kwa izo, chabwino, ndiye, inu mukanakhoza... Iye akanayenera kukhala nawo ulemu kwa iwo. Mukuona? Koma iye amalemekeza ndipo anali atawadalitsa

kale anthu awa ndi mdalitso, chifukwa Mzimu, Mfumu. . . Iwo anati, “Munali mfuwu wa Mfumu mu msasa.” Chiyani? Chiyani? “*Mfumu ya oyera.*” Kufuula ndi chisangalalo! Za chiyani? Ufumu wina.

229 Ine nditsimikizira kwa inu kuti iwo sanali zipembedzo. Inu mukufuna kuti ine ndichite zimenezo? Ine ndikuganiza ine ndalemba Lemba apa la zimenezo. Inde, bwana. Ndiroleni ine nditsimikizire kwa inu kuti Israeli sanali. . . Tiyeni tibwerere ku Numeri, basi kuti inu muwone kuti iwo sanali. Iwo. . . Tsopano, Moabu anali chipembedzo chachikulu. Ife titenga Numeri 23: 9, ine ndipeza ndi—ndime ya 8 ndi iyo:

Ndipo. . . *Ine ndingatani—ine ndidzatemberera bwanji, (anatero Balamu), amene Mulungu sanamutemberere? kapena ine ndinganyoze bwanji amene AMBUYE sanamnyoze?* (Uh-huh.)

230 Tsopano mvetserani zimene. . . zimene Iye ananena:

Pakuti—Pakuti kuchokera pamwamba pa matanthwe ine ndinamuwona iye, . . . (Ameneyo ndi Mulungu. Osati kuchokera mmusi mwa chigwa, koma kuchokera pamwamba pa matanthwe. Oh! “Diso lake limakhala pa mpheta, ndipo ine ndikudziwa kuti Iye amandiyang’ana ine.”) . . . kuchokera pamwamba pa matanthwe ine ndinamuwona iye, . . . (Ameni! Osati kuchokera kwina. . . kumbuyo kuseri kwa chigwa kuti ukakhoze kuwona mbali ya kumbuyo kwawo; “ine ndinawona chinthu chonsecho,” Mulungu anatero.) . . . kuchokera pamwamba pa matanthwe ine ndinamuwona iye, ndipo kuchokera kumapiri ndinamuwona iye: taonani, anthu adzakhala okha, ndipo sadzawerengedwa pakati pa mafuko.

231 Izo zikukhazikitsa izo? Iwo sanali chipembedzo, “mafuko.” Oh, iwo anali oyendayenda, mmahema, mmisewu, pansu pa mphambano ya msewu, mishoni yaying’ono. Amapita kumbuyo, lendi, amakawathamangitsako iwo; Mulungu ankafuna kuti iwo azipita kwina kwakwenso. Mukuona? Oyendayenda! Kulondola!

232 Uko ku Jamaica, osati kale kwambiri, kunali dokotala wabwino wa Chipentekoste waumulungu ataima pamenepo. Ndipo ine ndinati, “Oh, momwe Ambuye anadalitsira Mpingo woyambirira wa chipentekoste: iwo analibe kalikonse.” Ine ndinati, “Iwo anangokhala oyendayenda, pafupifupi.”

Iye anati, “Uh, M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Inde, m’bale.” Mkondeni iye; chabwino m’bale.

Ndipo iye anati, “Ine—ine ndimangofuna kukuwonetsani inu pamene inu mukulakwitsa.”

Ine ndinati, “Oh, ndine wokondwera kwambiri za izo. Ine—ine nthawizonse ndimafuna kudziwa pamene ine

ndalakwitsa, chifukwa Mulungu amadziwa zimenezo; ine—ine sindimafuna kumalakwitsa.” Ine ndinati, “Chabwino, ngati ine ndikulakwitsa, ine ndithudi ndimafuna kuti ndidziwe zimenezo, m’bale. Zikomo inu.”

Iye anati, “Inu mumangokhalira kuwatamandira anthu achipentekoste amenewo.”

Ine ndinati, “Eya!”

Iye anati, “Iwo anapanga kulakwitsa koipitsitsa komwe iwo anayamba apangapo, pamene iwo anagulitsa malo awo.” Anati, “Pamene chisautso chinayamba, iwo analibe ngakhale nyumba yoti angapiteko. Iwo analibe malo oti apiteko, ndipo iwo ankangoyendayenda.”

Ine ndinati, “Zinali ndendende basi chifuniro cha Mulungu.”

Iye anati, “Chifukwa chiyani?”

²³³ Ine ndinati, “Ngati iwo akanakhala ndi nyumba iwo akanamabwerera, koma iwo amayenera kuchoka apa nkupita uko, kumafalitsa uthenga, konsekonse, kuti Mzimu Woyera wabwera. Musandiuze ine kuti Mulungu amalakwitsa. Iye samalakwitsa konse. Iye amadziwa momwe angachitire izo. Iwo amagulitsa akatundu awo ndipo amakhala oyendayenda, akufalitsa uthenga konsekonse.” Ndipo anati, “Uthengawo unafalikira ku dziko lonse lodziwika nthawi imeneyo, ndi oyendayenda awo omwe anasiya zonse kuti adzakhale ndi Mzimu Woyera.” Anthuwo sanali mu chipembedzo. Mukuona?

²³⁴ Tsopano, kumbukirani, chipembedzo ndi chimene Mulungu akuchiyitana, “Chitabaidwira mu chiphunzitso cha Balamu.” Chabwino, ndiye, pamene iye sakanakhoza kuwabweretsa iwo mu chipembedzo ichi, inu mukudziwa zomwe Balamu anachita? Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano, ife tikuyandikira koti titseke. Tsopano zomwe Balamu anachita, iye anachita chinthu chomwecho chimene iwo anachita kuno ku Nicene Council. Ndi chifukwa chake Iye anati, “Inu muli nacho chiphunzitso cha Balamu ndi Achinikolai amenewo.”

²³⁵ Tsopano, Achinikolai anali anthu omwe anatuluka ndipo ankafuna kupanga mabungwe ndi—ndi zina zotero. Zimene, potsiriza...Ndi angati akudziwa kuti izo ndi Choonadi pamene ine ndikuti, “bungwe”? Ndizo ndendende Choonadi cha Mulungu. Ndipo pomaliza anapanga bungwe lalikulu kwambiri padziko lapansi. Ndipo kodi iwo analipanga chiyani ilo? Katolika. Ndipo kodi mawu akuti *katolika* amatanthauza chiyani? “Konsekonse.” Bungwe, la padziko lonse, bungwe, “Zinthu zing’onozing’ono izi ziyenera kubwera mu mpingo umodzi.” Tsopano, ngati inu mungazindikire. Oh, ine...inu muzingopitirirabe kumapita.

²³⁶ Taonani! Kodi Babulo anali chiyani? Ndani anayambitsa Babulo? Nimrodi. Kodi iye anachita chiyani? Iye anapanga

nsanja imodzi yaikulu mu mzinda wawukulu, ndipo anapangitsa mizinda ina yonse kumapereka msonkho kwa mzinda uwu. Bungwe! Ndiwo maziko ake. Ndithudi. Anabwera komwe kuno mu m'badwo wa mpingo ndipo anadzapanganso bungwe, ndipo anabweretsa mafuko onsewo mmenemo. Ndipo pomwe apa ilo linati, "Hule amene anapangitsa mafuko onse kumwa vinyo wa ziwerewere zake." Chigololo chake chimene iye anali kuchita, kumadzinenera kuti ndi "Mkhristu" ndi kumapereka zinthu zonga zimenezo: katekisiru, mabukhu a mapemphero, ndi china chirichonse. Ndipo Achiprotestanti anadzabwerapo, chinthu chomwecho, basi kumangotsatira mmapazi ake.

²³⁷ Chabwino, tiyeni tipite patsogolo pang'ono tsopano. Chabwino. Chabwino. Iye ananena tsopano, kuti, "Izi zinali ziphunzitso za Balamu."

²³⁸ Tsopano, kodi Balamu anachita chiyani pamene iye anazindikira kuti iye sangakhoze—kuti iye sangakhoze kutemberera Israeli? Iye anamuuza Balaki kuti lingakhale lingaliro labwino, ndiye, kuti awaitane anthuwa ku phwando la mulungu. Iwo anali ndi—iwo anali ndi—ndi chikondwerero chachikulu kumtunda uko, iwo anali. . . kumene iwo anali oti akakhale. Ndipo iwo. . . Phwandolo linkatchedwa "Phwando la Baala-p-i-y-o, Baala-piyo." Ine ndikuganiza p- . . . piyo, Baala-piyo. Ilo linali phwa—phwando, la kupembedza.

²³⁹ Ndipo Balamu anati, "Tsopano, ine ndikukuuzani inu, Balaki, ine ndikupatsani inu lingaliro labwino. Ngati inu mungatero. . . ngati inu. . . Mulungu sadzawatemberera iwo, ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo, chotero ine ndikuuuzani inu zomwe ife titachite. Ife sitingathe kuwachotsa iwo; koma ngati inu mutangowaitanira iwo kuno, inu mudzachikokera chinthu chonsecho kumbali yanu."

²⁴⁰ Mwaona, ndendende, ndendende zomwe Konstantine anachita. Mwangwiro! Ndi chifukwa chake "chiphunzitso cha Balamu."

²⁴¹ Kodi iwo anachita chiyani? Iwo ndiye. . . Chiphunzitso cha Balaki chinatsikira pakati pa Israeli. Ndipo iwo anawaitanira a Israeli onse ku phwando lalikulu ili, kupambana kwakukulu komwe iwo anali nako. Oh, phwando lina lalikulu, chiphokoso cha chinthu kumtunda uko iwo anali nacho. Ndipo pamene iwo anakafika kumeneko, bwanji, anthu Achiisraeli awa anayamba kuwawona akazi okongola, ovala mwachigololo achi Moabu awa. Inde, sanali monga atsikana awo wamba kumeneko. "Oh, iwo ankawoneka okongola kwambiri. Mai! Momwe iwo anapangidwira ndipo, oh, momwe iwo amakhoza kudziwonetsera okha." Ndipo iwo anagwera izo, ndipo anayamba kuchita chigololo. Ndipo Balamu ankadziwa ngati Mulungu sangawatemberere iwo, iye adzawatengera iwo kumbali iyi ya chipembedzo ndi kupangitsa mkwiyo wa

Mulungu kuti uwaphe iwo mulimonse; kumulola Mulungu awaphe iwo Iyemwini, ngati iye angakhoze konse kuwachotsa iwo mu njira ya Choonadi.

²⁴² Ndipo mwamsanga inu mukangotuluka ndi kujowina tchalitchi mmalo molandira ubatizo wa Mzimu Woyera, inu mwafa! (Osati za inu, koma *apa*, ine ndikulola kuti izo zilowerere kwakanthawi pang'ono.) Wafa! “Inu muli nalo dzina,” anatero kwa Lutera apa, za M’badwo wa Sarde. Mawu oti *Sarde* amatanthauza “wakufa.” “Iwe uli nalo dzina kuti ndiwe wamoyo, koma ndiwe wakufa!” Ndizo zomwe Mulungu ananena. Eya. Mukuona?

²⁴³ Ndipo pamene iwo anali atachita ziwerewere zauzimu kumtunda uko, mpingo unakwatira kuchokera ku ubatizo wa Mzimu Woyera kupita ku chipembedzo, iwo anakhala akufa. Ndi zimenezotu. Ndizo zomwe Baibulo linanena, ndi zomwe Mulungu ananena, poyankhula ndi mipingo.

²⁴⁴ Tsopano ine ndikufuna kuti ndingowerenga chinachake apa kwa inu, kuti ine . . .

²⁴⁵ Ndipo Mulungu, kodi Iye anachita chiyani? Ndipo tsopano pamene iwo anachita chinthu choyipa ichi, ndipo iwo anali mu chigololo, Mulungu anapha forte thuu sauzande a iwo pa nthawi imodzi; forte-thuu sauzande, chifukwa chochita chigololo. Ndipo kodi izo zikuyankhula za chiyani apa mu mpingo? Chigololo chاوزimu, chomwe inu mumadzinenera kuti ndinu “Mkhristu” ndipo mukukhalabe monga dziko. Oh, m’bale, landirani inu Mzimu Woyera! Chokaniko ku tizikhulupiriro takale iti ndi zinthu zomwe inu . . . izo ndi zakufa; kubwereza Kachikhulupiriro ka Atumwi, kapena mtundu wina wa kachikhulupiriro, ndi kunena mapemphero angapo olembedwa kuchokera mu bukhu la pemphero, kapena chinachake chonga izo. Yesu sanawauze konse anthu Ake kuti adzinena pemphero, Iye anati, “Pempherani!” Pempherani! Chabwino.

²⁴⁶ Tsopano, phwando la Konstantine, chimodzimodzi monga la Balamu. Tsopano penyani. Monga phwando lachikunja la Balamu, Konstantine anali ndi phwando lachikunja. Chabwino. Pergamo anaitanidwa. Ndipo zindikirani tsopano izi . . .

²⁴⁷ Ine ndiri ndi chinachake ndalembe apa, ine ndichisiya icho chokha pakadali pano. Chabwino. Chabwino. Ine ndimangoyesera kuti ndigwire cholemba ichi apa cha . . . chinachake chimene ine ndinalembe.

²⁴⁸ Pergamo anaitanidwa. Chabwino, iwo anayitanidwa kuphwando pambuyo pa Nicene Council. Iwo anaitanidwira ku phwando la *Winter Solstice*; chimene chimatanthauza, “dzuwa, kupembedza kwa dzuwa,” amene anali mulungu wachikunja; zomwe zinkachitika pa Disembala 21, tsiku lalifupi kwambiri mu chaka. Ndi zaka . . . Nthawi yomweyo simasinth

mpaka Disembala 25. Achikunja onse amakondwerera ilo, tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa. Tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa linali tsiku lalifupi kwambiri mchaka, Disembala 21. Ndipo kenako aliyense amene anawerengapo mbiriyakale ya mipingo akudziwa kuti achikunja ankapembedza pa tsiku limenelo. Icho chinali chikondwerero.

²⁴⁹ Chabwino, Achiroma anali ndi... iwo anali ndi masewero akuluakulu, masewero Achiroma. Ndi angati anaziwonapo izi kuno, chirichonse chomwe icho chinali, kuno osati kale litali, iwo anali nazo uko? Ben Hur! Mukuona? Tsopano, masewera Achiroma; ndi zomwe Aroma anali nazo pa tsiku la dzuwalo, pokumbukira tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa. Mukuona?

²⁵⁰ Ndipo tsopano... ndipo iwo anakonza phwando lalikulu kumeneko ndipo anawaitanira Anikolai kuti abwere. Oh! Kodi izo si zangwiro? “Chiphunzitso cha Balaamu chimene inu muli nacho mwa inu.” Mwawona, kuwauza a Pergamo zomwe iwo anali nazo, mafuko aakulu. Pamenepo iwo ankaganiza kuti... Anikolai awa ankaganiza, “Chabwino, tsopano, zimenezo ndi zabwino. Phwando lalikulu ili limakondwereredwa chaka chirichonse? Inde.” Chotero ndiye ndi kuitanidwa kwa—kwa—kwa wotchedwa bishopu wamkulu, kapena chirichonse chomwe iye anali nthawi imeneyo, ndi chirichonse, iwo anachitenga kuti chikhale chinthu chomapitirira: kubweretsamo ziwerewere, kubweretsamo chigololo, kupanga mpingo wa Katolika; chimene chiri chipembedzo chirichonse cha Chiprotestanti membala wa izo, bungwe. Mulungu alibe bungwe, ndipo amadana nalo dzina lake kumene la ilo. Baibulo linanena chomwecho.

²⁵¹ Ndipo pamene iwo anachita zimenezo, chinachitika ndi chiyani? Iwo—iwo ananena tsopano... Iwo amayenera kukhala ndi mawonekedwe auzimu, chotero iwo anasinthana (Ambuye Yesu) M-w-a-n-a wa tsiku lobadwa la Mulungu kuyambira Epulo (Chimene masikolala onse abwino amadziwa, ndi aliyense wokhala ndi mavumbulutso auzimu, kuti Iye anabadwa mu nthawi ya chirengedwe monga pamene nkhosa ndi china chirichonse zimabadwa: mu Epulo.) kumbuyo mpaka tsiku la 25 Disembala. Ndipo akupembedzabe Khrisimasi, tsopano ndi Santa Claus. Ndipo chiyani... Oh, chifundo. Mukuona? Zikondwerero zochulukirapo zinawonjezeredwa kwa izo. Basi ndizo zonse. Ndi zimenezotu, oitanidwa, Balamu. “Inu muli nacho chiphunzitso cha Balamu pakati panu.” Ndi zimenezo. (O Mulungu, ingowululani izo, Atate.) Mukuona? Tsiku lobadwa kuyambira Epulo mpaka... .

²⁵² Tsopano, azambiriyakale amanena kuti “Umboni wonse wakuti Yesu anabadwa mmwezi wa Epulo pamene moyo wina wonse umatulukira.” Koma iwo azisintha izo kubwerera ku tsiku la 25 Disembala, patatha masiku asanu (mukuona?) kutsatira mulungu wachikunja, kuti akhoze kuyika miyambo yawo pamodzi: chikunja ndi Chikhristu. Ndipo Chikatolika

sikanthu mdziko koma gulu la zikhulupiriro zamizimu ndi zotayika za Chikhristu zitaikidwa pamodzi. Uko nkulondola. Izo nzoona. Ndipo Achiprotestanti omwe analumphira kwa icho ali ndendende basi mwana wamkazi wa mayi wachiwerewere. Ndizo ndendende.

²⁵³ Tsopano, Mulungu atithandize ife tikhale otsutsa enieni motsutsana ndi chirichonse chomwe sichiri chaumulungu. Mukuona? Oh!

²⁵⁴ Ndipo kuti mugwiritse ntchito zauzimu, kodi inu mukudziwa zomwe bishopuyo ananena? Bishopu anati, “Ife tiri ndi ululu wochita izi chifukwa iye ndi ‘Dzuwa la chirungamo.’” Hmm! Oh, iwo amapeza potseguka, monga iwo amachitira pa “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera;” Mateyu 28:19, mtundu womwewo, ndendende. Ndithudi, iwo ali ndi potseguka, iwo ayenera kukhala ndi mtundu wina wa machitidwe auzimu, inu mukuwona. Koma izo sizitero . . .

²⁵⁵ Baibulo linati, “Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatatu mulole mawu aliwonse akhale okhazikika.” Mulungu ananena pa zimenezo, Iye akuzinena izo katatu. Ngati Mulungu angatenge kutsimikizira chinachake, Iye anamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane; chirichonse chomwe Iye anachita, Iye anali ndi mboni ziwiri kapena zitatatu kuti atsimikizire zonse zomwe Iye ankachita, njira yonse kudutsa Lemba. Uko nkulondola.

²⁵⁶ Koma, inu mukuwona, tinthu tating’ono timeneto timayenera kubwera kumeneko kuti iwo adzatenge zimenezo kuti zidzakhale chimenecho. Mulungu anazidziwa izo asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Pamenepo iwo anazipeza izo, kamvetedwe kauzimu, “Chifukwa iye ndi M-w-a-n-a wa Mulungu, ife tingotenga tsiku lobadwa lachikunja la d-z-u-w-a ndi kulipanga ilo kukhala tsiku lobadwa la M-w-a-n-a, ndipo chifukwa iye ndi ‘Dzuwa la chirungamo.’” Hmm! Hmm! Inu mukudziwa, Achiprotestanti amagwerabe pa izo, chinachake chonga izo. Ndithudi, iwo angatero, amazichotsa izo nthawi yomweyo kuchokera ku Lemba kupita nazo kwinakwakenso. Oh, mai! Ine . . . Lolani—tiyeni tingoyima kwa miniti. Chabwino.

²⁵⁷ Apa pali chinthu chimodzi chaching’ono chomwe ine ndikufuna nditenge. Tiyeni titenge chomaliza cha ndime iyi apa mwachangu. Kodi ife tingathe kuchita zimenezo? Eya. Chabwino, ine ndifulumira kwenikweni, mofulumira kwenikweni tsopano, ndipo inu mudzatero . . . ife tigunda mfundo zikuluzikuluzo za Iwo. Chabwino. Kodi ife tiri pati tsopano?

*Koma . . . ndiri nazo zinthu pang’ono . . . ine ndiri . . .
motsutsana nawe, . . . Balamu, . . .*

Uko nkulondola, ine ndamvetsa zimenezo.

*Chotero uli nachonso . . . chiphunzitso cha
Chinikolai . . .*

Lapa; . . . apo ayi Ine . . . ndibwera . . . mwamsanga, ndipo . . . ndidzalimbana nawe ndi lupanga la pa kamwa panga.

Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu anena kwa mipingo; . . .

²⁵⁸ Mai! Apa pamene Konstantine anachita izi, izo zinali . . . Pamene iwo anakonza phwando lalikulu ili. Ine—ine basi . . . Ine ndinayamba kusunthira kutali ndi izo; Ine ndidikirira ndisanawerenge izo chifukwa Mzimu Woyera ukumasunthirabe mmbuyo, ndi chifukwa chake ndinachita zomwe ndinachita nthawi ija; anati, “Usazibwezere mmbuyo zimenezo.” Mwaona? Apa izo zikubwera! Uh-huh, uh-huh, uh-huh. Chabwino. Chifukwa chake . . .

²⁵⁹ Pamene iwo anakonza chinthu chachikulu ichi, (ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chimene chinachitika kuchitira kuti inu mumvetsetse.) kumeneko kunali kubadwa kwa zaka zikwi za mtsogolo. Chifukwa mpingo unali utalemera; iwo unali wolemera momwe iwo ukanathera. Ndipo kodi iwo unali chiyani? Wamphamvu. Iwo unali pamwamba pa boma; boma ndi mpingo zinali pamodzi.

²⁶⁰ Tsopano, Mulungu ali ndi ufumu? Ndipo kodi Yesu sananene kuti iwo . . . Uliwonse wa mafuko awa unali wake, anamuza Yesu chomwecho, anamuwonetsa Iye maufumu apa dziko lapansi, anati, “Onsewo ndi anga. Ine ndimachita nawo iwo chirichonse chomwe ine ndikufuna kuchita.” Ndipo kenako nkulumikizitsa Mulungu ndi mdierekezi pamodzi? Oh, inu simungakhoze kuchita zimenezo! Ndithudi, inu simungakhoze. Ndi chifukwa chake boma limachita bungwe. Mulungu siali, mabungwe awa. Ndithudi ayi, inu simungakhoze kuchita zimenezo.

²⁶¹ Koma iwo anali nazo izo pamenepo, iwo anali ndi mpingo wawo wotchedwa Chikhristu; iwo anali nawo iwo utayanjana ndi fuko, mfumu yonse ya Roma, zonse za izo. Bishopu wamkulu kumtunda uko wa zonse za izo, yemwe anali Boni- . . . Patapita kanthawi iwo anadzamutcha iye papa, koma iye anali—iye anali bishopu nthawi imenayo. Ndipo Boniface III anali iye amene anadzakhala papa woyamba.

²⁶² Ndiye ife tikudzapeza apa kuti iye anadzakhazikitsa kumeneko ngatidi papa wa pamwamba . . . Mulungu amene iwo anali naye, mmawonekedwe aumunthu. Iwo anali nalo guwa lalikulu. Iwo anali ndi chuma chambiri. Iwo anali nawo maguwa aakulu, amphamvu, okutidwa-nsangalabwi, ndi okongoletsedwa ndi miyala yodula, ndi zina zotero, paliponse pa izo. Ndipo iwo anali ndi matchalitchi akuluakulu. Iwo anali kulamulira boma. Ndipo inu mukudziwa chiyani? Mawu anatuluka kuti “zimenezo zinali Zakachikwi,” kukhala malonjezo onse a kwa Ayuda osauka awo, kuti, “Mulungu

anali atawasiya iwo” (zomwe Iye anati Iye sangathe kudzachita izo), ndipo anayesera kuti abweretsemo Zakachikwi kusanafike kudza kwa Ambuye Yesu. Pamene Yesu adzabwere ndi pamene Zakachikwi zidzayambike.

²⁶³ Ndiwo malo obadwira a zakachikwi zamtsogolo. Ndipo ndi chifukwa chake Akatolika samaphunzitsa kubwera kwa Yesu, kufikira lero. “Zonsezo ziri mu mpingo. Zakachikwi ndi izi. Mpingo uli nazo zonse. Izi ndi zimenezo.” Mwaona, zakachikwi-zamtsogolo (Oh, mai!) popanda kubweranso kwa Yesu Khristu. Izi zinakhalapo mpaka pakuphedwa kwa Konstantine komwe kunadzachitika pakati pa 312 ndi—ndi...A.D. 312 ndi 606. Kenako Boniface III anadzakhala bishopo wapadziko lonse kapena papa woyang’anira mpingo wonse wapadziko lonse.

²⁶⁴ Ine ndikukhulupirira kuti timalidzitsa ndime iyi, ndipo kenako ine ndidzakhala nayo iyo. Mulungu alemekezeke. Mukuona? Tsopano, ine ndinangoimikira kwa miniti chabe. Ndime ya 17:

Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu—Mzimu akunena kwa mipingo; Kwa iye amene alakika ine ndidzampatsa kuti adzadye... mana obisika, ndipo ndidzampatsa iye mwala woyera, ndi mmwalamo dzina latsopano lolembedwa, limene munthu wina aliyense salidziwa kupatula iye amene alilandira ilo.

²⁶⁵ Kodi inu mungafune kuti mudikire mpaka mawa usiku, kapena mukhale nalo ilo tsopano? [Osonkhana akuyankha, “Tsopano!”—Mkonzi]. Chabwino.

²⁶⁶ Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu muwalole anthu kuti amvetse tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti iwo akakhoze kumvetsetsa kulikonseko (ndi kumene matepi adzapite), kuti iwo akakhoze kudziwa kuti ine—ine ndikunena izi chifukwa Iko—Iko ndi Kutanthauzira Kwaumulungu kumene Inu mwandipatsa ine. Amenii.

...iye amene alakika...

²⁶⁷ Chinthu choyambirira chimene ine ndikufuna kuti inu mukumbukire: kuti uliwonse wa mauthenga awa sanalunjikidwe kwa mpingo, koma kwa mngelo wa mpingo. Tayang’anani mmbuyo kuno, woyamba uwo, mpingo wa Efe...Kwa mpingo...Kwa...

Kwa mngelo wa mpingo wa ku Efeso... (Nkulondola uko?)

²⁶⁸ Chabwino, m’badwo wa mpingo wotsatira, ndime ya 8:

...kwa mngelo wa mpingo wa Smurna...

²⁶⁹ Chabwino, ndipo ndime ya 12:

...kwa *mngelo wa mpingo wa Pergamo*...
(Nkulondola uko?)

²⁷⁰ Uthenga ukulembedwera kwa mtsogoleri wa mpingo. Mulungu amuthandize munthu ameneyo yemwe apite kutali ndi Uthenga umenewo! Koma Iwo umapatsidwa kwa mngelo, ndipo mngeloyo amakhala mdzanja Lake pansi pa ulamuliro Wake Womwe, kuwupatsa iwo mphamvu zopambana kuchokera kwa Iye, kuchokera mdzanja Lake lamanja. Iwo amakhala mdzanja Lake lamanja, ndiye kuti, amakhala mu mphamvu yapamwamba pamene iwo ali padziko lapansi pano; chifukwa iwo amakhala Kuwala kochokera kwa Iye, akupereka Kuwala kwa m'badwo wa mpingo umenewo. Mukuona? “Kwa *mngelo wa mpingo*.” Imalembedwera kwa *nyenyezi* (ya m'badwo) imene ili ndi udindo. Mngelo wa mpingo amakhala woyankhira ngati iye salalikira Mawu. Uko nkulondola. Ndipo mngelo ameneyo adzayenera kudzayankhira pa chiweruzo.

²⁷¹ Ndi angati akukumbukira masomphenya kuno osati kale kwambiri okhudza... Yang'anani apa. Pamene ine ndinali—pamene ine ndinali nditagona pa kama, ndipo Mzimu Woyera unabwera; ndipo ine ndimayang'ana mmbuyo, mkazi wanga ali pamene. Ndipo ine ndinali nditagona pamene, ndipo ndinadzapita mpaka mu Kukhalapo pamene, ndipo ine ndinawawona anthu onse amenewo. Ndipo inu mukukumbukira ine ndikukuuzani zimenezo? Nonse a inu mukutero. Mukuona?

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kodi iwo ali...?”

Iye anati, “Iwo ndi ako.”

Ndipo ine ndinati, “Onsewa ndi ma Branham?”

Iye anati, “Ayi.” Panali mamiliyoni a iwo. Iye anati, “Amenewo ndi owatembenuza ako.”

Ndipo ine ndinati, “Otembenuka?”

²⁷² “Tamuwona mkazi uyo yemwe iwe umamuyamikirayo, pamene, wachichepere ndi wokongola,” anati, “iye anali atapitirira zaka nainte pamene iwe unamutsogolera iye kwa Khristu.”

Ndipo ine ndinati, “Oh!” ine ndinati, “Ndiye ine ndimachita mantha ndi izi?”

Ndipo iye anati, “Ife tikuyembekezera kuno kudza kwa Ambuye.”

Ine ndinati, “Ine ndikufuna kumuwona Iye.”

²⁷³ Anati, “Iwe sungathe kumuwona Iye tsopano, koma” anati, “posachedwa Iye adzabwera. Ife tikumuyembekezera Iye, koma pamene Iye adzabwera, Iye adzabwera kwa iwe poyamba. Ndipo inu udzaweruzidwa molingana ndi Uthenga umene iwe unalalikira, ndipo ife tidzakhala anthu ako.”

“Chabwino,” ine ndinati, “inu mukutanthauza kuti ndine woyankhira wa onsewa?”

“Tonse a ife!”

Ine ndinati, “Chabwino, kodi aliyensenso. . .?”

Iye anati, “Iwe unabadwa mtsogoleri.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kodi aliyense adzakhala wodzayankhira?”

Iye anati, “Mtsogoleri aliyense.”

Ine ndinati, “Nanga bwanji Paulo Woyera?”

Anati, “Iye adzakhala wodzayankhira m’badwo *wake*.”

“Chabwino,” ine ndinati, “Ine ndinalalikira Uthenga womwewo iye anachita.”

Ndipo mamiliyoni a maliwu anamveka, anati, “Ife tikupumula pa zimenezo!” [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Mukuona? Ndi zimenezotu, “tikupumula.”

²⁷⁴ Chotero *mngelo* wa Mulungu, mtumiki kwa mpingo, amakhala ndi udindo ngati iye sakulalikira Mawu. Chabwino.

²⁷⁵ “Mana obisika.” Tiyeni tipereke kutanthauzira momwe ife tingathere. Kodi “mana obisika” amaimira chiyani? Mana obisika amakhala mana omwe amasungidwa pamalopo. . . kapena mkate wopanda chotupitsa, mu Baibulo, umenewo umakhala wa wansembe yekha. Ndi angati akudziwa zimenezo pano? Mukuona? Tsopano, iwo sumakhala wa. . . Iwo amakhala ndi mkate wa osonkhana, koma pamakhala mkate wapadera wa wansembe. Nkulondola uko?

²⁷⁶ Uwu umakhala mkate wapadera, mkate wapadera, manna *obisika*. Ndi chiyani chimenecho? Manna athu ndi ndani? Khristu. Chabwino, Yohane Woyera, mutu wa 6, ndime 48 mpaka ya 50, ngati inu mukulemba zimenezo. Yesu anati Iye anali “Mkate wa Moyo umene unabwera kuchokera kwa Mulungu Kumwamba,” Manna.

²⁷⁷ Chabwino, kodi ndi chiyani “manna obisika”? Manna omwe samaperekedwa kwa osonkhana onse. Vumbulutso limatsanuliridwa pa mngelo wa mpingo, vumbulutso la Mawu. Mukuona? Vumbulutso la Mawu limaperekedwa kwa mngelo wa m’badwo umenewo, pakuti izo zimabisika kulikonseko, ndipo zimawululidwanso (manna obisika) kwa. . . Iyo imalembedwera kwa *mngelo* wa mpingo. Mukuona? Inu mukumvetsa zimenezo? Ilo limakhala vumbulutso lokulirapo pang’ono la chimene Khristu ali, mwinamwake kuyitana kwapamwamba pang’ono.

²⁷⁸ Ndikudabwa ngati Luther anazindikira zimenezo? Ndikudabwa ngati Wesley anatero mmasiku ake? Oh! Ndikudabwa ngati Martin Woyera anazindikira izo? Ireniasi? Tsopano, inu mukudziwa, mpingo sunawavomereze konse amuna amenewo, iwo sanali oyera kwa iwo; koma iwo ndi

omwe anali ndi zizindikiro zikuwatsatira. Iwo anatenga awo—mabishopu awo omwe, ndi zina zotero, kuti avomereze.

279 Bwanji, kuno osati kale litali, mkazi anapita kukatenga *Life of Saint Martin* mu sitolo ya mabuku a Chingerezi. Ndipo pamene . . . Iye anati, “Martin Woyera.”

280 Ndipo munthuyo anatuluka panja, anati, “Iye siwodziwika kwambiri mu mbiriyakale, iye sanavomerezedwe.” Mukuona? Mpaka tsiku la lero; koma Mulungu ali nalo dzina lake, Mulungu amadziwa yemwe iye ali.

281 Mwaona, ndiko kusiyana kwake. Winawake amafuna dzina lake mu china chachikulu, koma anthu a Mulungu amafuna kupewa zinthu za mtundu umenewo. Iwo samafuna zinthu zazikuluzikulu kwambiri, ndi chinachake chachikulu kwambiri; iwo amafuna kukhala odzichepetsa, kudzichepetsa kumeneko. Njira—njira yopitira mmwamba ndi kutsika. “Iye amene amadzichepetsa yekha adzakwezedwa; iye amene amadzikuza yekha adzachepetsedwa.” Anadzichepetsa iyeyekha. Musamayesere kukhala chinachake chachikulu; mudziyesetsa kukhala chinachake chaching’ono, koma muzikhala chimene inu muli. Mukuona? Mudzikhala wamng’ono pamaso pa Mulungu, mudzikhala wamng’ono mmaso mwanu momwe, wina aliyense ali pamwamba panu. “Mulole iye amene ali wamkulu pakati panu akhale mtumiki wa onse.”

282 Ndani angakhale wamkulu kuposa Yesu Khristu amene anadzimanga mchiuno mwake ndikutsuka mapazi a ophunzira? Wosambitsa mapazi, Iye anadzakhala. Mulungu wa Kumwamba, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, kumatsuka mapazi akuda a asodzi (Oh!) okhala ndi manyowa ndi zinthu, ndi fumbi la mmisewu, komwe zovala zawo zimasesako izo, ndi kumawasambitsa iwo; Wosambitsa mapazi, chimene Iye anali. Ndiyeno ife timaganiza, “Ndife winawake. Ife tiyenera kukhala Doctor, Ph.D., *Wakuti-ndi-wakuti*.” Oh, mai! Ameneyo si Khristu. Zimenezo sizimawonetsera chikondi . . . Yesu Khristu wokonedwa. Iye anadzakhala Wantchito kwa onse. Uko nkulondola. Anati-phunzitsa ife chitsanzo kuti tizichitirana wina ndi mzake momwe Iye ankachitira kwa ife. Oh, awo—ameneyo ndi Mbuye wanga. Chomwe chimamupangitsa Iye kukhala wamkulu, chifukwa Iye anadzipanga Yekha kukhala wamng’ono. Mwaona, ndi chimene chinamupangitsa Iye kukhala wamkulu.

283 Ine ndakhalapo nawo mwayi wokumana ndi amuna ena otchuka mmoyo wanga, ndipo ndakhalapo nawo mwayi wokumana ndi amuna amene *amaganiza* iwo anali opambana. Munthu wamkulu weniweni amayesa kukupangitsa iwe kumaganiza kuti ndiwe wamkulu ndipo iye si kanthu. Mukuona? Kukumana ndi mafumu, ndi zina zotero, ndipo amuna omwe alidi amuna aakulu. Ndipo iwe ukakumana ndi Akhristu

okhazikika enieni, zovala zazigamba, ndi zinthu monga chomwecho. Ndipo ena a iwo amabwera paguwa ngati bokosi labandi ndipo kenako. . . Mukuona? Oh, mai! Chabwino, ndi patali kwambiri. . . Chabwino.

²⁸⁴ “Manna obisika,” chinachake *chapadera* pang’ono. Kodi *chapadera* ndi chiyani? Osati chinachake choti. . . Madalitso a Mzimu Woyera? Oh, ayi, izo ndi za osonkhana onse. Koma “mana obisika” anali vumbulutso lapadera chifukwa iye amayenera kukawaphunzitsa enawo. Mukuona? Limakhala chidziwitso pang’ono cha Lembu, kuti iye akakhoze kuwaphunzitsa ena. Iye akuyenera kukhala. Nkulondola uko? Inu simungakhale moyo wapamwamba kumuposa m’busa wanu. Inu muzikumbukira zimenezo, mwawona. Ndipo chotero. . . Chifukwa iye ndi m’busa amene amakudyetsani inu. Ngati iye ali m’busa, iye akuyenera kudziwa komwe kuli manna, kuti azidyetsa nkho—nkhosa. Nkulondola uko? Tsopano, lapadera pang’ono. Ndipo penyani izi miniti yokha, vumbulutso, manna obisika.

²⁸⁵ Tsopano, “Thanthwe loyera, adzakhala ndi thanthwe loyera.” Mngelo uyu adzakhala ndi mwala woyera. Limenelo ndi thanthwe, sichoncho? [M’bale akuti, “Chiyero.”—Mkonzi.] Ndipo a. . . Iye akunena zowona, “chiyero.”

²⁸⁶ Iye—Iye anakumana ndi munthu nthawi ina dzina lake Simoni, ndipo anamusintha dzina lake kukhala Thanthwe, “Petro.” Chifukwa chiyani? Iye anali nawo mafungulo. Nkulondola uko? Iye anamusintha dzina lake ndipo anamupanga iye thanthwe. Nkulondola uko? Petro anali ndi mafungulo chifukwa iye anali mmodzi amene anali ndi makiyi a Ufumu.

²⁸⁷ “Dzina latsopano, dzina latsopano lolembedwa mu thanthwe ili lomwe palibe amene akulidziwa koma iye yekha.” Iye amadziwa yemwe iye ali, koma iye sangathe kuwauza ena. Mukuona? Mukuona? Palibe amene akudziwa koma iyemwini. Mukuona? Petro ankadziwa kuti iye anali ndi makiyi, koma inu simunamumve iye akubwekerera za izo. Mukuona? Amuna awa omwe amabwekerera za zomwe iwo ali nthawi zambiri samakhala kanthu. Uh-huh, uh-huh. “Thanthwe loyera, ndipo mmenemo dzina latsopano.” Osati dzina lake lomwe, koma iye ndi wa winawake (Mukuona?) kuti iye yekha amadziwa; iye amene ali ndi thanthwelo, dzina. Mwaona, manna apadera akuti azidyetsa mpingo, kumbukirani.

²⁸⁸ Kumbukirani pamene Izi zinkachitika ku mpingo uwu, unali m’badwo womwewo (nthawi yomweyo imene Izi zimafulidwa) kuti Anikolai anali atadziyikira okha mkulu wa mpingo *wawo*, papa, ndipo anamupatsa iye guwa la mwala oyera pansu pake, pansu pa iye, guwa la nsangalabwi. Nkulondola uko? Ndipo litakulungidwa ndi zokongoletsera, ndi zinthu monga choncho, zomwe zinali zamtengo wapatali kwa *iye*.

289 Koma mngelo uyu wa Ambuye ankadziwa yemwe *iyе* anali, mwana wa Mulungu, kudzera—kudzera mu vumbulutso la Yesu Khristu.

290 Ndipo pamene—pamene Chinikolai chinadzakhazikitsa mtsogoleri *wawo* ndi kudzayika mwala wa nsangalabwi pa mapazi ake (Mukuona?), Mulungu anakhazikitsa mtsogoleri Wake wodzazidwa ndi Mzimu ku gulu Lake lodzazidwa—Mzimu; mngelo Wake; ndipo Iwo unaika pa iye chisindikizo cha dzina, koma iye sayenera kuwulula ilo. Iye ayenera kuti azisunge izo kwa iye yekha, mwawona. “Palibe munthu amene amadziwa koma iyemwini.”

291 “Manna obisika, mwala, dzina latsopano limene palibe munthu amene amalidziwa koma iye mwiniwake,” ndipo iyo imalembedwera kwa mngelo wa mpingowo. Ine ndikudabwa ngati Luther ankadziwa zimenezo? Ine ndikudabwa ngati Wesile ankadziwa zimenezo? Ine ndikudabwa ngati—ngati angelo ena aakuluwo?

292 Ndipo ine ndikudabwa lero, ngati mu. . . Akubwera mdziko posachedwapa, mngelo wamkulu wa Kuunika yemwe adzabwere kwa ife, amene adzatitsogolere ife kuti tituluke, Mzimu Woyera wamkulu, adzabwera mu mphanvu, ndipo adzatitsogolera ife kupita kwa Ambuye Yesu Khristu. Iye mwinamwake sadzazidziwa zimenezo, koma iye adzakhala pano ena a masiku amenewa. Iye adzapanga. . . Mulungu adzamupangitsa iye kuti adziwike. Iye sadzasowa kuti azidziwitse iyemwini, Mulungu adzamupangitsa iye kudziwika. Mulungu adzatsimikizira Ake Omwe. Ndizo zomwe Iye ananena pamene Yesu anali kuno ndipo iwo sanamudziwe Iye, mwawona. Iye anati, “Ngati ine sindichita ntchito za Atate Wanga, ndiye musandikhulupirire Ine; koma ngati ine ndikuchita ntchito za Atate Wanga, ndipo inu simukundikhulupirira Ine, ndiye mukhulupirire ntchitozo.” Nkulondola uko?

293 Oh, kodi Iye si wodabwitsa! Bukhu la Chivumbulutso. Tsopano, inu mukuwona kumene mipingo ili? Mukuwona momwe yawunjikirana uko? Mukuwona momwe mpingo unatulukira kunja kuno? Tsopano, *uno* ndi m'badwo umene ife tikubwerako mawa usiku, Ambuye akalola.

294 Tsopano, ine ndikupepesa kuti ine ndakusungani inu motalika kwambiri, koma ine—ine—ine ndikuyembekeza kuti inu—inu muphunzira chinachake. Ndi kulemba zolemba, kuti pamene. . . Ine ndiri ndi zina zowonjezera pano, pafupifupi masamba atatu kapena foro enanso, koma ine basi ndiribe nthawi yofikira kwa izo, ndipo, chifukwa kwayamba kuda, ndipo ndi pafupifupi maminiti seventini tsopano kuti ikwane. . . Koma ife tiziika izo mu bukhu, mulimonse, ndipo chotero tidza—ife tidza—tidzakhala nazo izo.

²⁹⁵ Tsopano, ndi angati amamukonda Iye ndi mtima wanu wonse? Ndi angati amamukhulupirira Iye ndi mtima wanu wonse? Oh! Tsopano, kodi inu mukuganiza kuti ine ndingaimo pano basi chifukwa choti sitiri mmabungwe— kuti ife sitiri mmabungwe ndipo tikhoza kunena zinthu zimenezo? Kodi inu mukumvetsetsa tsopano, abale, chifukwa chimene ine— ine (moyo wanga wonse) ndakhala ndikulimbana nacho chinthu chimenecho? Mwawona, Iwo unali Mzimu Woyera. Ine sindimatha kuzimvetsa izo ndekha, ine sindimazidziwa izo kufikira masiku angapo apitawo. Mukuona? Ine sindimadziwa chimene chinandipangitsa ine kuchita izo; Ine sindimadziwa chifukwa chimene ine ndimakhala ndikufuula motsutsana ndi akazi okhala molakwika, ndi zinthu; ine sindimadziwa izo, ine ndikudziwa tsopano. Mukuona?

²⁹⁶ Tsopano, Ambuye akudziwa kuti zinthu izi ndi zolakwika. Apa iwo akokedwa kumene mu mbiriyakale, ndipo abwera. . . Baibulo linati. . . Tsopano penyani apa, Baibulo linanena (zisanachitike) kuti zinthu izi zikanadzachitika. Tsopano, ife tikudziwa zimenezo, sichoncho ife? Ndiye ife tikutenga mbiriyakale ya m'badwo umenewo, ndi kuwona kuti izo zinachitika ndendende basi momwe Baibulo linanenera. Nkulondola uko? Chabwino, ndiye, pamene ife tidzafika kuno ku m'badwo *wathu* wa mpingo, ndi zomwe Iye akuneneratu za m'badwo *wathu* wa mpingo, izo zidzachitika ndendende basi momwe Mulungu ananenera kuti zikanadzachitikira. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Oh! Kodi inu simukufuna. . .

Oh, ndifuna kumuwona Iye, kuyang'ana pa nkhope Yake,
Kukaiimba za chisomo Chake chopulumutsa;
Pa misewu ya Ulemerero ndzakweza liwu
langa;
Zonse zatha, ndiri kwathu, ndikusangalala.

Oh, ine ndikufuna kumuwona Iye, kuwona. . .
(Ndi angati akufuna?)
Kukaiimba za chisomo Chake chopulumutsa;
Pa misewu ya Ulemerero ndzakweza liwu
langa;
Zonse zatha, ndiri kwathu, ndikusangalala.

Tsopano pamene mukugwirana chanza wina ndi mzake, kutsogolo, kumbuyo, ndi pozungulira, ndi Amethodisti onse, Abaptisti, Apresbateria, chirichonse chomwe chiri:

Pakuyenda mdzikoli, kuimba pamene
ndikupita,
Oh, kuloza miyoyo ku Kalvare (Osati mpingo,
Kalvare.), kudzera mu kuyenda kofiira,

Mivi yambiri yalasa moyo wanga, kuchokera
kunja, mkati;

Koma Ambuye wanga anditsogolera, kwa Iye
ndiyenera kumamatira.

Tiyeni tiimirire tsopano:

Oh, ndikufuna kumuwona Iye, kuyang'ana
nkhope Yake,

Kumeneko kuyimba kwanthawizonse . . .

Tiyeni tikweze manja athu mmwamba.

. . . chisomo chopulumutsa;

Pa misewu ya Ulemerero ndzakweza liwu
langa;

Zonse zatha, ndiri kwathu, ndikusangalala.

²⁹⁷ Oh, momwe ine ndikumukondera Iye! Momwe ine
ndimamukondera Iye! Wodabwitsa! Wodabwitsa!

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,
Wauphungu, Kalonga wa Mtendere, Iye ndiye
Mulungu Wamphamvu;

Oh, kundipulumutsa ine, kunditeteza ku
tchimo lonse ndi manyazi,

Wodabwitsa ndi Muomboli wanga,
litamandike Dzina Lake!

Poyamba ndinali nditataika, tsopano
ndapezeka, wopanda kutsutsika,

Yesu amapereka ufulu ndi chipulumutso
chathunthu;

Kundipulumutsa ndi kundisunga oh, ku
tchimo lonse ndi manyazi,

Wodabwitsa ali Muwomboli wanga,
litamandike Lake . . .

Aliyense, mokweza kwenikweni:

Wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,
Wauphungu, Kalonga Wamtendere, Iye ndiye
Mulungu Wamphamvu;

Oh, kundipulumutsa, kunditeteza ku tchimo
lonse ndi manyazi,

Wodabwitsa ndi Muomboli wanga,
litamandike Dzina Lake!

Oh, nzodabwitsa bwanji!

Oh, wodabwitsa, wodabwitsa, Yesu ali kwa ine,
Iye ndi Wauphungu, Kalonga wa Mtendere,
Mulungu Wamphamvuzonse ali Iye;

Iye akundipulumutsa, akunditeteza kwa
tchimo lonse ndi manyazi,

Wodabwitsa ndi Muomboli wanga,
litamandike Dzina Lake!

²⁹⁸ Tiyeni palimodzi tinene, “Lilemekezeke Dzina Lake!” [M’bale Branham ndi osonkhana akuyankhula mogwirizana—Mkonzi.]: “Lilemekezeke Dzina Lake!” Muwomboli Wanga! Kumbukirani mawa usiku, seveni koloko. Kufikira nthawi imeneyo, kufikira mutadzabwereranso, chitani izi:

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakhala chisangalalo, chitonthozo...
(Wokondwa kukuwonani pano abale,
Ambuye akudalitseni.)
...kulikonse iwe upita.

Dzina lofunika (Dzina Lofunika!), Oh ndi lokoma! (Oh ndi lokoma!)
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina Lofunika (Dzina Lofunika!), Oh ndi lokoma!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

²⁹⁹ Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu tsopano mu pemphero, kwa nyimbo yotsiriza, kapena, gawo lotsiriza:

Pa Dzina la Yesu kugwada,
Kugwa modzilambatitsa pa... (Ambuye Mulungu, achizeni awa, Ambuye, pamene ife...)... tidzamuveka Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.



M'BADWO WA MPINGO WA PERGAMO CHA60-1207
(The Pergamean Church Age)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu madzulo, Disembala 7, 1960, ku Branham Tabernacle ku Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org